***KAFUKUFUKU***

***WA***

***CHIPANGANO CHAKALE***

## HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a **Harvest International Institute** ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinasandulitsa anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

@Harvestime International Institute

# ZAMKATI MWA BUKULI

Kagwiritsidwe Ntchito Ka Bukuli……………………………………………………………….…..4
Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira Limodzi Pagulu………………………………………5
Mau Oyamba…………………………………………………………………………………....6
Zolinga za Maphunzirowa………………………………………………………….........7

### MAWU OYAMBA A BAIBULO

1. Mawu oyamba a Baibulo……………………………………………………………….8
2. Mabuku a Baibulo…………………………………………………………………..21
3. Ziyankhulo za Baibulo…………………………………………………………...…46
4. Kuonetsa Magawo…………………………………………...……………….…50

### CHIPANGANO CHAKALE

Mawu oyamba a Mabuku a Chilamulo…………………………………………………55

5. Genesis……………………………………………………………………….......56
6. Eksodo……………………………………………………………………….....62
7. Levitiko………………………………………………………………………….68
8. Numeri…………………………………………………………………...……....73
9. Deuteronomo……………………………………………………………………77

Mawu oyamba a Mabuku a Mbiri…………………………………………………...81

10. Yoswa……………………………………………………………………………82
11. Oweruza…………………………………………………………………………86
12. Rute………………………………………………………………………………92
13. I ndi II Samueli……………………………………………………………......96
14. I ndi II Mafumu…………………………………………………..…………..101
15. I ndi II Mbiri…………………………………………………………….....107
16. Ezara……………………………………………………………………………112
17. Nehemiya…………………………………………………….................116
18. Estere……………………………………………………………………………121

Mawu oyamba a Mabuku a Ndakatulo…………………………………………..126

19. Yobu……………………………………………………………………………....127
20. Masalmo…………………………………………………………………….......132

21. Miyambo…………………………………………………………………………..138
22. Mlaliki……………………………………………………………………..............142
23. Nyimbo ya Solomoni……………………………………………………………...146

Mawu oyamba a Mabuku a Uneneri………………………………………………..151

24. Yesaya…………………………………………………………………….….154
25. Yeremiya……………………………………………………………………..159
26. Maliro……………………………………………………………………...…163
27. Ezekieli……………………………………………………………......…….167
28. Danieli………………………………………………………………………..171
29. Hoseya………………………………………………………………………..176
30. Yoweli……………………………………………………………..……….181
31. Amosi………………………………………………………………………...186
32. Obadiya…………………………………………………………………………190
33. Yona………………………………………………………………………..…194
34. Mika………………………………………………………………………..…198
35. Nahumu………………………………………………………………………202
36. Habakuku……………………………………………………………..………206
37. Zefaniya…………………………………………………………………...……210
38. Hagai……………………………………………………………………...…....214
39. Zakariya…………………………………………………………...…………219
40. Malaki…………………………………………………………………….….224

Mayankho a mafunso odziyetsa nokha………………………………………………..228

## KAGWIRITSIDWE NTCHITO KA BUKULI

## KAKONZEDWE KA BUKULI

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

**Zolinga**: Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Welengani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

**Vesi Yotsogololera:** Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

**Zopezeka mu Magawo**: Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

**Mayeso Odziyesa Nokha:** Osathamangira kulememba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

**Zophunzira Zowonjezera:** Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mau Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

**Mayeso Omaliza:** ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

## ZOWELENGA ZINA ZOFUNIKA POPHUNZIRA PHUNZIROLI

Mudzafunikira Buku Lopatulika

## NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU

## MKUMANO WOYAMBA

**Kutsekulira:** Yamabani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

**Khazikitsani Ndondomeko Zapagulu:** Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene mudzikumana.

**Mayamiko ndi Matamando:** Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

**Gawani Mabuku Kwa Ophunzira:** Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

**Perekani Nchito Yoyamba**. Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene adziphunzitsidwa pa mkumano uli onse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

## MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO

**Kutsekulira:** Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina awophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a wophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

**Kukumbutsira**: Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

**Phunziro:** Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphunzira komanso mmene angagwiritsire ntchito zimene aphunzira pamoyo wawo ndi utumiki.

**Mayeso Odziyesa Nokha**: Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankha kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adzipezere okha mayankho.

**Mayeso omaliza:** Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphunzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina aliyense ali ndi buku laphunziroli.

## PHUNZIRO: KAFUKUFUKU WA BAIBULO

## MAU OYAMBA

Mau ambiri a mu Chipangano Chakale amene Ambuye adawalankhula munthawi ya utumiki wawo wa pansi pano anaonetsera kufunikira kwa chimene Malemba akufotokoza. Pachifukwa chokhachi chotsindika kufunikira kwa Mau a Mulungu kwa ophunzira ake, Harvestime International yabwera ndi phunziro lokuti, "Kafukufuku wa Baibulo," ngati dongosolo la maphunziro okonzekeretsa atumiki kuti akathe kufikira anthu amitundu yonse ndi Mau a Mulungu.

Gawo "Kafukufuku wa Baibulo" akuonetsera Baibulo ndi matanthauzidwe ake mu malembedwe osiyanasiyana. Akupereka chithunzithunzi cha mbiri ya Mbaibulo, malo ndi moyo wake mmene unalili munthawi imene kunali Baibulo. Komanso kawuniwuniyi akuphunzitsa magawo a maluso ndi magawo a mabuku onse a mmene mungaphunzirile Mau a Mulungu.

Nkhani zonse zimene zikupezeka Mbaibulo ndi zokhuza amene analemba, anthu amene amawalembera, cholinga chimene analembera buku, vesi lotsogolera, anthu amene akutchulidwa ndi magawo onse. Osaiwalanso Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku lililonse. Mmfundo zimenezi ndi zofunika kwambiri pa kukula kwa moyo wa Chikhristu ndi utumiki choncho mukuyenera kukhala gawo limodzi la zimenezi. Matchati, madera komanso nthawi ya zimene zinthuzi zamalembedwa zikupezekamo ndi cholinga chokhuthandizani kuti mupindule pa maphunziro anu.

Phunzirolo lagawidwa mmagawo awiri:

Gawo Loyamba: Ili likupereka chiyamba cha nkhani ndi magawo a mabuku onse a Mchipangano Chatsopano.

Gawo Lchiwiri: Ili likupereka magawo a mabuku onse a Mchipangano Chatsopano.

"Kafukufuku wa Baibulo" ndi phunziro limene limagwirizana ndi phunziro la "Njira zatsopano zophunzirira Baibulo" zimene zimaphunzitsa njira zambiri zophunzirira Baibulo. Maphunziro onsewa akonzedwa ndi cholinga chopereka mwayi wapaderadera wophunzira Mawu a Mulungu.

## ZOLINGA ZA PHUNZIROLI

**Pakutha pa phunziroli muyenera**:

- Kudziwa magawo onse akukuakulu a Mbaibulo.
- Kulongosola kusiyana pakati pa mtundu wa kalembedwe, matanthauzidwe ndi malembedwe a chidule cha Bailbulo.
- Kulongosola moyo wa tsiku ndi tsiku mu nthawi ya Mbaibulo.
- Kulemba chidule cha nthawi ya Mbaibulo.
- Kupanga ndi kutambasula magawo.
- Mu buku liliilonse Mbaibulo ayenera kutchula:
    - -Wolemba bukulo
    - -Amene amawalembera
    - -Cholinga chimene amalembera bukulo
    - -Vesi lotsogolera.
    - -Moyo ndi mfundo ya utumiki.

- Kupitiliza kuwerenga mawu a Mulungu ngakhale atamaliza phunziroli.

## GAWO LOYAMBA: MAWU OYAMBA M'BAIBULO

## CHAPUTALA CHOYAMBA

### KUYAMBA NDI BAIBULO

ZOLINGA:

Pakutha pa phunziroli muyenera:

- Kulemba vesi kuchokera pamtima.
- Kupereka tanthauzo la mau oti "Baibulo."
- Kupereka tanthauzo la mau oti "Malemba."
- Kulongosola chiyambi chake cha Baibulo.
- Kudziwa zolinga zazikulu za Baibulo.
- Kudziwa magawo awiri akulu a Baibulo ngati Chipangano Chakale ndi Chatsopano.
- Kutchula magawo anayi a mabuku a Chipangano Chakale.
- Kutchula magawo anayi a mabuku a Chipangano Chatsopano.
- Kulongosola tanthauzo la "umodzi ndi kuchuluka" kwa Baibulo.
- Kudziwa munthu amene amalandira mavumbulutso a Zipangano zonse za Baibulo.

**VESI LOTSOGOLERA:**

> **Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa chiphunzitso, chitsutsano, chikonzero, chilangizo cha m'chilungamo: kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kuchita ntchito iri yonse yabwino**
> **(II Timoteo 3:16-17).**

### MAWU OYAMBA

Ndime imeneyi ikuonetsera kuti Baibulo limene ndi Mau olembedwa a Mulungu yekhayo woona. Mawu okuti "Baibulo" akutanthauza kuti "mabuku." Choncho Baibulo ndi buku limodzi limene lili ndi mabuku okwanira 66.

Mawu okuti "Malemba" amaimiliranso Mau a Mulungu. Mawuwa amachokera ku mawu a chilatini amene amatanthauza kuti "zolemba." Pamene mawu oti "Lemba" akuyamba ndi chilembo chachikulu "L" zikutanthauza kuti zolemba zopatulika za Mulungu mmodzi woona. Mawu oti "Baibulo" sanagwiritsidwe ntchito Mbaibulo. Amenewa ndi mawu amene anthu anasankha pofuna kuti ayimilire Mau onse a Mulungu.

### CHIYAMBI CHAKE CHA BAIBULO

Baibulo ndi Mau Mulungu olembedwa. Anawuzira mawu mu Baibulo ndipo anagwiritsa ntchito anthu osiyanasiyana okwanira 40 kulemba Mau ake. Ndipo anthuwa analemba kwa zaka

zopitilira 1500. Ungwiro wa mgwirizano wa anthu olembawa unali wakuti onse amatsogoleredwa ndi wolemba mmodzi yekha amene ndi Mulungu.

Ena mwa olembawa analemba zonse zimene Mulungu adanena:

> **Tenga buku lampukutu, nulembe m'menemo mau onse ndanena kwa iwe akunenera Israyeli……Yeremiya 36:**2.

Pomwe olemba ena adalemba za zimene adakumana nazo ndi zimene Mulungu adawaululira zokhudza tsogolo:

> **Chifukwa chache lembera zimene unaziona, ndi zimene ziripo, ndi zimene zidzaoneka m'tsogolomo (Chibvumbulutso 1:19).**

Koma olemba onsewa analemba mochita kuuzilidwa ndi Mulungu kudzera mu uthenga wake wa kwa ife.

## CHOLINGA CHAKE BAIBULO

Baibulo lokha limatsindika za cholinga chake chachikulu:

> **Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa chiphunzitso, chitsutsano, chikonzero, chilangizo cha m'chilungamo:**
>
> **Kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kuchita ntchito iri yonse yabwino (II Timoteo 3:16-17).**

Malemba amagwira ntchito pophunzitsa chiphunzitso, kudzudzula, kukonza zolakwika ndi kuphunzitsa chilungamo. Amakuthandizani kuti mukhale oyenera ndi okonzeka kugwira ntchito ya Mulungu.

## MAGAWO AKULU AKULU A BAIBULO.

Baibulo linagawika mmagawo akulu awiri amene ndi Chipangano Chakale ndi Chipangano Chatsopano. Mawu oti “chipangano” amatanthauza pangano limene ndi mgwirizano. Chipangano Chakale chimakamba za pangano kapena mgwirizano woyambilira wa Mulungu ndi munthu. Pamene Chipangano Chatsopano chimakamba za pangano latsopano la Mulungu mwa Mwana wake Yesu Khristu.

Kodi nanga mutu waukulu wa mapangaano amenewa ndi otani? Mapangano onsewa amatsindika za kubwenzeretsa ubale wabwino pakati pa munthu wochimwa ndi Mulungu. Mulungu anapanga chilamulo chakuti tchimo likhoza kukhululukidwa kudzera mkukhetsedwa kwa mwazi:

**……. ndipo wopanda kukhetsa mwazi kulibe kumasuka (Ahebri 9:22).**

Mu pangano la Mulungu la Mchipangano Chakale linali lakuti mwazi wa nyama imene umaperekedwa nsembe ndi munthu umatha kukhululukira machimo ake. Ichi chinali chizindikiro cha nsembe ya mwazi wa Yesu Christ umene ndi pangano latsopano la Mulungu. Kudzera mu kubadwa, moyo, imfa ndi kuuka kwa Yesu, nsembe yotsiriza ya uchimo inaperekedwa:

> **Koma atafika Kristu, Mkuluwansembe wa zokoma zirinkudza, mwa chihema chachikuru ndi changwiro coposa, cosamangika ndi manja, ndiko kunena kuti, cosati ca cicilengedweci,**
>
> **Kapena mwa mwazi wa mbuzi ndi ana a ng'ombe, koma mwa mwazi wa iye yekha, analowa kamodzi ku malo opatulika, atalandirapo ciombolo cosatha.**
>
> **Pakuti ngati mwazi wa mbuzi ndi ng'ombe zamphongo, ndi makala a ng'ombe yamthandi owazawaza pa iwo odetsedwa, upatutsa kufikira ciyeretso ca thupi;**
>
> **Koposa kotani nanga mwazi wa Kristu amene anadzipereka yekha wopanda cirema kwa Mulungu mwa Mzimu wosatha, udzayeretsa cikumbu mtima canu kucisiyanitsa ndi nchito zakufa, kukatumikira Mulungu wamoyo?**
>
> **Ndipo mwa ici ali Nkhoswe ya cipangano catsopano, kotero kuti, popeza kudacitika imfa yakuombola zolakwa za pa cipangano coyamba, oitanidwawo akalandire lonjezano la zolowa zosatha (Ahebri 9:11-15).**

Zipangano zonse ziwiri ndi Mau Mulungu ndipo tiyenera kuwerenga zonse ndi cholinga chofuna kumvetsetsa uthenga wa Mulungu. Mawu oti chipangano cha "kale" ndi "tsopano" amagwiritsidwa ntchito pofuna kusiyanitsa pakati pa pangano la Mulungu ndi munthu Yesu Khristu asanafe ndi pamene atangofa. Choncho pokhala kuti ndi Chipangano "Chakale", sizikutanthauza kuti tisamachilabadire.

## MAGAWO ENA

Baibulo lagawidwabe ngati mabuku okwanira 66. Chipangano chakale chili ndi mabuku okwana 39, ndipo chatsopano chili ndi mabuku okwana 27. Ndipo buku lililonse lililonse lagawidwa mmachaputala ndi mmavesi. Ngakhala zonse zolembedwa ndi Mau a Mulungu, koma machaputala ndi mavesi anapanga ndi munthu, ndi cholinga choti zikhale zosavuta ndi kudziwa ndime zomwe zikufunika. Zikanakhala zovuta kupeza ndime ngati mabuku onse akanakhala ndime imodzi yaitali.

Chithunzi ichi ndi chitsanzo cha cha magawo a Baibulo:

BAIBULO

Chipangano Chakale Chipangano Chatsopano

Mabuku 39 Mabuku 27

## UMODZI WA M'BAIBULO

Tikamakamba za umodzi wa M'baibulo, timatanthauza zinthu ziwiri izi:

CHOYAMBA: BAIBULO NDI LIMODZI MOLINGANA NDI ZOMWE ZIKUPEZEKAMO

Ngakhale kuti Baibulo linalembedwa ndi antuu ambiri kwa zakanzo zochuluka, koma palibe kutsutsana. Wolemba mmodzi samatsutsana ndi wolemba wina.

Tikukamba za Baibulo limene lili ndi mazana a zolankhulidwa pa mitu yovuta. (Mutu wovuta ndi umene umabweretsa maganizo osiyana ukatchulidwa). Koma ndithu wolemba onse a Baibulo amalankhula pa zofanana pa mitu imeneyi ngakhale kuyambira m'buku la Genesis kufikira buku lomaliza la Chibvumbulutso. Izitu zinali zotheka chifukwa panali wolemba weniweni mmodzi: ndiye Mulungu. Anthu amene amalemba aja amalemba koma mosogozedwa ndi kuuzilidwa ndi Mulungu. Chifukwa cha ichi, zolembedwa za Mbaibulo ndo zogwirizana.

CHACHIWIRI: BAIBULO NDI LOGWIRIZANA PA MUTU:

Ena amaganiza kuti Baibulo ndi unyinji wa mabuku okwana 66 amene ndi osiyana mitu yake. Iwowa samamvetsa kuti Baibulo ndi logwirizana pa mutu waukulu. Kuchokera pachiyambi, Baibulo limaulula, cholinga cha Mulungu chapaderadera chimene chidule chake ndi ichi:

> **Anatizindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye;**
>
> **Kuti pa tinakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko.**
>
> **Mwa iye tinayesedwa colowa cace, popeza tinakonzekeratu monga mwa citsimikizo mtima ca iye wakucita zonse monga mwa uphungu wa cifuniro cace (Aefeso 1:9-11).**

Baibulo limaulula chinsinsi cha dongosolo la Mulungu limene limabweretsa pamodzi mutu wa Mbaibulo. Baibulo ndi chibvumbulutso cha Yesu Khristu ngati mpulumutsi wa mtundu wochimwa. Yesu analongosola kuti Chipangano Chakale chakhazikika pa Iye:

**Ndipo anati kwa iwo, Awa ndi mauwo ndinalankhula nanu, paja ndinakhala ndi inu, kuti ziyenera kukwanitsidwa zonse zolembedwa za Ine m'cilamulo ca Mose, ndi aneneri, ndi masalmo (Luka 24:44).**

Ndi mawu amenewa Yesu anapitiliza kunena kuti….

**... Ndipo anawatsegulira mitima yao, kuti adziwitse malembo (Luka 24:45).**

Kodi Yesu adawapatsa chani kuti amvetsetse malembo? Pa chifukwa chokhachi chakuti mutu wankhani umakamba za Iye:

**… Ndipo anati kwa iwo, Kotero kwalembedwa, kuti Kristu amve zowawa, nauke kwa akufa tsiku lacitatu;**

**ndi kuti kulalikidwe m'dzina lace kulapa ndi kukhululukidwa kwa macimo kwa mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu. Inu ndinu mboni za izi (Luka 24:46-48).**

Motero chipangano Chakale ndi Chatsopano chakhazikika pa nkhani ya Yesu. Chipangano Chakale chimatikonzekeretsa ife kudziwa za mmene nkhaniyi idzachitikira ndipo Chipangano Chatsopano chimafotokoza za mmene nkhaniyi inachitikira. Izi zimalumikizitsa Baibulo pa mutu umodzi. Anthu amene amayembekezera Yesu mu nthawi ya Chipangano Chakale anapulumutsidwa ku machimo awo kudzera mwa chikhulupiriro pa lonjezo la Mulungu. Aliyense amene amene ayang'ana mmbuyo atazindikira kuti zakwaniritsidwa mwa Yesu amapulumutsidwanso mwa chikhulupiriro: Kuti kudzera mwa chikhulupiriro zinachitika molingana ndi mmene Mulungu analonjezera.

## KUCHULIKA KWA BAIBULO

Tikamakamba za "kuchuluka" kwa Baibulo tikutanthauza kuti Baibulo lili ndi zinthu zambiri. Limaonetsa njira zosiyanasiyana zimene Mulungu anagwiritsa ntchito pochita ndi anthu ake amene amachitanso zinthu kwa Iye koma mosiyananso.

Baibulo linalembedwa mu nyengo zosiyanasiyana. Magawo ena amakamba za chimwemwe pomwe ena za chisoni. Ndipo Baibulo lili ndi mitundu yonse ya kalembedwe monga mbiri, ndakatulo, uneneri, makalata, zomvetsa chisoni kapena zosangalasa, mafanizo, zodabwitsa, nkhani za chikondi. Chifukwa cha kuchulukaku, Baibulo lagawidwanso mmagulu akuluakulu a mabuku.

## MAGAWO A CHIPANGANO CHAKALE

Mabuku a Chipangano Chakale agawidwa mmagulu okwana anayi: Chilamulo, Mbiri, Ndakatulo ndi Uneneri.

### MABUKU A CHILAMULO:

Pali mabuku asanu amene ndi a chilamulo. Mabukuwa ndi awa:

Genesis
Eksodo
Levitiko
Numeri
Deuteronomo

Mabuku amenewa amakamba za mmene Mulungu analengera munthu ndi dziko komanso muli mbiri ya munthu woyamba. Komanso amafotokoza za mmene Mulungu anasankhira mtundu wa Israyeli ngati anthu ake amene kudzera mwa iwo anaziulula yekha ku mafuko ena a dziko lapansi.

Mabuku amenewa amkambanso za malamulo a Mulungu. Makamaka gawo lodziwika bwino la Malamulo khumi a Mulungu (Eksodo 20:3-7), komanso za lamulo lalikulu loposa onse (Deuterenomo 6:5) ndiponso za lamulo lachiwiri lalikulu (Levitiko 19:18).

Tsekulani Baibulo lanu ndipo pezani mabulu a chilamulo mu Chipangano Chakale. Pezani mavesi atatu amene akutchulidwa mu ndime yotsatirayo ndipo awerengeni. Amenewa ndi zitsanzo za malamulo a Mulungu opezeka mmabukuwa.

**MABUKU A MBIRI:**

Mabukuwa alipo okwanira khumi ndi awiri mu Chipangano Chakale. Mayina awo ndi awa:

Yoswa
Oweruza
Rute
I ndi II Samueli
I ndi II Mafumu
I ndi II Mbiri
Ezara
Nehemiya
Estere

Pezani mabukuwa Mbaibulo lanu. Amapezeka kumapeto kwa mabuku a chilamulo. Mabuku a mbiri amafotokoza mbiri yonse ya zaka chikwi ya anthu a Mulungu, Israyeli. Mwachikhalidwe, samafotokonza chilichonse chimene chinachitika, koma amafokoza za nkhani zikuluzikulu ndi kuonetsa zotsatira za kumvera ndi kusamvera lamulo la Mulungu.

**MABUKU A NDAKATULO:**

Mabukuwa alipo okwana asanu okha. Ndipo mayina awo ndi awa:

Masalmo
Miyambo

Mlaliki
Nyimbo ya Solomoni

Awa ndi mabuku amene amakamba za kulambira kwa anthu a Mulungu, Israyeli. Ndipo amagwiritsidwabe ntchito lero pa kulabira kwa okhulupirira. Pitani pa Masalmo 23 ndipo werengani. Ichi ndi chitsanzo chitsanzo cha ndakatulo ya kulambira kokoma kumene kuli mmabukuwa.

**MABUKU A UNENERI:**
Mabuku a uneneri a Mchipangano Chatsopano agawidwa mmagulu awiri amene amatchedwa kuti aneneri a akulu ndi aneneri a ang'ono. Komatu izi sizimatanthauza kuti aneneri a akulu ndiwo amene ali ofunika kuposa a ang'ono. Akutchulidwa aneneri a akulu chifukwa mabuku awo ndi a atali koposa aneneri a ang'ono. Pali mabuku a aneneri okwana khumi asanu ndi awiri (17), ndipo mayina awo ndi awa:

**Aneneri a akulu:**
Yesaya
Yeremiya
Maliro
Ezekieli
Daniyeli

**Aneneri a ang'ono**

| | |
|---|---|
| Hoseya | Nahumu |
| Yoweli | Habakuku |
| Amosi | Zefaniya |
| Obadiya | Hagai |
| Yona | Zakaliya |
| Mika | Malaki |

Mabukuwa ali ndi uthenga wa uneneri ochokera kwa Mulungu, kupita kwa anthu ake, uthengawu ndi wokhuza zinthu za mtsogolo.
Ambiri mwa mauneneriwa akwaniritsidwa kale, koma ena akwaniritsidwa mtsogolo. Pezani mabuku a uneneriwa Mbaibulo lanu. Mabukuwa ndi omalizira mu Chipangano Chakale.

## MAGAWO A CHIPANGANO CHATSOPANO

Chipangano Chatsopano chagawidwanso mmagawo anayi monga: Mauthenga abwino, Mbiri, Makalata ndi Uneneri.

**MAUTHENGA ABWINO:**
Mauthenga abwinowa alipo okwana anayi. Mayina awo ndi awa:

Mateyu Marko Luka Yohane

Mabukuwa amakamba zambiri za moyo, imfa ndi chiukitso cha Yesu. Cholinga chawo ndiko kukutsogolerani kuti mukhulupirire kuti Iye ndi Khristu, Mwana wa Mulungu. Pezani mabuku a mauthenga abwino Mbaibulo lanu ndipo werengani Yohane 20:31 pamene amafotokozapo za cholingachi.

**BUKU LA MBIRI**

Buku la mbiri lilipo limodzi lokha mu Chipangano Chatsopano, ndipo limeneli ndi buku la Machitidwe. Bukuli limafotokoza za mmene mpingo unayambira ndi kukwaniritsidwa kwa kutuma kwakulu kwa Khristu kolalikira uthenga wabwino padziko lonse lapansi. Pezani bukuli Mbaibulo lanu.

**MAKALATA**

Pali makalata okwanira 21 mu Chipangano Chatsopano. Mayina awo ndi awa:

Aroma
I ndi II Akorinto
Agalatiya
Aefeso
Afilipi
Akolose
I ndi II Atesalonika
I ndi II Timoteo
Tito
Filemoni
Ahebri
Yakobo
I ndi II Petro
I, II ndi III Yohane
Yuda

Makalatawa amalembera kwa okhulupirira onse. Cholinga ndi chofuna kuwatsogolera makhalidwe awo ndi kuwathandiza kuchita zimene Yesu anawalamulira. Mukawerenga Aroma 12 kuti pali chitsanzo chabwino cha ziphunzitso. Tsekulani ndi kuwerenga ndime imeneyi bu Baibulo lanu. Makalatawa nthawi zina amatchedwanso ma “episito” kutanthauza kuti makalata.

**UNENERI:**

Chibvumbulutso ndi buku lokhalo la uneneri mu Chipangano Chatsopano. Bukuli limatsindika za chigonjetso chotsiriza cha Yesu ndi Anthu ake. Cholinga cha bukuli ndi kukulimbikitsani kuti mukhalebe mkhristu kufikira kumapeto kwa nthawi. Chidule cha uthenga wake chikupezeka pa Chibvumbulutso 2:10.

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima:
______________________________________________________________
______________________________________________________________
______________________________________________________

2. Kodi mawu oti “Baibulo amatanthauza chiyani?___________________________
3. Nanga mawu oti “Lembo” amatanthauza chiyani?___________________________
4. Kodi magulu awiri a Baibulo ndi ati?
   ___________________________  ______________________________
5. Kodi Mbaibulo muli mabuku okwanira angati?_____________________________
6. Tchulani magulu anayi amene amapanga mabuku a Chipangano Chatsopano:
   _____________________  _______________________________
   _____________________  _______________________________
7. Tchulani magulu anayi a akulu a Chipangano Chatsopano:
   _____________________________  _________________________
   _____________________________  _________________________
8. Kodi mawu okuti “Chipangano” akutanthauza chani?
   ____________________________________________________________
   ____________________________________________________________
9. Kodi zolinga zinayi za Baibulo ndi chani? Perekeni vesi poyankha funso limeneli.
   ____________________________________________________________
   ____________________________________________________________
   ____________________________________________________________
   ____________________________________________________________
10. Kodi “umodzi wa Baibulo” umatanthauza chiyani?
   ____________________________________________________________
11. Kodi “kuchuluka kwa Baibulo” kumatanthauza chiyani?
   ____________________________________________________________
12. Werengani chiganizo chili mmusimu ndipo gwiritsani ntchito mawu oti ZOONA kapena ZONAMA poyankha koyambirira kwa chiganizo.
   a.__________Baibulo ndi Lemba lolembedwa ndi Mulungu mmodzi woona.
   b.__________Ngakhale Mulungu anauzira Baibulo, koma adagwiritsa ntchito anthu kulemba mawu ake.
   c.__________Pokhala kuti anagwiritsa ntchito anthu ambiri kulemba kwa zaka zochuluka, Baibulo limadzitsutsa lokha.
   d.__________Mu Baibulo mulibe mutu umodzi wogwirizana. Langokhala unyinji wa mabuku omwe uli ndi mitu yosiyanasiyana.

d.____________Aneneri a akulu mu Chipangano Chakale ndiwo ofunika kwambiri kuposa aneneri a ang’ono.

13. Kodi mmavumbulutso onse Zipangano ziwiri akhazikika pa ndani? Lembani vesi lake poyankha funso limeneli.
___________________________________Vesi lake_____________________________

(Mayankho onse a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli).

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

Tsamba lotsatirali likuonetsa pomwe polekezera kuwerenga ndipo likuthandizani kuphunzira magawo a akulu a Baibulo. Dulani mzere polekezerapo pamene ikuwagawa ndipo ziikeni Mbaibulo lanu. Ngati mwakumana ndi mavuto pochita zimenezi, gwiritsani ntchito mitu imene ndi yopezeka mkatimo koyambirira kwa Baibulo lanu. Amalemba mabuku onse a Baibulo mu ndondomeko monga mmene alili mu Baibulo. Komanso tsamba lililonse lili ndi nambala koyambirira kwa buku lililonse.

## CHIPANGANO CHAKALE

Lembani polekezera 1 koyambirira kwa Genesis.

Lembani polekezera 2 koyambirira kwa Yoswa.

Lembani polekezera 3 koyambirira kwa buku la Yobu.

Lembani polekezera 4 koyambirira kwa buku la Yesaya.

## CHIPANGANO CHATSOPANO

Lembani polekezera 5 koyambirira kwa buku la Mateyu.

Lembani polekezera 6 koyambirira kwa buku la Machitidwe.

Lembani polekezera 7 koyambirira kwa buku la Aroma.

Lembani polekezera 8 koyambirira kwa buku la Chibvumbulutso.

Tsopano mwatha kuika magawo a akulu a Baibulo. Gwiritsani ntchito chionetserochi kufikira mutakwanitsa kutchula ndi kupezera malo ake magawo amenewa komakuchokera pamtima.

| **CHIPANGANO CHAKALE CHILAMULO (1)** | **CHIPANGANO CHAKALE MBIRI (2)** | **CHIPANGANO CHAKALE NDAKATULO (3)** |
|---|---|---|
| GENESIS | YOSWA | YOBU |
| EKSODO | OWERUZA | MASALMO |
| LEVITIKO | RUTE | MIYAMBO |
| NUMERI | I SAMUELI | MLALIKI |
| DEUTERONOMO | II SAMUELI | NYIMBO YA SOLOMONI |
| | I MAFUMU | |
| | II MAFUMU | |
| | I MBIRI | |
| | II MBIRI | |
| | EZARA | |
| | NEHEMIYA | |

ESTERE

**CHIPANGANO CHAKALE**
**UNENERI (4)**

ANENERI A AKULU
YESAYA
YEREMIYA
MALIRO
EZEKIELI
DANIELI

ANENERI A ANG'ONO
HOSEYA
YOWERI
AMOSI
OBADIYA
YONA
MIKA
NAHUMU
HABAKUKU
ZEFANIYA
HAGAI
ZAKARIYA
MALAKI

**CHIPANGANO CHATSOPANO**

**MAUTHENGA ABWINO (5)**
MATEYU
MARKO
LUKA
YOHANE

**CHIPANGANO CHATSOPANO**

**MBIRI (6)**
MACHITIDWE

**CHIPANGANO CHATSOPANO**

**MAKALATA (7)**
AROMA
I AKORINTO
II AKORINTO
AGALATIYA
AEFESO
AFILIPI
AKOLOSE
I ATESALONIKA
II ATESALONIKA
I TIMOTEO
II TIMOTEO
TITO
FILEMONI
AHEBRI
YAKOBO
I PETRO

II PETRO
I YOHANE
II YOHANE
III YOHANE
YUDA

---

**CHIPANGANO CHATSOPANO**
**UNENERI (8)**

CHIBVUMBULUTSO

## CHAPUTALA CHA 2

### MABUKU A M'BAIBULO

**ZOLINGA:**
Pakutha ma chaputala ichi muyenera:

- Kulemba vesi lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kuzindikira chiwerengero cha mabuku a Mchipangano Chakale.
- Kuzindikira chiwerengero cha mabuku a Mchipangano Chatsopano.
- Kulongosola chifunkwa chiyani ndi zofunika kukhala ndi dongosolo lowerenga Baibulo.
- Alembe zinthu zinayi za kuchita bwino powerenga Baibulo.

**VESI LOTSOGOLERA:**

**Kupfuula kwanga kuyandikire pamaso pano, Yehova;**
**Mundizindikiritse monga mwa mau anu (Masalmo 119:169).**

### MAWU OYAMBA

Muchaputala changothachi, mwaphunzira kuti Baibulo ndi Lemba lolembedwa ndi Mulungu. Ndiponso kuti lagawidwa magawo awiri a akulu; Chipangano Chakale ndi Chatsopano. Mwaphunziranso magawo anayi a Chipangano Chakale:

Chilamulo
Mbiri
Ndakatulo
Uneneri

Komanso mwaphunzira magawo anayi a Chipangano Chatsopano:

Mauthenga abwino
Mbiri
Makalata
Uneneri

Tchati lili pansili ndi chidule cha mmene mwaphunzirila:

BAIBULO
□
MAU A MULUNGU OLEMBEDWA
□
MABUKU 66
□

□ □

MAGAWO A CHIPANGANO CHAKALE | MAGAWO A CHIPAN CHATSOPANO

□ □

Chilamulo
Mbiri
Ndakatulo
Uneneri

Mauthenga abwino
Mbiri
Makalata
Uneneri

Chaputala ichi chikuonetsa chidule cha mabuku okwanira 66 omwe amapanga magawo a akulu a Chipangano Chakale ndi Chatsopano. Likupereka chiyambi cha zomwe zilimo mu zipangano zonse. Zinthu zinayi za kuchita bwino powerenga Baibulo zaperekedwa ndipo muzasankha dongosolo la mmene mungayambire kuwerenga Mau a Mulungu.

## CHIPANGANO CHAKALE

(Mabuku 39)

**MABUKU A CHILAMULO:**

Genesis: Amafotokoza za chiyambi cha dziko, munthu, Sabata, ukwati, tchimo, nsembe, mitundu ndi ulamuliro. Komanso amakamba za anthu ofunika ngati Abraham, Isaki, Yakobo ndi Yofefe.

Eksodo: Amakamba za tsatanetsatane wa mmene Israyeli anakhalira mtundu mosogoleredwa ndi Mose. Israyeli ndi mtundu umene unawomboledwa mu nsinga za Aigupto ndipo anayenda kufikira phiri la Sinayi kumene analandira lamulo Mulungu.

Levitiko: Bukuli amagwiritsa ntchito pa chipembedzo cha Israyeli. Komanso limapereka malangizzo kwa atsogoleri a chipembedzo ndi za mmene munthu wochimwa angafikire kwa Mulungu wolungama. Limafanana ndi kubwera kwa Yesu Khristu monga mwana wa nkhosa ya Mulungu amene achotsa tchimo.

Numeri: Amafotokoza za mbiri ya Israyeli ndi ulendo wawo wa mchipululu kwa zaka zokwana 40 chifukwa cha kusamvera Mulungu. Dzina la bukuli likuchokera ku chiwerenero cha ana Aisrayeli pa ulendo wautaliwu.

Deuteronomo: Bukuli limakamba za za masiku omaliza a moyo wa Mose, ndi kuonanso kwa malamulo omwe anaprekedwa mu Eksodo ndi Levitiko.

**MABUKU A MBIRI:**

Yoswa: Amafokoza zambiri za mmene Yoswa amene analowa mmalo mwa Mose, ndi kutsogolera Israyeli kudziko la malonjezo la Kanani. Limakambanso za kumemeza kwa asilikali ndi kugawana kwa malo kwa anthu.

Oweruza: Kubwerera mmbuyo kwa Israyeli atangofa Yoswa. Bukuli limakamba za nkhani yomvetsa chisoni ya kubwereza kwa machimo ndi oweruza amene Mulungu anawatuma kuti apulumutse Israyeli kwa adani awo.

Rute: Iyi ndi nkhani ya Rute, mkazi wamitundu wa ku moabu, amene anasankha kutumikira Mulungu wa Israyeli. Kumapeto adakhala kholo la Davide.

I Samueli: Bukuli limatsindika za anthu atatu: Samueli, amene anali woweruza womaliza wa Israyeli; Sauli amene anali mfumu yoyamba ya Israyeli, ndi Dvide amene analowa mmalo mwa Sauli.

II Samueli: Amafotokoza za zaka 40 za ulemerero wa ulamuliro wa Davide.

I Mafumu: Bukuli amafotokoza za ufumu wa mfumu Solomoni ndi mafumu a ufumu wogawanika a kumpoto kumene Ahabu amalamulira ndi kumwera kumene Yehosafati amalamulira.

II Mafumu: Kugwa kotsiriza kwa Israyeli ndi Yuda kukupezeka mbukuli. Anthu a Mulungu anagwa mu uchimo wakuya.

Ezara: Bukuli limafotokoza za kubwerera ka Ayuda kuchokera ku ukapolo wa Babulo.

Nehamiya: Limatsindika za kumangidwanso kwa chipata cha Yerusalemu pansi pa utsogoleri wa Nehemiya. Ntchitoyi inayamba patatha zaka 14 za kubwerera kwa Ezara ndi anthu.

Estere: Bukuli limafotokoza za chipulumutso cha Ayuda kudzera mwa Estere ndi Modekayi.

**MABUKU A NDAKATULO:**

Yobu: Bukuli muli nkhani ya Yobu, munthu amene anakhala mu nthawi ya Abrahamu. Mutu waukulu wa bukuli ndi funso lakuti ndichifukwa chiyani munthu wolunganma amasautsika.

Masalmo: Ili ndi buku la pemphero ndi matamando.

Miyambo: Iyi ndi mnzeru ya Umulingu pa zome timakumana nazo mmoyo watsiku ndi tsiku.

Mlaliki: Uwu ndi mkambirano wa kupanda kanthu kwa moyo wosadalira Mulungu.

Nyimbo ya Solomoni: Iyi ndi nyimbo ya chikondi cha Solomoni kwa mkazi wake wa ku Sulamiti. Nkhaniyi imaimirira chikondi cha Mulungu pa Israyeli ndi chikondi cha Yesu pa mpingo wake.

**MABUKU A UNENERI:**
Ambiri mwa mabukuwa analembedwa mu nthawi imene Israyeli anagawika kukhala maufumu awiri osiyana: Israyeli ndi Yuda.

Yesaya: Bukuli amachenjeza za chiweruza pa Ayuda chifukwa cha kuchimwira Mulungu.

Yeremiya: Bukuli linalembedwa kumapeto kwa kugwa kwa kwa ufumu wa Yuda. Ndipo amalankhula za chiweruzo ndi kugonjera kwa Nebukadinezara.

Maliro: Uku ndi kulira kwa Yeremiya (kuonetsa chisoni) pa kuonongedwa kwa Yerusalemu ndi Babulo.

Ezekieli: Umu muli uneneri wa kugwa koyamba kwa Yerusalemu ndi uneneri wa kubwenzeretsedwa kwake.

Danieli: Uku ndi kutengedwa kwa mneneri Danieli munthawi imene Yuda anali pa chitetezo kumka ku Babulo. Ndipo bukuli limafotokoza za mbiri ndi chiphunzitso cha uneneri chimene ndi chofunika pakumvetsa kwa uneneri wa Mbaibulo.

Hoseya: Mutu wa bukuli ndi Kusakhulupirika kwa Israyeli, chilango chawo, ndi kubwenzeretsedwa ndi Mulungu.

Yoweli: Amafotokoza za milili imene izaonekera mu chiweruzo cha mtsogolo.

Amosi: Pamene chuma cha kuthupi chachuluka, pamakhalanso kuonongeka kwa chikhalidwe. Amosi amawachenjeza ana Aisrayeli ndi maiko oyandikana nawo pa zachiweruzo cha Mulungu cha mtsogolo chifukwa cha machimo awo.

Obadiya: Chiweruza cha Mulungu pa Edomu, mtundu woipa wopezeka kumwera kwa Nyanja yakufa.

Yona: Iyi ndi nkhani ya mneneri Yona amene analalikira za kulapa ku Ninevi, mzinda wa ufumu wa Asuri. Bukuli limauluranso za chikondi cha Mulungu ndi dongosolo la kulapa kwa amitundu.

Mika: Uwu ndi uneneri wina wokhuza tchimo la Israyeli. Akuneneranso za malo amene Yesu azabadwirako koma patapita zaka zokwana 700 izi zisanachitike.
Nahumu: Amakamba za kubwera kwa chionongeka pa Ninevi chimene chinasiyidwa kwa zaka zokwana 150 kuchokera mkulalikira kwa Yona.

Habakuku: Limaulula za dongosolo la Mulungu lolanga mtundu wochimwa ndi wochimwitsitsa. Limaphunzitsa kuti "wolungama adzakhala ndi moyo ndi chikhuluiriro."

Zefaniya: Ichi ndi chiweruzo ndi kubwenzeretsedwa kwa Yuda.

Hagai: Bukuli limapempha Ayuda kumanganso kachisi atachedwetsedwa ndi adani kwa zaka zokwana 15.

Zakariya: Ili ndi pempho lopitilira la kumaliza kachisi ndi kudzikonzaso ku uzumu wawo. Limaneneranso za kubwera koyamba ndi kachiwiri kwa Khristu.

Malaki: Uneneri uwu ndi chenjezo pa kulowa pansi kwa moyo wa uzimu ndi kubwera kwa Yohane Mbatizi ndi Yesu.

## MABUKU A CHIPANGANO CHATSOPANO

(Mabuku 27)

**MAUTHENGA ABWINO:**
Mabuku oyambirira anayi Mchipangano Chatsopano ndi mauthenga. Mabuku amenewa ali ndi mbiri ya kubadwa, moyo, utumuki, ziphunzitso, imfa ndi kuuka kwa Yesu Khristu. Njira za buku lililonse ndi zosiyana:

**Mateyu:** Bukuli limamutchula Yesu ngati mfumu ya a Yuda. Ndipo koyamba ndi mndandanda wa makolo ake a Yesu. Ndipo mathero ake akuonetsa Yesu ngati mfumu akutuma ophunzira.

**Marko:** Bukuli limamutchula Yesu ngati mtumiki wa Mulungu kwa anthu amtundu wa Chiroma. Bukuli silikambapo za mndandanda wa makolo a Yesu chifukwa chakuti Yesu akuonetseredwa ngati mtumiki wa Mulungu ndipo palibe amene anaonetsa chidwi pa mbiri ya ubwino wake ngati mtumiki.

**Luka:** Mubuku ili Yesu akuonetseredwa ngati "Mwana wa Munthu" munthu wangwiro ndi mpulumutsi wa anthu ochimwa. Ndime 3 ya Luka akukammba za makolo a Yesu kuchokera kwa Adamu. Ndipo bukuli likumalizira ndi munthu wangwiro ameneyi, Yesu akukwera Kumwamba kwa Atate wake.

**Yohane:** Amakamba za Yesu ngati Mwana wa Mulungu monga mwa ulamuliro wake. Bukuli limayamba kufotokoza za Yesu ngati Mawu a Mulungu ovumbulutsidwa. Ndipo ndime yomaliza ya bukuli imaonetsa kuti dziko silikanakwanitsa kudziwa zonse za utumiki wake wa padziko lapansi. Uwu ndi umboni wapadera kuti analidi Mwana wa Mulunngu.

**BUKU LA MBIRI:**

Machitidwe: Buku la Machitidwe ndi buku lokhalo la mbiri mu Chipangano Chatsopano. Limakamba za zinthu zinthu zimene zinachitika pamene Ambuye Yesu atangokwera kupita kumwamba kufikira ukapolo wa Paulo wa Kwa Aroma. Bukuli limafotokoza zinthu zimene zinachitika kwa zaka zokwana 33 ndi kutsindika za ntchito za Mzimu Woyera.

**MAKALATA:**

**Aroma:** Kalata imeneyi imapereka uthenga umene umatsindika za chipulumutso mwa chikhulupiriro chokha.

**I Akorinto:** Iyi inalembedwa ndi cholinga chofuna kukonza makhalidwe olakwika a akhristu mu mpingo.

**II Akorinto:** Kalatayi imakamba za utumiki weniweni wa Uthenga Wabwino, Woyang’anira bwino chuma ndi ulamuliro wa mtumwi Paulo.

**Agalatiya:** Uthenga wa mu kalatayi umalimbana ndi zolakwika za kusakaniza lamulo ndi chikhulupiriro. Mutu waukulu mu kalatayi ndi kulungamitsidwa ndi chikhulupiriro chokha basi.

**Aefeso:** Kalatayi inalembedwa ndi cholinga chofuna kulimbikitsa okhulupirira onse amene amagawana malo a kumwamba limidzi ndi Yesu ngati ziwalo za mpingo.

**Afilipi:** Kalatayi imasindika za chimwemwe chakukhala Mkhristu.

**Akolose:** Iyi imalimbana ndi zolakwikwa za chipunzitso cha bodza chakuti chipulumutso timachipeza pokhala anzeru. Chiphunzisochi chimakana kuti Yesu analidi Mwana wa Mulungu ndi Mwana wa Munthu.

**I Atesalonika:** Limapereka uphungu wa makhalidwe a Chikhristu ndi kutsindika pa zakubweranso kwa Yesu.

**II Atesalonika:** Limapereka malangizo oonjezera pa za kubwera kwa Ambuye Yesu, ndi mmene angakhalire moyo wa tsiku ndi tsiku atatha kuzindikira malangizowa.

**I Timoteo:** Kalatayi imatsindika za chiphunzitso cholondora, dongosolo la utsogoleri wa mpingo ndi mfundo zotsogolera mpingo mu zaka zamtsogolo.

**II Timoteo:** Iyi imalongosola za Yesu Mkhristu ngati Mtumiki weniweni. Limachenjezanso za kulowa pansi kwa moyo wa uzimu kumene kudayamba kale, ndi kuonetsera Mawu a Mulungu ngati chida chokonza zolakwikwa.

**Tito:** Iyi ndi kalata ya Paulo yolembera mtumiki wachichepere wotchedwa Tito amene amatumikira Mulungu pa chilumba cha Krete. Bukuli limakamba za chiphunzitso ndi moyo wa umulungu.

**Filemoni:** Kalata iyi ndi pembedzero la Paulo kwa kapolo yemwe anathawa kwa Filimoni yemwe anali Mkhristu wochita bwino kwa Akolose. Limaonetsera pembedzero la Yesu mmalo mwa okhulupirira onse amene anamasulidwa ku ukapolo wa uchimo.

**Ahebri:** Kalata iyi imalongosola za kupambana kwa Chikhristu kuyerekeza ndi Chiyuda. Komanso limamufotokoza Yesu ngati Mkulu wa Nsembe mkhala pakati pa Mulungu ndi anthu.

**Yakobo:** Buku ili limaphunzitsa za Chikhulupiriro chenicheni chokhala ndi ntchito zake, ngakhale chipulumutso chimachokera ku chikhulupiriro chokha.

**I Petulo:** Iyi ndi kalata ya chitonthozo komanso chilimbikitso kwa okhulupirira, makamaka iwo amene akulandira chizunzo cha muuzimu kuchokera kwa iwo amene ndi osakhulupirira ali kunja kwa mpingo.

**II Petulo:** Kalata iyi imapereka chenjenzo kwa iwo amene akupereka chiopsezo cha kuuzimu kuchokera kwa iwo amene ali mkati mwa mpingo. Mwachitsanzo aphunzitsi oneynga amene anali ndi ma udindo mu mpingo.

**I Yohane:** Iyi ndi kalata imene idalembedwa ndi cholinga chofuna kulimbana ndi chiphunzitso cha nzeru chimene chimene chimakana kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu komanso Mwana wa Munthu. Komanso limalimbikitsa za chiyanjano komanso chikondi pakati pa okhulupirira ndi kuwatsikimizira kuti za moyo osatha.

**II Yohane:** Kalata iyi imachenjeza za kusakaniza chikhristu ndi chiphunzitso cholakwikwa, komanso kuti choonadi chitsogoleledwe ndi chikondi.

**III Yohane:** Kalata iyi imachenjeza za tchimo losafuna kuyanjana ndi omwe ndi okhulupirira owona.

**Yuda:** Iyi imapereka chenjezonso koma lotsutsana ndi kulowa pansi kwa moyo wa uzimu ndi chiphunzitso cha bodza. Mutu wa kalatayi umafanana ndi kalata ya II Petulo.

**BUKU LA UNENERI:**

**Chibvumbulutso:** Ili ndi buku la uneneri mu Chipangano Chatsopano. Limanenera zinthu zotsiriza za mbiri ya dziko zimene zidzachitika mtsogolo. Limakambanso za zinthu zimene tinali, zimene tili, ndi zimene tidzakhala mu dongosolo la Mulungu.

**KUCHITA BWINO PA KUWERENGA BAIBULO**

Muphunzira zambiri mu phunziroli zokhuza mmene mungamvetsetsere ndi kutanthauzira Baibulo. Muphunziranso njira za kawerengedwe ka Baibulo. Koma gawo loyamba lomvetsetsa Baibulo ndiko kuyamba kuliwerenga. Kufuna kukuthandizani kuwerenga Mau a Mulungu, taika mndandanda wa dongosolo la mmene mungawerengere. Dongosolo limeneli ndi la iwonso amene angoyamba kuwerenga komanso iwo amene anayambapo ndipo amachita bwino kuwerenga kwawo Mau a Mulungu.

Koyamba, izi ndi njira zinayi zimene zingakuthandizeni kuchita bwino kuwerenga:

1. **WERENGANI TSIKU NDI TSIKU:**

   **Komatu m'cilamulo ca Yehova muli cikondwerero cace; Ndipo m'cilamulo cace amalingima usana ndi usiku (Masalmo 1:2).**

Mulungu analenga thupi lanu ndi cholinga choti mudzidya tsiku ndi tsiku kuti mukhale athanzi. Momwenso, mzimu wanu muyenera kuudyetsa chakudya tsiku ndi tsiku chimene ndi Mau a Mulungu ngati mukufunadi kukhala anthanzi ku uzimu:

**…Kwalembedwa, kuti, Munthu sadzakhala ndi moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mau ochokera kwa Mulungu (Luka 4:4).**

2. **WERENGANI MOSANKHA:**

Yambani ndi kuwerenga "mkaka" wa mawu. Zimenezi ndi choonadi chosavuta cha Mau a Mulungu:

**Lirani monga makanda alero mkaka woyenera, wopanda cinyengo, kuti mukakule nao kufikira cipulumutso (I Petro 2:2).**

Kumapeto kwake mudzakula mu uzimu pamene muzayamba kudya "nyama" ya Mau a Mulungu. Izi zikutanthauza kuti mudzayamba kumvetsetsa ziphunzitso zovuta za Baibulo:

**Pakuti yense wakudya mkaka alibe cizolowezi ca mau a cilungamo; pakuti ali khanda.**

**Koma cakudya cotafuna ciri ca anthu akulu misinkhu, amene mwa kucita nazo anazoloweretsa zizindikiritso zao (Ahebri 5:13-14).**

**Ndinaiyetsa inu mkaka, si cakudya colimba ai; pakuti simunakhoza; ngakhale tsopano lino simucikhoza; pakuti mulinso athupi (I Akorinto 3:2).**

3. **WERENGANI MWAPEMPHERO:**

   **Pakuti Ezara adaikiratu mtima wace kucifuna cilamulo ca Yehova (Ezara 7:10).**

Musanayambe kuwerenga, pempherani kwa Mulungu ndi kumpempha kuti akuthandizeni kumvetsetsa uthenga umene akupatseni kudzera mmawu ake olembedwa. Mulole mapemphero anu akhale ngati Davide wolemba Masalmo anapempherera:

> **Munditsegulire maso, kuti ndipenye zodabwiza za m'cilamulo canu (Masalmo 119:18).**

4. **WERENGANI MWANDONDOMEKO:**

Anthu ambiri samvetsa Mau a Mulungu chifukwa alibe dongosolo la ndondomeko ya kawerengedwe. Amatha kuwerenga chaputala apa ndi apo ndi kulephera kumvetsa mmene zikulumikizirana. Uku kulingati kuwerenga masamba ochepa apa ndi apo mu buku la mankhwala kenako kuyesera kugwiritsa ntchito mankhwalawo.

Baibulo limatiuza kuti "santhulani malembo onse" (Yohane 5:39). Izi zikutanthauza kuti kuwerenga mosamala. Baibulo lili ngati buku limene limagwiritsidwa ku sukulu. Choncho mukuyenera kuliwerenga mwandondomeko ngati mukufuna kumvetsa zimene mukuwerenga. Sankhani imodzi mwa ndondomeko za kawerengedwe ndipo yambani kuwerenga Baibulo lanu tsiku ndi tsiku.

### KWA IWO ANGOYAMBA KUMEME

Ngati simunawerengepo Baibulo chiyambireni, yambani kuwerenga bulu la Yohane mu Chipangano Chatsopano. Bukuli linalembedwa ndi mmodzi mwa ophunzira a Yesu Khristu wotchedwa Yohane. Amatiuza nkhani ya Yesu mosavuta kuimvetsetsa. Werengani chaputala chimodzi mu buku la Yohane tsiku lililonse mundondomeko yogwirizana ndi mmene alembera mbukulo. Gwiritsani ntchito tchatichi pofuna kuona kuti chaputala chilichonse pamene mukuwerenga.

**Uthenga wabwino wa Yohane:**

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| _____1 | _____5 | _____9 | _____13 | _____17 |
| _____2 | _____6 | _____10 | _____14 | _____18 |
| _____3 | _____7 | _____11 | _____15 | _____19 |
| _____4 | _____8 | _____12 | _____16 | _____20 |

### DONGOSOLO LALIFUPI

Ndondomeko ya kawerengedwe ka Baibulo yaifupi yapangidwa ndi cholinga chofuna kuyala maziko a chidziwitso cha Baibulo kudzera mkusankha ndime zochepa za Malemba. Werengani

ndime zasankhidwazi mundondomeko imene aziikira. Gwiritsani ntchito tchati pofuna kuona gawo lililonse pamene mukumaliza kuwerenga kwanu.

**CHIPANGANO CHATSOPANO:**

_____Yoahane
_____I Atesalonika
_____Aefeso
_____Marko
_____I Akorinto
_____II Timoteo
_____Luka
_____Aroma
_____I Petro
_____Machitidwe
_____Filemoni
_____I Yohane
_____Aroma
_____Afilipi
_____Chibvumbulutso 1-5; 19:6-22:21

**CHIPANGANO CHAKALE:**

______Genesis
_____Amosi
______Eksodo l-20
_____Yesaya l-12
______Numeri 10:11-21:35
_____Yeremiya l-25;39-33
______Deuteronomo l-11
_____Rute
______Yoswa l-12; 22-24
_____Yona
______Oweruza l-3
_____Masalmo l-23
______I Samueli l-3, 9-10,1 3,15-18,31
_____Yobu1-14, 38-42
______II Samueli l
_____Miyambo 1-9
______I Mafumu l-11
_____Danieli 1-6
______Nehemiya

## DONGOSOLO LALITALI

Dongosolo limeneli limatenga mbali yaikulu ya mwakuya kuposa dongosolo lalifupi, koma silimafikira Baibulo lonse.

**CHIPANGANO CHATSOPANO:**

_____Marko
_____Afilipi
_____Mateyu
_____Aefeso

_____Yohane

_____Luka

_____Machitidwe

_____I Atesalonika

_____II Atesalonika

_____I Akorinto

_____II Akorinto

_____Agalatiya

_____Aroma

_____Filimoni

_____Akolose

_____II Timoteo

_____Tito

_____I Timoteo

_____I Petro

_____Ahebri

_____Yakobo

_____I Yohane

_____II Yohane

_____III Yohane

_____Yuda

_____II Petro

_____Chibvumbutso 1-5 and 19:6-22:21

**CHIPANGANO CHAKALE:**

_____Genesis

_____Eksodo (l-24)

_____Levitiko l-6:7

_____Numeri 10:11-21:35

_____Deuteronomo l-11 ndi 27-34

_____Yoswa l-12 ndi 22-24

_____Oweruza l-16

_____I Samueli

_____II Samueli

_____I Mafumu

_____II Mafumu

_____Yeremiya 1-25 ndi 30-33

_____Nahumu

_____Habakuku

_____Ezekieli 1-24 ndi 33-39

_____Obadiya

_____Maliro

_____Yesaya 40-66

_____Zakariya 1-8

_____Malaki

_____Yoweli

_____Rute

_____I Mbiri

_____II Mbiri

_____Ezara

_____Nehemiya

_____Amosi

_____Hoseya

_____Mika

_____Yesaya l-12

_____Zefaniya

_____Yona

_____Masalmo

_____Yobu

_____Miyambo 1-9

_____Nyombo ya Solomoni

_____Mlaliki

_____Estere

_____Danieli

## DONGOSOLO LONSE LA KAWERENGEDWE KA BAIBULO

Dongosolo lonse la kawerengedwe mumawerenga Baibulo lonse mu ndandanda uwu:

**Januwale**

_____1. Genesis l-2

_____2. Genesis 3-5

_____3. Genesis 6-9

_____4. Genesis 10-11

_____5. Genesis 12-15

_____6. Genesis 16-19

_____7. Genesis 20-22

_____8. Genesis 23-26

_____9. Genesis 27-29

_____10. Genesis 30-32

_____11. Genesis 33-36

_____12. Genesis 37-39

**Febuwale**

_____1. Eksodo 14-17

_____2. Eksodo 18-20

_____3. Eksodo 21-24

_____4. Eksodo 25-27

_____5. Eksodo 28-31

_____6. Eksodo 32-34

_____7. Eksodo 35-37

_____8. Eksodo 38-40

_____9. Levitiko 1-4

_____10. Levitiko 5-7

_____11. Levitiko 8-10

_____12. Levitiko 11-13

______13.  Genesis 40-42

______14.  Genesis 43-46

______15.  Genesis 47-50

______16.  Yobu 1-4

______17.  Yobu 5-7

______18.  Yobu 8-10

______19.  Yobu ll-13

____20.  Yobu 14-17

______21.  Yobu 18-20

______22.  Yobu 21-24

______23.  Yobu 25-27

______24.  Yobu 28-31

______25.  Yobu 32-34

______26.  Yobu 35-37

______27.  Yobu 38-42

______28.  Eksodo l-4

______29.  Eksodo 5-7

______30.  Eksodo 8-10

______31.  Eksodo 11-13

______13.  Levitiko 14-16

______14.  Levitiko 17-19

______15.  Levitiko 20-23

______16.  Levitiko 24-27

______17.  Numeri 1-3

______18.  Numeri 4-6

______19.  Numeri 7-10

______20.  Numeri 11-14

______21.  Numeri 15-17

______22.  Numeri 18-20

______23.  Numeri 21-24

______24.  Numeri 25-27

______25.  Numeri 28-30

______26.  Numeri 31-33

______27.  Numeri 34-36

______28.  Deuteronomo 1-3

**Marichi**

______1.  Deuteronomo 4-6

______2.  Deuteronomo 7-9

______3.  Deuteronomo 10-12

______4.  Deuteronomo 13-16

**Epulo**

______1.  I Samueli 21-24

______2.  I Samueli 25-28

______3.  I Samueli 29-31

______4.  II Samueli 1-4

______5.  Deuteronomo 17-19

______6.  Deuteronomo 20-22

______7.  Deuteronomo 23-25

______8.  Deuteronomo 26-28

______9.  Deuteronomo 29-31

______10.  Deuteronomo 32-34

______11.  Yoswa 1-3

______12.  Yoswa 4-6

______13.  Yoswa 7-9

______14.  Yoswa 10-12

______15.  Yoswa 13-15

______16.  Yoswa 16-18

______17.  Yoswa 19-21

______18.  Yoswa 22-24

______19.  Oweruza 1-4

______20.  Oweruza 5-8

_____21.  Oweruza 9-12

______22.  Oweruza 13-15

______23.  Oweruza 16-18

______24.  Oweruza 19-21

______25.  Rute 1-4

______26.  I Samueli 1-3

______27.  I Samueli 4-7

______28.  I Samueli 8-10

______29.  I Samueli ll-13

______5.  II Samueli 5-8

______6.  II Samueli 9-12

______7.  II Samueli 13-15

______8.  II Samueli 16-18

______9.  II Samueli 19-21

______10.  II Samueli 22-24

______11.  Masalmo l-3

______12.  Masalmo 4-6

______13.  Masalmo 7-9

______14.  Masalmo 10-12

______15.  Masalmo 13-15

______16.  Masalmo 16-18

______17.  Masalmo 19-21

______18.  Masalmo 22-24

______19.  Masalmo 25-27

______20.  Masalmo 28-30

______21.  Masalmo 31-33

______22.  Masalmo 34-36

______23.  Masalmo 37-39

______24.  Masalmo 40-42

______25.  Masalmo 43-45

______26.  Masalmo 46-48

______27.  Masalmo 49-51

______28.  Masalmo 52-54

______29.  Masalmo 55-57

______30.  I Samueli 14-16

______31.  I Samueli 17-20

______30. Masalmo 58-60

**Meyi**

______1.  Masalmo 61-63

______2.  Masalmo 64-66

______3.  Masalmo 67-69

______4.  Masalmo 70-72

______5.  Masalmo 73-75

______6.  Masalmo 76-78

______7.  Masalmo 79-81

______8.  Masalmo 82-84

______9.  Masalmo 85-87

______10.  Masalmo 88-90

______11.  Masalmo 91-93

______12.  Masalmo 94-96

______13.  Masalmo 97-99

______14.  Masalmo 100-102

______15.  Masalmo 103-105

______16.  Masalmo 106-108

______17.  Masalmo 109-111

______18.  Masalmo 112-114

______19.  Masalmo 115-118

_____20.  Masalmo 119

______21.  Masalmo 120-123

**Juni**

______1.  Miyambo 1-3

______2.  Miyambo 4-7

______3.  Miyambo 8-11

______4.  Miyambo 12-14

______5.  Miyambo 15-18

______6.  Miyambo 19-21

______7.  Miyambo 22-24

______8.  Miyambo 25-28

______9.  Miyambo 29-31

______10.  Mlaliki 1-3

______11.  Mlaliki 4-6

______12.  Mlaliki 7-9

______13.  Mlaliki 10-12

______14.  Nyimbo ya Solomoni 1-4

______15.  Nyimbo ya Solomoni 5-8

______16.  I Mafumu 5-7

______17.  I Mafumu 8-10

______18.  I Mafumu 11-13

______19.  I Mafumu 14-16

______20.  I Mafumu 17-19

______21.  I Mafumu 20-22

______22.  Masalmo 124-126

______23.  Masalmo 127-129

______24.  Masalmo 130-132

______25.  Masalmo 133-135

______26.  Masalmo 136-138

______27.  Masalmo 139-141

______28.  Masalmo 142-144

______29.  Masalmo 145-147

______30.  Masalmo 148-150

______31.  I Kings l-4

______22.  II Mafumu 1-3

______23.  II Mafumu 4-6

______24.  II Mafumu 7-10

______25.  II Mafumu 11-14:20

______26.  Yoweli 1-3

______27. II Mafumu 14:21-25; Yona 1-4

______28.  II Mafumu 14:26-29; Amosi 1-3

______29.  Amosi 4-6

______30.  Amosi 7-9

**Julaye**

______1.  II Mafumu 15-17

______2.  Hoseya l-4

______3.  Hoseya 5-7

______4.  Hoseya 8-10

______5.  Hoseya ll-14

______6.  II Mafumu 18-19

______7.  Yesaya l-3

______8.  Yesaya 4-6

______9.  Yesaya 7-9

______10.  Yesaya 10-12

______11.  Yesaya 13-15

______12.  Yesaya 16-18

______13.  Yesaya 19-21

**Ogasiti**

______1.  II Mafumu 20-21

______2.  Zefaniya l-3

______3.  Habakuku 1-3

______4.  II Mafumu 22-25

______5.  Obadiya/Yeremiya 1-2

______6.  Yeremiya 3-5

______7.  Yeremiya 6-8

______8.  Yeremiya 9-12

______9.  Yeremiya 13-16

______10.  Yeremiya 17-20

______11.  Yeremiya 21-23

______12.  Yeremiya 24-26

______13.  Yeremiya 27-29

______14.  Yesaya 22-24
______15.  Yesaya 25-27
______16.  Yesaya 28-30
______17.  Yesaya 31-33
______18.  Yesaya 34-36
______19.  Yesaya 37-39
______20.  Yesaya 40-42
______21.  Yesaya 43-45
______22.  Yesaya 46-48
______23.  Yesaya 49-51
______24.  Yesaya 52-54
______25.  Yesaya 55-57
______26.  Yesaya 58-60
______27.  Yesaya 61-63
______28.  Yesaya 64-66
______29.  Mika 1-4
______30.  Mika 5-7
______31.  Nahumu 1-3

______14.  Yeremiya 30-32
______15.  Yeremiya 33-36
______16.  Yeremiya 37-39
______17.  Yeremiya 40-42
______18.  Yeremiya 43-46
______19.  Yeremiya 47-49
______20.  Yeremiya 50-52
______21.  Maliro 1-5
______22.  I Mbiri 1-3
______23.  I Mbiri 4-6
______24.  I Mbiri 7-9
______25.  I Mbiri 10-13
______26.  I Mbiri 14-16
______27.  I Mbiri 17-19
______28.  I Mbiri 20-23
______29.  I Mbiri 24-26
______30.  I Mbiri 27-29
______31.  II Mbiri 1-3

**Sepetembala**

______1.  II Mbiri 4-6
______2.  II Mbiri 7-9
______3.  II Mbiri 10-13
______4.  II Mbiri 14-16
______5.  II Mbiri 17-19

**Okotobala**

______1.  Estere 4-7
______2.  Estere 8-10
______3.  Ezara 1-4
______4.  Hagai 1-2/Zakariya 1-2
______5.  Zakariya 1-2

______6. II Mbiri 20-22

______7. II Mbiri 23-25

______8. II Mbiri 26-29

______9. II Mbiri 30-32

______10. II Mbiri 33-36

______11. Ezekieli 1-3

______12. Ezekieli 4-7

______13. Ezekieli 8-11

______14. Ezekieli 12-14

______15. Ezekieli 15-18

______16. Ezekieli 19-21

______17. Ezekieli 22-24

______18. Ezekieli 25-27

______19. Ezekieli 28-30

______20. Ezekieli 31-33

______21. Ezekieli 34-36

______22. Ezekieli 37-39

______23. Ezekieli 40-42

______24. Ezekieli 43-45

______25. Ezekieli 46-48

______26. Danieli 1-3

______27. Danieli 4-6

______28. Danieli 7-9

______29. Danieli 10-12

______30. Estere l-3

______6. Zakariya 3-6

______7. Zakariya 7-10

______8. Ezara 5-7

______9. Ezara 8-10

______10. Nehemiya l-3

______11. Nehemiya 4-6

______12. Nehemiya 7-9

______13. Nehemiya 10-13

______14. Malaki l-4

______15. Mateyu 1-4

______16. Mateyu 5-7

______17. Mateyu 8-11

______18. Mateyu 12-15

______19. Mateyu 16-19

______20. Mateyu 20-22

______21. Mateyu 23-25

______22. Mateyu 26-28

______23. Marko l-3

______24. Marko 4-6

______25. Marko 7-10

______26. Marko ll-13

______27. Marko 14-16

______28. Luka l-3

______29. Luka 4-6

______30. Luka 7-9

______31.  Luka 10-13

**Novembala**

______1.  Luka 14-17

______2.  Luka 18-21

______3.  Luka 22-24

______4.  Yohane 1-3

______5.  Yohane 4-6

______6.  Yohane 7-10

______7.  Yohane 11-13

______8.  Yohane 14-17

______9.  Yohane 18-21

______10.  Machitidwe 1-2

______11.  Machitidwe 3-5

______12.  Machitidwe 6-9

______13.  Machitidwe 10-12

______14.  Machitidwe 13-14

______15.  Yakobo 1-2

______16.  Yakobo 3-5

______17.  Agalatita l-3

______18.  Agalatiya 4-6

______19.  Machitdwe 15-18:11

______20.  I Atesalonika l-5

______21.  II Atesalonika l-3

______22.  I Akorinto 1-4

**Disembala**

______1.  Aroma 5-8

______2.  Aroma 9-11

______3.  Aroma 12-16

______4.  Machitidwe 20:3-22

______5.  Machitidwe 23-25

______6.  Machitidwe 26-28

______7.  Aefeso 1-3

______8.  Aefeso 4-6

______9.  Afilipi 1-4

______10.  Akolose 1-4

______11.  Ahebri 1-4

______12.  Ahebri 5-7

______13.  Ahebri 8-10

______14.  Ahebri 11-13

______15.  Filemoni/I Petro 1-2

______16.  I Petro 3-5

______17.  II Petro 1-3

______18.  I Timoteo l-3

______19.  I Timoteo 4-6

______20.  Tito l-3

______21.  II Timoteo l-4

______22.  I Yohane l-2; Machitidwe 18:12-19:10

_____23. I Yohane 3-5

_____24. II Yohane, III Yohane

_____25. Chibvumbulutso 1-3, Yuda

_____26. Chibvumbulutso 4-6

_____27. Chibvumbulutso 7-9

_____28. Chibvumbulutso 10-12

_____29. Chibvumbulutso 13-15

_____30. Chibvumbulutso 16-18

_____31. Chibvumbulutso 19-22

_____23. I Akorinto 5-8

____24. I Akorinto 9-12

_____25. I Akorinto 13-16

_____26. Machitidwe 19:11-20:1; II Akorinto 1-3

_____27. II Akorinto 4-6

_____28. II Akorinto 7-9

_____29. II Akorinto 10-13

_____30. Machitidwe 20:2/Aroma 1-4

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera kuchokera pamtima.

___________________________________________
___________________________________________
___________________________________________

2. Kodi mu Chipangano Chakale muli mabuku angati?

___________________________________________

3. Nanga mu chipangano chatsopano muli mabuku angati?

___________________________________________

4. Chifukwa chiyani ndi zofunikira kukhala ndi dongosolo lowerenga Baibulo?

___________________________________________
___________________________________________
___________________________________________

5. Kodi ndi zinthu ziti zinayi zimaonetsa kuchita bwino powerenga Baibulo?

___________________________________________
___________________________________________
___________________________________________
___________________________________________

**(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli).**

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

-Onaninso za mmene buku lililonse alilongosolera Mbaibulo mu chaputala chimenechi.
-Lembani dzina la buku lililonse la Baibulo mmusimu.
-Monga mwa dzina la buku lililonse, lembani chidule cha bukulo mmawu atatu kapena anayi.
-Ziwiri zoyambazi akulemberani kale ngati chitsanzo choti mutsatire.
(Pakumvetsetsa zinthu mu zimenezi, mukhoza kupanga chidziwitso cha zonse zimene zikupezeka Mbaibulo).

| **Dzina la Buku** | **Zomwe zikupezekamo** |
|---|---|
| Genesis | Buku la chiyambi |
| Eksodo | Kutuluka kwa Aigupto |

## CHAPUTALA CHA 3

CHIYANKHULO CHA BAIBULO

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputala ichi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kutchula chiyankhulo chimene Baibulo chinalembedwa.
- Kupereka tanthauzo la mawu oti "chiyankhulo."
- Alongosole kusiyana pakati pa chitanthauziro ndi chiyankhulo chachidule cha Baibulo.

**VESI LOTSOGOLERA:**

**Ambuye anapatsa mau: Akazi akulalikira uthengawo ndiwo khamu lalikuru (Masalmo 68:11).**

### MAWU OYAMBA

Chaputala ichi chikutionetsera ziyankhulo zimene Baibulo linalembedwandi kulongosola mmene Malemba anatanthauzilidwa ku zilankhulo zina. Muphunziranzo kusiyana pakati pa kutanthauzira ndi malembedwe a Baibulo achidule. Zitsanzo za malembedwe osiyanasiyana a Baibulo zaperekedwanso.

### ZILANKHULO ZITATU

Pachiyambi, Baibulo linalembedwa mu zilankhulo zitatu. Gawo lalikulu la Chipangano Chakale linalembedwa mu Chibeli kupatula magawi a mabuku a Danieli ndi Nehemiya amene analembedwa mu Aramaiki. Pomwe Chipangano Chatsopano chinalembedwa mu Chigiriki.

Pakadali pano pa zilankhulo zonsezi za Baibulo zatchulidwazi palibepo zolembedwa zawo ndi chimodzi chomwe. Zina mwa zolembedwa zawo zabwino zimapezeka. Mtundu wa kalembedwe ndi matanthauziro a zolembedwazi zoyambazi. Kuchokera nthawi imeneyo, anthu adaona kuti ndikofunika kwambiri kutanthauzira Baibulo muzilankhulo zimene aliyense akhoza kuwerenga.

Choncho palibe chitanthauziro chenicheni chifukwa choti ngakhale zilankhulo zingapo sizifana. Choncho mawu ena amene anagwiritsidwa ntchito Mbaibulo samapezeka mu zilznkhulo zosiyana. Mwachitsanzo ngati mtundu wa Achimwenye ku Ekuda, kumwera cha Ulaya otchedwa Auka. Pamene a mishoni anafikako munthawi yawo yoyamba amwenyewa samadziwa kuwerenga ndi kulemba. Pakuti munalibe mawu mu chilanhkulo chawo oti akanatha "kulemba" kapena "buku."

Amwenye amenewa analibe chikhalidwe chosema kuika zizindikiro pa katundu wawo. Chifukwa chakuti munalibe mawu mu chilankhulo chawo ngati “kulemba” kapena “buku” pamene Baibulo linatanthauzilidwa kwa iwo ngati “Chosema cha Mulungu.” Ichi chimadziwika ngati chithu cha Mulungu. Chimenechi ndi chitsanzo chabe cha vuto lotanthauzira Baibulo ku zilankhulo zambiri.

## MATANTHAUZIRO NDI KUBWEREZANSO

Pali matanthauziro a Baibulo osiyanasiyana. Mawu oti “chitanthauziro” akutanthauza kuti Baibulo linalembedwa mu chiyankhulo chosiyana ndi chimene Mau a Mulungu analili pachiyambi. Choncho pali ziyankhulo ziwiri za Baibulo: Matanthauziro ndi chidule.

### MATANTHAUZIRO:

Iyi inali ntchito yowonetsera chimene chi Giriki, Chiheberi ndi chi Aramaiki chimalankhula. Kunali kuonetsera tanthauzo limene silimathawana ndi mawu ake enieni. Mawu ena owonjezera amaikidwamo pokhapokha ngati zinali zofunika ndi cholinga choti wowerenga the kumvetsetsa.

### KUBWEREZANSO:

Uku sikunali kutanthauzira mawu ena aliwonse ayi. Koma kunali kutanthauzira ganizo pa ganizo. Uku kunali kubwerezanso zomwe zinalankhulidwa mu mawu ena koma osasintha tanthauzo. Chiyankhulo chobwerenzaso chimakhala chosavuta kuwerenga komanso kumvetsa chifukwa choti zimakhala kuri zalembedwa mu chilankhulo chatsopano koma tanthauzo la Mau a Mulungu silikhalilatu lofanana ngati mmene linalili.

Pa gawo la “kupitiliza kuphunzira” mu chaputala ichi, muli zitsanzo za ziyankhulo za Baibulo za chingerezi zomwe mukuyenera kuti muzifananitse. Zitsanzozi zikuonetsa kusiyana kwa chitanthauziro ndi kubwerezanso.

## KUSANKHA BAIBULO LOPHUNZIRIRA

Chifukwa cha phunziro ili ndi kufuna kuphunzira Baibulo, ndibwino kugwiritsa ntchito Baibulo lotanthauzidwa ndi King James. Zifukwa zosankhira King James ndi izi:

### CHOYAMBA:

Bukuli limaoneka kuti ndi lolondolo ndiponso ndi labwino pa maphunziro a Baibulo. Pomwe matanthauziro obwereza amaoneka kuti sakhala ndi mawu olondola monga mmene analili mu Malembo ake.

### CHACHIWIRI:

Mu buku la King James muli zipangizo zambiri zimene mungathe kugwiritsa ntchito pophunzira Baibulo. Mulinso gawo lalikulu la nkhokwe ya mawu, zowonjezera, ndi matanthauzo a mawu ambiri ndi zina.

**CHACHITATU:**

Bukuli lilinso mu zilankhulo zambiri kusiyana ndi matanthauziro ena. Podziwa kuti maphunziro athu a ife a Harvestime International Institute amagwiritsidwa ntchito padziko lonse, tidasankha buku limeneli chifukwa lili mu zilankhulo zambiiri. Choncho ndizofunika kukhala ndi Baibulo limene ndi lolembedwa mu chilankhulo chanu chifukwa mumatha kuganiza ndi kumvetsa muziyankhulo zanu.

Ngati mulibe Baibulo la chiyankhulo cha King James lemberani ku adilesi iyi: American Bible Society P.O Box 5601, Grang Central Station, New York 10164, U.S.A. Iwowa ali ndi Baibulo a zilankhulo zonse kuphatikizapo King James. Ngati mupeze kuti Baibuloli silili mu chiyankhulo chanu, kapena mukukumana ndi zovuta kulipeza, lemberani ku: United Bible Societies, Bible House, P.O. Box 755, Stuttgart l, Germany. Iwowa amasungabe ndandanda wa "Malemba a dziko" amene amazindikira zilankhulo zonse za padziko lapansi zimene Baibulo lake lilipo.

Ngati mumakwanitsa kuwerenga Chingerezi, koma mawu ena simuwadziwa, zingakhale bwino mutapeza "Baibulo la Chingerezi chosavuta." Baibuloli limakhala ndi chipangano chakale ndi chatsopano chomwe koma lolembedwa mu chingerezi pogwiritsa ntchito mawu 1,000 odziwika. Lemberani ku: Cambridge University Press, New York, New York, U.S.A. Kuti mudziwe zambiri.

## ZILEMBO ZOFIIRA

Zilankhulo zambiri za Baibulo, zinabwera ndi mawu ena "olembedwa zofiira." Mawuwa amakhala kuti analankhula ndi Yesu. Mawu ena onse amalembedwa mu zilembo za mtundu wakuda.

Ngati zilembo zofiira za King James zikupezeka mu chilankhulo chanu, ndiye kuti munalipeza. Zimene Yesu anaphunzitsa ndi limodzi mwa magawo a akulu amene ife a Harvestime International Institute timakhazikikapo pa maphunziro athu ndipo zilembo zofiirazi ndizo ziphunzitso zake za Yesu.

## CHIDULE

Tchati lili mmusimu ndi chidule cha zilankhulo zosiyanasiyana za Baibulo:

Baibulo:

Louzilidwa ndi Mulungu

□

Lovumbulutsidwa kwa anthu opatulika amene analemba Mau a Mulungu

Mu Chigiriki, Chiheberi ndi Chi amaraiki

□

Lotanthauzilidwa mu zilankhulo zambiri

Zotsatira zake ndi

□

Chitanthauziro chenicheni ndi chibwerezo cha chiyankhulo cha Baibulo

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Veso Lotsogolera kuchokera pamtima.

2. Kodi mawu oti “chiyankhulo akutanthauza chiyani?

3. Kodi pali kusiyana kwanji pakati pa “chitanthauziro cha Baibulo ndi chibwerezo cha chiyankhulo cha Baibulo.

4. Kodi ndi mtundu wanji wa chiyankhulo cha Baibulo umene ukugwiritsidwa ntchito mmaphunzirowa?

5. Kodi ndi chifukwa chiyani palibe chitanthauzire chenicheni cha Baibulo?

6. Kodi ndi zilankhulo zitatu ziti zimene Baibulo linalembedwa pa chiyambi?

**(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa phunziroli).**

## CHAPUTALA CHA 4

KUONETSA MAGAWO

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputala ichi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kupereka tanthauzo la mawu oti “chigawo”
- Kuwerenga chigawo.
- Kupanga chigawo.

**VESI LOTSOGOLERA:**

> **Ananenanso nane, Wobadwa ndi munthu iwe, mau anga onse ndidzawanena ndi iwe uwalandire m'mtima mwako, utawamva m'makutu mwako (Ezekieli 3:10).**

### MAWU OYAMBA

“*Kafukufuku wa Baibulo I”* amakhudzanso magawo a buku lililonse la muchipangano chakale. Magawowa amapereka chithunzithunzi cha zimene zikupezeka mmawu a Mulungu. Tsatanetsatane wa wa magawowa akupezeka mu *“Kafukufuku wa Baibulo II* “wa mauthenga abwino, Machitidwe ndi Makalata molingana ndi chidwi chawo pa Harvestime International Institute. Sukuluyi imatsindika pa zimene Yesu anaphunzitsa ndi zotsatira zake pamene ziphunzitso zake zimagwira ntchito mupmingo woyamba uja.

Magawowa mu phunziroli akupereka chidule chabe cha zomwe zikupezeka mu buku lililonse la Mbaibulo. Pamene mwamaliza kafukufuku ameneyi mukyenera kubwereranso ndi kuyambanso kuphunzira buku lililonse mwatsatanetsatane. Magawo amenewa pangokhala pongoyambira basi kuti mukakhazikike pa kupanga zowerenga zanu za buku lililonse la Mbaibulo. Koma kuti izi zitheke, mukuyenera kudziwa za mmene mungapangire gawo loyenera.

### MNDANDANDA

Mndandanda ndi njira imodzi yokonza zolemba zomwe tikufuna kuziphunzira kapena kuziphunzitsa. Imakhaka njira yobweretsa zinthu pamodzi koma mwachidule kuti zizagwire ntchito mu utumiki kutsogolo kapena kuphunzira. Mndandanda umakuthandizani kuti “mumve ndi makutu anu ndi kulandira ndi mtima wanu” mau a Mulungu (Ezekieli 3:10). Mndandanda umakhazikika pa mwini nkhani yomwe mwasankha. Mwininkhaniyi amakhala mutu wa mndandanda. Tagwiritsapo mayina a mabuku a Mbaibulo ngati magawo a mitu mu phunziro ili chifukwa akhala ngati mwininkhani ya zomwe tikuphunzira.

Nkhani yeniyeni imene imakhalapo mu mndandanda imatiuza za mwininkhani. Palinso magawo ena ang'onoang'ono amene amatiuzanso zokhuza mfundo yaikulu. Magawo a ang'onowa amafanana ndi mfundo yaikulu. Ndipo amapereka tsatanetsatane wa mfundo yaikulu.

Pali njira zambiri zopangira magawo kapena mndandanda. Choncho tasankha imodzi imene imagwiritsa ntchito manambala a chiroma polemba mitu yaikulu. Ngati manambala a chiromawa zimuwadziwa, mndandandanso waikidwa mu gawo la "kupitiliza kuphunzira" mu chaputalachi. Mfundo zing'onozing'ono mu magawowa zikuonekanso ndi zilembo koma zazikuluzikulu za Malembo. Ngati pali mfundo zina zopitilira pamenepa, mupeza kuti zaonetsedwa ndi manambala odziwika.

Phunzirani chitsanzo cha mndandanda uwu:

**Apa mumalembapo mutu waukulu**

I. Iyi ndi nambala ya Chiroma kuyimaira 1 ndipo ikusonyeza mfundo yoyamba yaikulu.

   A. Ichi ndi chilembo chachikulu choimira mfundo yotsatira ku mfundo yaikulu.

      1. Ngati pali mfundo ina yogwirizana ndi mfundo yotsatira ku mfundo yaikulu ndipo imaonetsedwa ngati nambala l.
      2. Ngati palinso mfundo ina yogwiriza ndi yotsatira ku mfundo yachiwiri imaonetsedwa nagti nambala 2.

   B. Pa mfundo zanga zazikulu ndingathe kukhala ndi mfundo zotsatira zingapo, choncho malembedwe ake amatsatira zilembo zomwe ndi zazikulu. Mfundozi zimachokera ku mfundo yaikulu.

II. Pofuna kulemba mfundo ina yaikulu koma yachiwiri, mumalembanso mu nambala ya Chiroma.

   A. Mfundo zotsatira zimatenganso mndandanda omwewo.

**KUTAMBASULA MAGAWO**

Ngati chitsanzo cha mmene mungatambasulire magawo mu phunziro ili, tasankha Aroma 12:1-2. Koyamba werengani mavesi:

> **Cifukwa cace ndikupemphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa, Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera.**

**Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire cimene ciri cifuno ca Mulungu, cabwino, ndi cokondweretsa, ndi cangwiro (Aroma 12:1-2).**

Umu ndi mmene mungapangire mndandanda kuchokera mu mavesiwa:

**Njira zopezera chifuniro cha Mulungu**

I. Perekani matupi anu ngati nsembe:
  A. Yopatulika.
  B. Yolandilika kwa Mulungu.

II. Musafanizidwe ndi makhalidwe a dziko
  A. Khalani osinthika
    1. Timasinthika pakukonzanso kwa malngaliro anthu.

III. Njira izi zingatithandize kuti tipeze chifuniro cha Mulungu chimene ndi:
  A. Chabwino.
  B. Cholandilika.
  C. Changwiro.

Mukhoza kuona kuti mndandandawu ndi chidule cha njira zopezera chifuniro cha Mulungu mu buku la Aroma 12:1-2.

Simungamalize mndandanda wophunzira chifuniro Mau a Mulungu. Mzinu Woyera amapitiliza kukupatsanibe kumvetsetsa kwachilendo kwa mawu pamene mufuna kuonjezera mndandanda wanu.

## MAYESO OZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.

2. Kodi mndandanda ndi chiyani?

3. Mupita pa mndandanda wa Genesis uphunziroli. Kodi mungathe kuwerenga ndi kumvetsetsa zomwe zikukambidwa pa mndandandawu?

4. Kodi mfundo zazikulu zimaonetsedwa bwanji ku mndandanda?

5. Kodi nanga mfundo zotsatira zimaonetsedwa bwanji?

**(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwa phunziroli)**

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Mfundo yomwe imatsatira ku mfundo yaikulu ndi pamene mumaonjera zinthu zina ndi kutambasula mndandanda mu phunziroli. Mwachitsanzo, onani mndandanda wa Buku la Danieli pa tsamba 174. Mfundo yoyamba yaikulu ikutchedwa "Chiyambi cha mmene zinalili: Zifukwa za kuchita bwino kwa Danieli" ndipo zikuchokera mu chaputala 1:1-21. Werengani mavesiwa ndi kupeza zifukwa zimene iye anachitira bwino. Lembani mndandanda wa mfundo zazing'ono pansi pa mfundo zazikulu.

2. Mndandanda wa manambala a Chiromawa ukuthandizani pamene mukupanga ndi kutambasula magawo anu:

| Nambala | nambala ya Chiroma. |
|---|---|
| 1 | I |
| 2 | II |
| 3 | III |
| 4 | IV |
| 5 | V |
| 6 | VI |
| 7 | VII |
| 8 | VIII |
| 9 | IX |
| 10 | X |
| 11 | XI |
| 12 | XII |
| 13 | XIII |
| 14 | XIV |
| 15 | XV |
| 16 | XVI |
| 17 | XVII |
| 18 | XVIII |
| 19 | XIX |
| 20 | XX |
| 30 | XXX |
| 40 | XL |
| 50 | L |
| 60 | LX |
| 70 | LXX |
| 80 | LXX |
| 90 | XC |
| 100 | C |

## CHIPANGANO CHAKALE

## CHIYAMBI CHA MABUKU A CHILAMULO

Machaputala ammbuyomu mwaphunzira kuti Baibulo ndi Mau a Mulungu olembedwa. Ndipo mwaphunzira kuti Baibulo lagawidwa mmagawo awiri a akulu amene ndi Chipangano Chakale ndi Chatsopano. Mwaphunziranso kuti pali magawo awiri a mabuku a Chipangano Chakale: Chilamulo, Mbiri, Ndakatulo ndi Uneneri. Mwaphunziranso magawo anayi a mabuku a Chipangano Chatsopano monga: Mauthenga abwino, Mbiri, Makalata ndi Uneneri.

Mu phunziro ili mwayamba ndi kafukufuku wa mabuku amene agawidwa monga mmene mwaphunzirila kuti pali mabuku okwana 39 mu Chipangano Chatsopano. Choncho tiyamba kafukufuku wathu ndi mabuku a chilamulo:

## MABUKU A CHILAMULO

Mabuku a Chilamulo analembedwa ndi Mose ndipo akhala kwa zaka zochuluka zokwana 600. Mabuku a Chilamulo amenewa alipo okwana asanu:

**Genesis**: Amafotokoza za chiyambi cha dziko, munthu, Sabata, ukwati, tchimo, nsembe, mitundu ndi ulamuliro. Komanso amakamba za anthu ofunika ngati Abraham, Isaki, Yakobo ndi Yofefe.

**Eksodo**: Amakamba za tsatanetsatane wa mmene Israyeli anakhalira mtundu mosogoleredwa ndi Mose. Israyeli ndi mtundu umene unawomboledwa mu nsinga za Aigupto ndipo anayenda kufikira phiri la Sinayi kumene analandira lamulo Mulungu.

**Levitiko**: Bukuli amagwiritsa ntchito pa chipembedzo cha Israyeli. Komanso limapereka malangizzo kwa atsogoleri a chipembedzo ndi za mmene munthu wochimwa angafikire kwa Mulungu wolungama. Limafanana ndi kubwera kwa Yesu Khristu monga mwana wa nkhosa ya Mulungu amene achotsa tchimo.

**Numeri**: Amafotokoza za mbiri ya Israyeli ndi ulendo wawo wa mchipululu kwa zaka zokwana 40 chifukwa cha kusamvera Mulungu. Dzina la bukuli likuchokera ku chiwerenero cha ana Aisrayeli pa ulendo wautaliwu.

**Deuteronomo**: Bukuli limakamba za za masiku omaliza a moyo wa Mose, ndi kuonanso kwa malamulo omwe anaprekedwa mu Eksodo ndi Levitiko.

## CHAPUTALA CHA 5

GENESIS

**ZOLINGA**:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Genesis.
- Kudziwa kumene buku la Genesis amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Genesis.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Genesis kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Genesis.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Mose

**OMWE AMAWALEMBERA:** Israyeli

**CHOLINGA:** Kufuna kusunga mbiri ya ana Asrayeli ndi nkhani ya chilengedwe, tchimo, chiombolo, ndi kukhala koyamba kwa Mulungu ndi munthu.

**VESI LOTSOGOLERA:** Genesis 3:15

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Dongosolo la Mulungu kuchokera pachiyambi ndi mitundu yonse ya anthu. Mulungu akuyamba zinthu zatsopano ndi anthu.

**ANTHU OMWE AKUTCHULIDWAMO:** Adamu, Hava, Abele, Enoki, Esau, Yakobo (Israyeli), Abrahamu, Isaki, Yosefe.

### MAGAWO

I. Mbiri ya munthu: 1:1-11:26

   A. Chilengedwe: 1:1-2:25
   B. Kuchiwa kwa munthu: 3:1-4:26
      l. Adamu ndi Hava: 3:1-24
      2. Kaini ndi Abele: 4:1-26
   C. Mbadwo wa anthu munthu atachimwa kufikira chigumula: 5:1-32

D. Chigumula: 6:1-9:29

l. Kuipa kwa munthu: 6:1-4
2. Chisankho cha Mulungu: 6:5-7
3. Nowa: 6:8-10
4. Mulungu alankhula ndi Nowa: 6:11-21
5. Yankho la Nowa: 6:22
6. Mulungu alankhula ndi Nowa: 7:1-4
7. Yankho la Nowa: 7:5-16
8. Moyo wa mu Chingalawa: 7:17-24
9. Kutuluka mu Chingalawa: 8:1-19
10. Pangano la Mulungu: 9:1-17
11. Mibadwo ya Nowa: 9:18-19
12. Machimo a banja la Nowa: 9:20-29

E. Kuchokera kuchigumula kufika kwa Abrahamu: 10:1-11:26

l. Mbadwo wa ana a Nowa: 10:1-32
2. Nsanja ya Babele: 11:1-9
3. Mibadwo ya Semu: 11:10-26
4. Mibadwo ya Tera: 11:27-32

II. Mbiri ya Makolo a Israyeli: 11:27-50:26

A. Abrahamu: 11:27-25:10

1. Kubadwa kwa Abrahamu ndi makolo ake: 11:26-30
2. Chikhalidwe cha moyo wake: 11:31-13:1
   (a) Kuchoka ku Uri kupita ku Harani: 11:31-32
   (b) Kuchoka ku Harani kupita ku Kanani: 12:1-9
   (c) Kupita ku Aigupto ndi kubwerera: 12:10-13:1
3. Abrahamu ndi Loti: 13:2-14:24
   (a) Mikangano ndi kugawana: 13:2-13
   (b) Lonjezo la Mulungu kwa Abrahamu: 13:14-18
   (c) Loti atengeka ndi mafumu a kummawa: 14:1-24
4. Pangano: 15:1-20
5. Ismayeli: 16:1-16
6. Mdulidwe: 17:1-27
7. Lonjezo la mwana wamamuna: 18:1-15
8. Sodomu ndi Gomora: 18:16-19:38
9. Abrahamu ayendera Abimeleki: 20:1-18
10. Isaki abadwa Ismayeli atulutsidwa: 21:1-21
11. Abrahamu ndi Abimeleki: 21:22-34
12. Pempho la nsembe ya Isaki: 22:1-19
13. Imfa ndi kuikidwa kwa Sarai: 23:1-20

14. Ukwati wa Isaki ndi Rabeka: 24:1-67
15. Abrahamu ndi Ketura: 25:1-6
16. Imfa ya Abrahamu ndi kuikidwa kwake 25:7-10

B. Isaki: 25:11-35:29

1. Kubadwa kwa Isaki: 21:1-8
2. Ukwati ndi Rebeka: 24
3. Isaki ndi ana ake: 25:19-35:29
4. Kukonzanso pangano: 26:1-5
5. Chinyengo cha Abimeleki: 26:6-33
6. Ukwati wa Yuditi ndi Basemati: 26:34-35
7. Isaki anyengedwa ndi Yakobo: 27:1-45
8. Yakobo athawira ku Harani: 27:46-28:5
9. Imfa ya Isaki: 35:27-29

C. Yakobo: 28:10-36:43

l. Kubadwa kwake: 25:19-26
2. Udani pakati pa Yakobo ndi Esau: 25:27-45
    (a) Ukulu pa kubadwa: 25:27-34
    (b) Madalitso: 27:1-45
3. Kuthawira ku Harani: 27:46-29:14
4. Ukwati wa Yakobo kwa Leya ndi Rakele: 29:15-30
5. Moyo wa ku Harani: 29:31-30:43
6. Kubwerera ku Kanani: 31:1-55
7. Kukonzekera kukumana ndi Esau: 32:1-23
8. Yakobo alimbana ndi Mngelo: 32:24-32
9. Mtendere ndi Esau: 33:1-17
10. Yakobo ndi banja lake ku Kanani: 33:18-45:28
11. Masiku otsiriza ndi imfa ya Yakobo: 46:1-50:14

D. Yosefe: 37:1-50:26

l. Masiku oyamba a Yosefe: 37:1-36
    (a) Mwinjiro: 37:1-4
    (b) Maloto ake: 37:5-11
    (c) Agulitsidwa ku ukapolo: 37:12-36
    (d) Tchimo la Yuda: 38:1-30
2. Yosefe ndi ukapolo: 39:1-40:23
    (a) Mnyumba mwa Potifala: 39:1-20
    (b) Kundende: 39:21-40:23
3. Yosefe akhala wachiwiri kwa olamulira: 41:1-45:28
    (a) Kukonzekera njala: 41:1-57
    (b) Yosefe ndi abale ake: 42:1-45:28
    (c) Yosefe ndi banja lake ku Aigupto: 46:1-50:21

(d) Imfa ya Yosefe: 50:22-26

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Genesis ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Genesis.

3. Kodi buku la Genesis amalembera kwa ndani?

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Genesis.

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Genesis.

**(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwenikweni kwa bukuli).**

## KUPITLIZA KUPHUNZIRA

1. Dzina loti "Genesis" limatanthauza chiyambi. Bukuli lili ndi chiyambi cha zinthu izi:
   -Dziko: 1:1-25
   -Munthu: 1:26-2
   -Tchimo: 3:1-7
   -Chipulumutso: 3:8-24
   -Mabanja: 4:1-15
   -Kusintha kwa zinthu: 4:16-9
   -Mitundu: 10:1-11:32
   -Mtundu wa Chiyuda: 12:50

2. Buku la Genesis lagawidwa mmagawo awiri a akulu: Machaputala 1-11 amakamba za zochitaka zazikulu zinayi. Machaputala 12-50 amakamba za anthu otchuka anayi.

3. Werengani machaputala 1-2 ndipo malizitsani tchatili:

| Tsiku | Chimene Mulungu analenga |
|---|---|
| 1 | |
| 2 | |
| 3 | |
| 4 | |
| 5 | |
| 6 | |
| 7 | |

4. Kodi muchaputala 3-9 mumaphunziramo chiyani zokhudza:
   -Machenjerero a mdani (Satana…njoka):________________________________________
   -Kuchimwa kwa Hava: ___________________________________________________
   -Zotsatira za tchimo kudziko lapansi: __________________________________________
   -Chiweruzo cha Mulungu ndi Chigumula:_______________________________________

5. Pezani anthu ofunikira anayi mu chaputala 12-50, ndipo muphunzire kuya kwa miyoyo yawo, ndi mmene moyo wanu wa uzimu umasinthira. Komanso phunzirani mawu oti "pangano" amene agwiritsidwa ntchito kochuluka mu gawoli.

## CHAPUTALA CHA 6

EKSODO

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula yemwe analeba buku la Eksodo.
- Kudziwa kumene buku la Eksodo amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Eksodo.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Eksodo kuchokera pamtima.
- Kutchula moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Eksodo.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA**: Mose

**OMWE AMAWALEMBERA**: Israyeli

**CHOLINGA**: Kudziwitsa za chipulumutso cha Israyeli kuchokera ku ukapolo ndi kutsindiki chifukwa chimene akukhala ngati mtundu.

**VESI LOTSOGOLERA**: Eksodo 12:13

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMUKI**: Chipulumutso chimachokera kwa Mwana wa nkhosa wa Mulungu, ndiye Yesu.

**ANTHU AMENE AKUTCHULIDWAMO**: Mose, Aroni, Farao, Miliyamu, Yetero.

### MAGAWO

I. Mtundu wa Israyeli ku Aigupto: 1:1-12:36

A. Ukapolo wa Aigupto: 1:1-22
B. Mulungu akonzekera chipulumutso: Mose: 2:1-4:31
C. Kucheza ndi Farao: 5:1-11:10
D. Pasaka: 12:1-30

E. Kupulumuka kwa Aigupto: 12:31-36

II. Israyeli muchipululu: 12:37-18:27

A. Ulendo ndi kutsatidwa ndi Aigupto: 12:37-15:21
B. Ulendo wa ku Sinai: 15:22-17:16
C. Kuyenderedwa ndi Yetero: 18:1-27

III. Israyeli pa Sinai: 19:1-40:38

A. Kupatsidwa chilamulo: 19:1-25
B. Malamulo otsogolera moyo: 19-22
C. Malamulo otsoglera makhalidwe ndi anthu ena: 22-23
D. Malamulo otsogolera moyo wachipembedzo: 24:1-31:18
E. Chihema: 24:12-40:38
   l. Akonza chihema: Malangizo a pa chihema ndi ansembe: 24:12-31:18
   2. Kuchedwa kwa chihema: Mwana wang'ombe ndi pangano latsopano: 32:1-34:35
   3. Amalidzitsa chihema: Kukwezedwa kwa chihema ndi malangizo a unsemba: 35:1-40:38

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Eksodo ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Eksodo.

3. Kodi buku la Eksodo amalembera kwa ndani?

4. Tchulani moyo ndi mfindo ya utumiki ya buku la Eksodo.

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku l Eksodo.

**(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli).**

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Mulungu adatumiza milili yokwana khumi kwa Aigupto ndi cholinga chofuna kumpanga kuti amasula ana Aisrayeli ku ukapolo:
   -Mwazi: 7:14-25
   -Achule: 8:1-15
   -Nsabwe: 8:16-19
   -Ntchentche: 8:20-32
   -Kalila: 9:1-7
   -Zilonda: 9:8-12
   -Matalala: 9:13-35
   -Dzombe: 10:1-20
   -Mdima: 10:21-29
   -Imfa: 11:1-10, 12:29-36

2. Pa Eksodo chaputala 20:1-17 akamba za malamulo khumi a Mulungu odziwika bwino.

3. Imodzi mwa nkhani yofunika kwambiri mu buku la Eksodo ndi dongosolo la chihema. Chinthunzi chimene chili patsamba lotsatilali chikuonetsa dongosolo limene Mulungu adampatsa Mose la malo oyera a kulambirapo.

   Chihema chinali chofunikira pa nkhani ya chipembedzo ndi kupereka nsembe kwa ana Aisrayeli. Komanso chihemachi chinali malo a uzimu. Izi zikutanthauza kuti gawo lililonse la chihemacho chinali chizindikiro za choonadi cha uzimu.

   Kunja kwake kwa chihemacho chinali 150 mulitali ndi 75 mulifupi. Ichi ndi chizindikiro cha dziko lapansi.

   Guwa lomwe amapserezapo nsembe linali 7 ndi theka ndi 4 ndi theka kutalika. Nsembe zimene amapsereza zinali chizindikiro cha nsembe ya Yesu pa machimo a dziko lapansi.

   Panali mbale yaikulu imene wansembe amagwiritsa ntchito kusamba mmanja ndi mapazi asanalowe mmalo oyera. Ichi ndi chizindikiro cha ubatizo wa akhristu.

   Malo oyera anali 30 ndi 15 kutalika kwake. Izi zikuimilira kuti mpingo ukuyenera kusiyanitsidwa ndi dziko ndipo kuti nsembe ya Yesu ndiye imene iyenera kulowa ndi ubatizo.

   Gome la mkate limaimira mgonero wa Ambuye.

Choilapo nyali chimapereka kuwala ku malo oyera. Ichi ndi chizindikiro cha Mau a Mulungu.

Gome la zofukiza anali malo amene amapserezerapo zofukiza. Fungo lokoma la utsi wa zofukiza limakwera kupita kwa Mulungu. Izi ndi chizindikiro cha mapemphero a oyera mtima.

Chophimba chinali chinsalu chimene chinali pakati pa malo oyera ndi malo oyeretsetsa. Zimaimira kusiyana pakati pa Mulungu ndi munthu.

Malo amene ndi oyeretsetsa anali 15 utali, otambasuka ndi a pamwamba. Chinali ngati bokosi langwiro kimirira kumwamba. Anali malo amene Mulungu amakhalapo.

Likasa la pangano linali mu bokosi la matabwa lomatidwa ndi golidi. Linali lokongola ndi a Kerubi awiri. Mu likasali ndi mmene munali Malamulo khuma Mulungu amene amaimira boma la Mulungu, mbale ya mana imene imaimira thandizo la Mulungu, ndi ndodo la Aroni imene imawakumbutsa za mphamvu ya Mulungu pa iwo. Pa chaka kamodzi mkulu wansembe amawaza mwazi pa mwamba pa likasa. Mwazi umene umaimira mwazi wa Yesu umene timatsukidwa nawo machimo athu.

**Masiku opatulika**

Werengani mabukuwa mbali imodzi ndipo malizitsani tchatichi. Chitsanzo choyamba chaperekedwa kuti mutsatire. Awa ndi masiku opatulika amene Mulungu anawasankha kuti mtundu wa Israyeli udzisunga.

| **Ndime** | **Masiku oyera** | **Tsiku** | **Cholinga chosungira** |
|---|---|---|---|
| Levitiko 23:3<br>Eksodo 20:8-ll<br>Deuteronomo 5:12-15 | Sabata | Tsiku Lachisanu ndi chiwiri | Kupumula ku ntchito; kulambira |
| Levitiko 23:5<br>Numeri 28:16<br>Deuteronomo 16:1-2 | Pasaka | 1/14 | |
| Levitiko 23:6-8<br>Numeri 28:17-25<br>Deuteronomo 16:3-8 | Mkate wopanda chotupitsa | 1/15-21 | |

| | | |
|---|---|---|
| Levitiko 23:9-14<br>Eksodo 23:16<br>Numeri 28:26-31 | Zipatso zoyamba | 1/16 |
| Levitiko 23:15-22<br>Eksodo 34:22<br>Deuteronomo 16:9-12 | Pentekosite | 3/6 |
| Levitiko 23:23-25<br>Numeri 29:1-6 | Malipenga | 7/1 |
| Levitiko 23:26-32<br>Levitiko 16<br>Numeri 29:7-11 | Tsiku la nsembe | 7/10 |
| Levitiko 23:33-44<br>Numeri 29:12-40<br>Deuteronomo 16:13-15 | Chigono | 7/15-21 |
| Levitiko 25:1-7<br>Eksodo 23:10-11 | Chaka cha sabata | Chaka chilichonse cha 7 |
| Levitiko 25:8-55 | Chisangalalo | Chaka chilichonse cha 50 |

## CHAPUTALA CHA 7

LEVITIKO

**ZOLINGA**:

Pakutha pa chaputala ichi muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Levitiko.
- Kudziwa kumene buku la Levitiko amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Levitiko.
- Kulemba vesi lotsogolera la buku la Levitiko.
- Kutchula moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Levitiko.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Mose

**OMWE AMAWALEMBERA:** Israyeli

**CHOLINGA:** kuwaonetsera a Israyeli za mmene angakhalire mtundu woyera pa chiyanjano ndi Mulungu ndi kuwakonzekeretsa kutalikitsa dongosolo la Mulungu loombola mitundu yonse ya anthu.

**VESI LOTSOGOLERA:** Levitiko 20:7

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Mulungu amafuna chiyero kwa anthu ake.

**ANTHU OMWE AKUTCHULIDWAMO:** Mose, Aroni

### MAGAWO

I. Malamulo okhuza nsembe: 1:1-7:38
   A. Mawu oyamba: 1:1-2
   B. Nsembe yopsereza: 1:3-17
   C. Nsembe ya chakudya: 2:1-16
   D. Nsembe ya mtendere: 3:1-17
   E. Nsembe ya uchimo: 4:1-5:13
   F. Nsembe yolakwitsa: 5:14-17

II. Laws and incidents concerning the priests: 8-10

A. Malangizo okhuzana kudzipatula: 8:1-9:24
B. Chilango pa kulakwira: 10:1-20

III. Malamulo pa kudziyeretsa: 11:1-15:33

A. Chakudya choyera ndi chodetsedwa: 11:1-47
B. Chiyeretso mwana akabadwa: 12:1-8
C. Khate: 13:1-14:57
D. kudetsedwa pa kugonana ndi mayeretso ake: 15:1-33

IV. Tsiku la nsembe ya uchimo: 16:1-34

A. Chikonzero cha Aroni: 16:1-10
B. Nsembe ya uchimo ya ansembe: 16:11-14
C. Nsembe ya uchimo ya anthu: 16:15-19
D. Chotetezera: 16:20-22
E. Kumaliza nsembe: 16:23-28
F. Chilengezo cha tsiku: 16:29-34

V. Chizindikiro cha chiyero: 17:1-27:34

A. Zoletsedwa: 17:1-22:33
    1. Chiyero pa anthu: 17:1-20:27
    2. Chiyero cha ansembe: 21:1-22:33
B. Nyengo za chikondwerero: 23:1-44
    1. Sabata: 23:1-3
    2. Pasaka ndi mkate wopanda chotupitsa: 23:4-14
    3. Nyengo ya sabata, pentekosite: 23:15-22
    4. Nyengo ya malipenga: 23:23-25
    5. Tsiku la nsembe ya machimo: 23:25-32
    6. Madyerero a misasa: 23:33-44
C. Zizindikiro za chipembedzo: 24:1-23
D. Chaka cha sabata ndi chopumula: 25:1-26:2
E. Malonjezo ndi machenjezo: 26:3-46
    1. Kufunika kwa ubale wabwino ndi Mulungu: 26:1-2
    2. Madalitso pakumvera Mulungu: 26:1-2
    3. Zilango pa kusamvera Mulungu: 26:14-39
    4. Kukhulupilika kwa Mulungu pa pangano lake: 26:40-45
    5. Mawu oomba mkota: 26:46

F. Zowinda ndi zakhumi: 27:1-34

1. Zowinda kwa anthu: 27:2-8
2. Zowinda za nyama zoweta: 27:9-1.
3. Zowinda za nyumba ndi minda: 27:14-25
4. Chakhumi: 27:30-33
    (a) Zoyamba za nyama: 27:26-27
    (b) Zinthu zopatulika: 27:28-29
    (c) Chakhumi: 27:30-33

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Levitiko ndi ndani?

2. Cholinga chimene amalembera buku la Levitiko.

3. Kodi buku la Levitiko amalembera kwa ndani?

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Levitiko.

5. Lembani vesi lotsogolera la buku la Levitiko.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka mumapeto kwenikweni kwa bukuli).

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Werengani mawu oti “chiyero” mu buku la Levitiko. Mawuwa agwiritsidwa ntchito kopitilira ka 100. Mawu enanso ofunikira ndi “nsembe” amene agwiritsidwa ntchito ka 42, mawu oti “wansembe” agwiritsidwa ntchito ka 189 ndipo mawu oti mwazi agwiritsidwa ntchito ka 86.

2. Muyeso weniweni wa chiyero walongosoledwa mu Levitiko mbali zonse ziwiri, kupita mmwamba ndi kupita mbali. Kupita mmwamba kukupezeka pa Levitiko machaputala 1-10 (“ndine woyera”) ndi kupita mbali kukupezeka pa Levitiko machaputala 11-27 (“khalani woyera”).

Ndine Woyera
machaputala 1-10
□

□
Muzikhala oyera
Machaputala11-27

3. Pali nsembe zisanu zosiyana zimene zikupezeka mu Levitiko. Zitatu zoyamba za nsembezi zinaikidwa kuti zisunge chiyanjano ndi Mulungu. Ziwiri zomalizira zinandi cholinga chofuna kubwenzeretsa chiyanjano chimene chinaonongeka.

4. Nambala ya chisanu ndi chiwiri (7) ndi yofunikira kwambiri mu buku la Levitiko:
   -Tsiku la nambala 7 la sabata.
   -Mwazi umakhetsedwa ka 7 mu chihema.
   -Chaka cha 7 chinali chaka cha sabata.
   -Chaka cha nambala 7 cha sabata chimatsatana ndi chaka cha chisangalalo
   -Mwezi wa nambala 7 unali woyera, ndipo umakhala ndi maphwando atatu.
   -Panali masabata 7 pakati pa Pasaka ndi Pentekosite.
   -Phwando la Pasaka limatha tsiku la nambala 7.
   -Munthu wodetsedwa amapatulidwa kwa masiku 7.
   -Phwando la kuchihema limatha tsiku la nambala 7.
   -Pa tsiku la Pasaka, ana ankhosa okwana 14 (2*7) amaperekedwa nsembe tsiku ndi tsiku.
   -Pa tsiku la pentekosite, ana ankhosa okwana 7 amaperekedwa nsembe.
   -Pa phwando la kuchihema ana ankhosa okwana 14 amaperekedwa nsembe.

## CHAPUTALA CHA 8

NUMERI

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:
- Kutchula wolemba buku la Numeri.
- Kudziwa kumene amalembera buku la Numeri.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Numeri.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Numeri kuchokera pamtima
- Kutchula moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Numeri.

**MAWU OYAMBA**

**WOLEMBA:** Mose

**OMWE AMAWALEMBERA:** Israyeli

**CHOLINGA:** Kulemba za zimene anakumana nazo pa ulendo wa mchipululu zimene zimaonetsera kugonjetsedwa kwa mkhristu.

**VESI LOTSOGOLERA:** Numeri 32:23

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Mulungu sasangalatsidwa ndi chinachilichonse kupatula kumumvera.

**ANTHU OMWE AKUTCHULIDWAMO:** Mose, Kora, Balamu, Aroni, Miriyamu, Joshua, Kalebe

**MAGAWO**

I. Kukonzekera kuchoka ku Sinai: 1:1-10:10

A. Anthu awerengedwa: 1:1-54
B. Malo okhala akonzedwa: 2:1-34
C. Ansembe ndi a Levi alangizidwa: 3:1-4:49
D. Anthu atetezedwa: 5:1-31
E. Chowinda cha Mnaziri: 6:1-27
F. Mphatso ya mwana wamfumu: 7:1-89
G. Kuwala kwa nyali ya chihema: 8:1-4

H. Kuyeretsa kwa a Levi: 8:5-26
I. Kuchita Pasaka: 9:1-14
J. Kutchinjiriza malo okhala: 9:15-23
K. Kuitana nsonkhano ndi kupita ku malo okhala: 10:1-10

II. Ulendo wochoka ku phiri la Sinai kupita ku Kadeshi- Baneya: 10:11-12:15

A. Kuyambapo ulendo: 10:11-28
B. Hobabu akana ntchito: 10:29-32
C. Mtambo upitilira: 10:34-36
D. Chiweruzo cha moto: 11:1-3
E. Maganizo odandaula: 11:4-9
F. Mneneri osokonezedwa: 11:10-15
G. Chakudya chakupha: 11:31-34
H. Mlongo wosautsidwa: 12:1-15

III. Israyeli ku Kadeshi-Baneya: 13:1-14:45

A. Kukazonda dziko: 13:1-25
B. Zimene anaona kudziko ndi zomwe anachita: 13:26-14:10
C. Chiweruzo cha Mulungu: 14:11-34

IV. Zochitika mu ulendo wa mchipululu: 20:1-35:34

A. Kumponya mwala wophwanya Sabata: 15:32-36
B. Kugalukira kwa Kora: 16:1-32
C. Kuphuka kwa ndodo ya Aroni: 17:1-13
D. Malangizo kwa Aroni: 18:1-19:22
E. Imfa ya Miriyamu: 20:1
F. Tchimo la Mose: 20:1-13
G. Pempho likanidwa: 20:14-22
H. Imfa ya Aroni: 20:23-29
I. Njoka pakati pa anthu: 21:5-9
J. Mneneri otayika: 22:1-24:25
K. Wanembe wokonda: 25:1-18
L. Malangizo owonjezera: 26:1-31:54
M. Kugawa madera a kummawa kwa Yorodani: 32:1-42
N. Zokhuza ulendo wa ku Aigupto: 33:1-56
O. Malangizo asanalowe ku dziko la Kanani: 34:1-36:13

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Numeri ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Numeri.

3. Kodi buku la Numeri amalembera kwa ndani?

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Numeri.

5. Lembani Vesi Lotsogolera ya buku la Numeri.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwa bukuli)

**KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Kusintha kwa utsogoleri wa Israyeli kwachitika mu Numeri. Yoswa akulowa mmalo mwa Mose ngati mtsogoleri wa dziko ndipo Eleazara alowa mmalo mwa Yoswa ngati mtsogoleri wa chipembedzo. Onani Numeri 27:15-23 ndi 20:23-29.

2. Imfa komanso kuukitsidwa kwa Yesu kukupezeka mu Numeri ndi njoka ndi ndodo: 21:5-9; 17:8

3. Tchatili likuonetsa zotsatira za "ziwerengero" ziwiri ya Israyeli:

| **Fuko** | **Chiwerengero choyamba** | **Chiwerengero chachiwiri** |
|---|---|---|
| Rubeni | 46,500 | 43,730 |
| Simeon | 59,300 | 22,200 |
| Gadi | 45,650 | 40,500 |
| Yuda | 74,600 | 76,500 |
| Isakara | 54,400 | 64,300 |
| Zebuloni | 57,400 | 60,500 |
| Efraimu | 40,500 | 32,500 |
| Manase | 32,200 | 52,700 |
| Benjamini | 35,400 | 45,600 |
| Dani | 62,700 | 64,400 |
| Aseri | 41,500 | 53,400 |
| Nafitali | 53,400 | 45,400 |
| **Zonse** | **603,550** | **601,730** |

# CHAPUTALA CHA 9

DEUTERONOMO

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kuthcula yemwe analemmba buku la Deuterenomo.
- Kudziwa komwe wolemba buku la Deuterenomo amalembera.
- Kutchula cholinga chimene wolemba bukun la Deuterenomo amalembera.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Deuteronomo kuchokera pamtima.
- Kutchula moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Deuterpnomo.

## MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Mose

**OMWE AMAWALEMBARA:** Israyeli

**CHOLINGA:** Kuperekanso lamulu kachiwiri ku mbadwo watsopano wa ana Aisrayeli umene unabadwa kuchokera pa phiri la Sinai.

**VESI LOTSOGOLERA:** Deuteronomo 6:4-5

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Kumvera kumabweretsa madalitso. Kusamvera kumabweretsa chiweruzo.

**ANTHU OMWE AKUTCHULIDWAMO:** Mose, Yoswa, Balamu, Amaleki, Miliyamu.

## MAGAWO

I. Ulaliki woyamba wa Mose: Mbiri 1:1-4

A. Chiyambi cha mbiri: 1:1-5
B. Kuonanso mmene anayendera kuchoka ku Horebi kufika ku Moabu: 1:6-3:29
C. Adandaulira mbadwo watsopano kusunga malamulo: 4:1-40
D. Dongosolo la kusankha mizinda yozitetedzera: 4:41-43
E. Chidule cha chilamulo cha Mose: 4:44-49

II. Ulaliki wachiwiri wa Mose: Lamulo 5:1-26:19

A. Malamulo khumi abwerezedwa: 5:7-21

B. Achenjeza za chigololo (23:17); zipembedzo zina (7:1-5); ndi za ufiti: 18:9-14
C. Mose alongosola za kanani: 8:7-8
D. Abwerezanso za kukumana kwake ndi Mulungu pa phiri la Sinai: 9:9-21
E. Aqakumnutsa za lamulo pa chuma kwa Mulungu: 26:1-19
F. Malamulo okhuzana ndi zovala (22:50; kulelana mmbanja (24:1-4); mbali ya akazi (21:10-17; 22:13-20); ndi zokhuza kunkhondo (20:1-20) aperekedwa.
G. Anena mwachidule za dongosolo la Mulungu: 6:23

III. Ulaliki wachitatu wa Mose: Onenera: 27:1-30:20

A. Kulembedwa kwa malamulo pa mwala, madalitso ndi natemberero: 27:1-26
B. Kulosera madalitso ndi matemberero: 28:1-68
C. Awadandaulira za chiyero: 29:1-30:20

IV. Za mbiri yomaliza: 31:1-34:12

A. Mawu a Mose omaliza ndi zakusankhidwa kwa Yoswa: 31:1-30
B. Nyimbo ya Mose ndi chilimbikitso: 32:1-47
C. Mawu a Mulungu omaliza kwa Mose: 32:48-52
D. Mose apereka mdalitso kwa mafuko: 33:1-29
E. Kumwalira ndi kuikidwa kwa Mose: 34:1-12

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Deuteronomo ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Deuteronomo.

3. Kodi buku la Deuteronomo amalembera kwa ndani?

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya utumiki ya buku la Deuteronomo.

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Deuteronomo.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwekweni kwa bukuli).

**KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Yesu adagwiritsapo ntchito mawu ochokera mu buku la Deuteronomo munthawi imene amayesedwa ndi Satana. Fanizirani Mateyu 4:4 ndi Deuteronomo 8:3; Mateyu 4:7 ndi Deuteronomo 6:16; ndi Mateyu 4:10 ndi Deuteronomo 6:13.

2. Buku la Deuteronomo ndi buku la Mbiri, koma lili ndi ma uneneri anayi amene ndi ofunikira kwambiri:
   -Kulowa kwa Israyeli ku Kanani pa utsogoleri wa Yoswa: 7:2; 9:1-3; 31:3,5
   -Tchimo la Israyeli ku Kanani: 31:16-18, 20, 29
   -Ukapolo wochoka ku Kanani: 4:26-28; 7:4; 8:19-20; 28:36,41,49,50,53,64
   -Kubwerera kwa Israyeli kupita ku Kanani: 4:29; 30:1-3,10

3. Werengani mawu awa "chita," "sunga," ndi "samalitsa." Mawuwa akupezeka kokwana ka 177 mu buku la Deuteronomo.

4. Mawu ena ofunikira mu buku limeneli ndi "kumbukira." Mawuwanso abwerezedwa kochuluka mu bukuli. Ana Aisrayeli amauzidwa kuti akumbukire:
   -Za kuperekedwa kwa Lamulo: 4:9-10
   -Pangano: 4:23
   -Ukapolo wakale: 5:15
   -Chipulumutso chawo: 7:18
   -Utsogoleri wa Mulungu ndi thandizo lake: 8:2-6
   -Machimo akale: 9:7
   -Ziweruzo za Mulungu: 24:9
   -Masiku akale: 32:7

5. Buku la Deuteronomo lili ndi nyimbo imene ikhoza kuyimba mu nthawi ya chisautso chachikulu. Fananitsani Deuteronomo 31:30-32:45 ndi Chibvumbulutso 15:3-4.

6. Mutu waukulu wa buku la Deuteronomo ndi kufunikira kwake kwa mawu a Mulungu. Onani 4:1, 2, 7, 9; 6:7-9; 11:18-21; 27:1-4; 30:11-14; 31:11-12; 32:46-47.

7. Pa zochitika mu mbiri za Levitiko, werengani Numeri 21:21-22:1 ndi Deuteronomo 1:1-5.

## MAWU OYAMBA A MABUKU A MBIRI

**Yoswa**: Amafokoza zambiri za mmene Yoswa amene analowa mmalo mwa Mose, ndi kutsogolera Israyeli kudziko la malonjezo la Kanani. Limakambanso za kumemeza kwa asilikali ndi kugawana kwa malo kwa anthu.

**Oweruza**: Kubwerera mmbuyo kwa Israyeli atangofa Yoswa. Bukuli limakamba za nkhani yomvetsa chisoni ya kubwereza kwa machimo ndi oweruza amene Mulungu anawatuma kuti apulumutse Israyeli kwa adani awo.

**Rute:** Iyi ndi nkhani ya Rute, mkazi wamitundu wa ku moabu, amene anasankha kutumikira Mulungu wa Israyeli. Kumapeto adakhala kholo la Davide.

**I Samueli**: Bukuli limatsindika za anthu atatu: Samueli, amene anali woweruza womaliza wa Israyeli; Sauli amene anali mfumu yoyamba ya Israyeli, ndi Dvide amene analowa mmalo mwa Sauli.

**II Samueli:** Amafotokoza za zaka 40 za ulemerero wa ulamuliro wa Davide.

**I Mafumu**: Bukuli amafotokoza za ufumu wa mfumu Solomoni ndi mafumu a ufumu wogawanika a kumpoto kumene Ahabu amalamulira ndi kumwera kumene Yehosafati amalamulira.

**II Mafumu**: Kugwa kotsiriza kwa Israyeli ndi Yuda kukupezeka mbukuli. Anthu a Mulungu anagwa mu uchimo wakuya.

**Ezara**: Bukuli limafotokoza za kubwerera ka Ayuda kuchokera ku ukapolo wa Babulo.

**Nehamiya**: Limatsindika za kumangidwanso kwa chipata cha Yerusalemu pansi pa utsogoleri wa Nehemiya. Ntchitoyi inayamba patatha zaka 14 za kubwerera kwa Ezara ndi anthu.

**Estere:** Bukuli limafotokoza za chipulumutso cha Ayuda kudzera mwa Estere ndi Modekayi.

## CHAPUTALA CHA 10

YOSWA

**ZOLINGA:**
Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Yoswa.
- Kudziwa kumene buku la Yoswa amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Yoswa.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Yoswa kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Yoswa.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Yoswa

**OMWE AMAWALEMBERA**: Israyeli

**CHOLINGA:** Kulemba za mbiri ya kugonjetsa Kanani.

**VESI LOTSOGOLERA:** Yoswa 24:15

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Palibe chigonjetso cha kupambana ku uzimu kapena cha makhalidwe popandapo kuchita nkhondo.

**ANTHU OMWE AKUTCHULIDWAMO:** Yoswa, Rahabe, Kalebe, Akani, Balamu, Eleazara.

### MAGAWO

I. Kulowa mdzikomo: 1:1-5:15

- A. Yoswa atumidwa: 1:1-9
- B. Kukonzekera kuwoloka Yorodano: 1:10-2:24
- C. Awoloka Yorodano: 3:1-4:24
- D. Akhala ku Giligala: 5:1-15

II. Kukhala mdzikomo: 6:1-12:24

- A. Yeriko ndi Ai atengedwa: 6:1-8:29
- B. Guwa la Yoswa: 8:30-35
- C. Awalandira a Gibeoni: 9:1-27

D. Agonjetsedwa a Kanani a kummawa: 10:1-43
E. Agonetsedwa a Kanani a kumpoto: 11:1-15
F. Chidule cha chigonjetso: 11:16-12:24

III. Kukhala mdzikomo: 13:1-22:34
A. Yoswa alangizidwa: 13:1-7
B. Mafuko a kummawa apatsidwa ntchito: 13:8-33
C. Mafuko a kumadzulo apatsidwa ntchito: 14:1-19:51
D. Mizinda yopulumukirapo: 20:1-9
E. Mizinda ya Levitiko: 21:1-45
F. Mafuko a kummawa atumidwa kwawo: 22:1-34

IV. Mawu otsiriza a Yoswa ndi kumwaalira kwake: 23:1-24:33
A. Awakumbutsa za ubwino wa Mulungu: 23:3-10
B. Awachenjedza za kusamvera: 23:11-13
C. Abwereza za mbiri yawo: 24:1-13
D. Awatsikizira kuti atumikire Mulungu: 24:14-18
E. Atsiriza buku limene lili ndi dzina llake: 24:26-28
F. Amwalira ndi kupita kumwamba: 24:29-33

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Yoswa ndi ndani?

___

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Yoswa.

___

___

3. Kodi wolemba buku la Yoswa amalembera kwa ndani?

___

___

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Yoswa.

___

___

___

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Yoswa kuchokera pamtima.

___

___

___

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli).

**KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

Buku la Yoswa likhoza kusiyanitsidwa ndi buku la Eksodo. Mu Eksodo, Mulungu akulekanitsa madzi a mnyanja yofiira ndi cholinga chofuna kuwombola anthu ake ku dziko la ukapolo la Aigupto. Mu Yoswa, Mulungu akulekanitsa madzi a mumtsinje wa Yorodano ndi cholinga choowabweretsa anthu ake ku dziko la Kanani, dziko la madalitso.

Mose analankhula za mmabuku onsewa mwachidule pa Deuteronomo 6:23.

"Ndipo anatitulutsa komweko, kuti atilowetse."

## CHAPUTALA CHA 11

OWERUZA

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputala ichi muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Oweruza.
- Kudziwa kumene buku la Oweruza amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Oweruza.
- Kulemba Vesi Lalikulu la buku la Oweruza kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Oweruza.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Samueli

**OMWE AMAWALEMBERA:** Israyeli

**CHOLINGA:** Kulemba mbiri ya ulamuliro wa Oweruza imene inachitika kumapeto kwa buku la Yoswa.

**VESI LOTSOGOLERI:** Oweruza 17:6

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Pamakhala chilango cha umulungu cha ana a Mulungu chifukwa cha tchimo ndi cholinga chofuna kuwapulumutsa.

**ANTHU OMWE AKUTCHULIDWAMO:** Oweruza (Onani mndandanda uli mmusimu).

### MAGAWO

I. Mawu oyamba mu nthawi ya oweruza: 1:1-2:5

A. Mmene unalili utsogoleri wawo mu nthawi ya Yoswa kufikira nthawi ya oweruza: 1:1-36
B. Mmene chinalili chippembedzo chawo kuchokera mu nthawi ya Yoswa kufikira oweruza: 2:1-5

II. Nthawi ya oweruza: 2:6-16:31

A. Chidule cha mmene chinalili chipembedzo chawo: 2:6-3:6
B. Mndandanda wa oweruza: 3:7-16:31
    l. Otiniyeli wa Yuda: 3:7-11
    2. Ehudi wa Benjamini: 3:12-30
    3. Samagara: 3:31
    4. Debora wa Efraimu ndi Baraki wa Nafitali: 4:1-5:31
    5. Gideoni wa Manase and Abimeleki: 6:1-9:57
    6. Tola wa Isakara: 10:1-2
    7. Yairi wa Gileadi: 10:3-5
    8. Yefita wa Gileadi: 10:6-12:7
    9. Ibrani wa Zebuloni: 12:8-10
    10. Eloni wa Zebuloni: 12:11-12
    11. Abidoni wa Efraimu: 12:13-15
    12. Samsoni wa fuko la Dani: 13:1-16:31

III. Za mu mbiri yotsiriza: 17:1-21:25
A. Fano la Mika ndi ana a Dani: 17:1-18:31
    1. Mika ndi wansembe wake: 17:1-13
    2. Ana a Dani apembedza mafano: 18:1-31
B. Mlandu wa Benjamini ku Gibeya ndi chilango chake: 19:1-21:25
    1. Kuima ku Gibeya: 19:1-15
    2. Mlandu: 19:16-27
    3. Yankho la Alevi: 19:28-29
    4. Mkwiyo wa a Israyeli: 19:30-20:11
    5. Nkhondo zitatu: 20:12-21:25

**MAYESO ODZIYETSA NOKHA**

1. Kodi analemba buku la Oweruza ndi ndani?

______________________________________________

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Oweruza.

______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________

3. Kodi buku la Oweruza amalembera kwa ndani?

______________________________________________
______________________________________________

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Oweruza.

______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Oweruza.

______________________________________________
______________________________________________

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli).

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Buku la Oweruza ndi losiyana ndi buku la Yoswa.

   Yoswa amakamba za chigonjetso, ufulu, kupita chitsogolo, masomphenya a uzimu, chimwemwe, mphamvu, ndi umodzi pakati pa mafuko ndi utsogoleri wamphamvu.

   Pamene Oweruza amakamba za kugonjetsedwa, ukapolo, kusakhulupirira, kugawikana, kusamvera, za kudziko, chisoni, chifooko, ndi kugawanika pakati pa mafuko.

2. Buku la Agalatiya limakamba mwachidule za mabuku a Yoswa ndi Oweruza. Agalatiya 5:22-26 amafotokoza za Yoswa, ndipo 5:17-21 amafokoza za Oweruza.

3. Buku la Oweruza ndi chitsanzo chenicheni cha buku la Hoseya 8:7 ndi Agalatiya 6:7.

4. Oweruza 17:6 amaomba mkoti za nyengo ya Israyeli mu nthawi ya Oweruza.

5. Nkhani ya munthu wamphamvu mu mbiri ikupezeka mu Oweruza 15.

6. Werengani nkhani ya Msirikali amene anaphedwa chifukwa chosatchula bwino mawu: Oweruza 12.

7. Mulungu anagwiritsa ntchito njira zosazolowereka mu buku la Oweruza. Anagwiritsa ntchito:
   -Mtoso wang’ombe: 3:31
   -Chichili: 4:21
   -Malipenga: 7:20
   -Mbiya: 7:20
   - Miuni: 7:20
   -Mwala wamphero: 9:53
   -Chibwano cha bulu: 15:15

8. Malizitsani tchatili pamene mukuwerenga za kubwereza kwa zochitika mu buku la Oweruza. Gawo loyamba ndi chitsanzo chanu choti mutsatire.

**Nthawi ya Oweruza**

Nthawi yawo **3:7-11 3:12-30 4:1-5:31 6:1-8:32 8:33-10:5 10:6-12:15 13:1-16:31**

---

T Mafano
C
H
I
M
O

---

U
T
U Zaka 8 za ufumu wa Mesopotamiya
M
I
K
I

---

P
E
M
B Kufuulira kwa Ambuye
E
D
Z
E
R
O

---

C
H
I
P
U
L
U
M
U

T Otiniyeli wa nkhondo
S
O

---

N
T
H
A
W
I

Y
A Zaka 40

C
H
E
T
E

**Oweruza a Israyeli**

| **Name** | **Zaka za Yesu asanabwere** | **Number of Years** |
|---|---|---|
| Otiniyeli | 1400-1360 | 40 |
| Ehudi | 1360-1280 | 80 |
| Shamagara | 1280 | 1 |
| Debora | 1280-1240 | 40 |
| Gideon i | 1240-1200 | 40 |
| Abimeleki | 1200-1197 | 3 |
| Tola | 1197-1174 | 23 |
| Yairi | 1174-1152 | 22 |
| Yefita | 1152-1146 | 6 |
| Ibrani | 1146-1138 | 8 |
| Eloni | 1138-1128 | 10 |
| Abidoni | 1128-1121 | 7 |
| Samsoni | 1121-1101 | 20 |

## CHAPUTALA CHA 12

RUTE

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Rute.
- Kudziwa kumene buku la Rute amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Rute.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Rute kuchokera pamtima.
- Kutchula moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Rute.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Osadziwika

**OMWE AMAWALEMBERA:** Israyeli

**CHOLINGA:** Linalembedwa ngati gawo limodzi la mbiri ya Israyeli poonetsera chidwi cha Mulungu pa anthu ake. Likuonetseranso za ubale wa momboli ndati Yesu Khristu.

**VESI LOTSOGOLERA:** Rute 1:16-17

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Mulungu amasintha zowawa kukhala mdalitso.

**ANTHU OMWE AKUTCHULIDWAMO:** Naomi (Mara), Elimeleki, Maloni, Kiliyoni, Oripa, Boazi, Momboli wosadziwika.

### MAGAWO

I. Moabu: 1:1-5
    A. Ulendo wa ku Moabu: 1:1-2
        1. Mmene nkhani inalili: 1:1
        2. Chifukwa chopitira ku Moabu: 1:1
        3. Chiyambi cha ku banja: 1:2
    B. Tsoka la ku Moabu: 1:3-5
        1. Mamuna wa Naomi amwalira: 1:3
        2. Ana a Naomi akwatira 1:4
        3. Ana a Naomi amwalira: 1:5

II. Kubwerera ku Betelehemu: 1:6-18

A. Naomi aganiza zobwerera ndi kuwauza apongozi ake kuti abwerere kwa anthu awo: 1:6-9
B. Pempho lawo loti akhale: 1:10
C. Yankho la Naomi: 1:11-13
D. Pempho lawo: 1:14
E. Chilengezo la Rute: 1:16-18
    1. Samafuna kumusiya Naomi: 1:16
    2. Adzapita kumene Naomi apita: 1:16
    3. Adzakhala kumene Naomi akhala: 1:16
    4. Anthu a Naomi adzakhalanso anthu ake: 1:16
    5. Mulungu wa Naomi adzakhalanso Mulungu wake: 1:16
    6. Adzakhala wokhulupirika kufikira imfa: 1:17

III. Kufika ku Betelehemu: 1:19-22

A. Mzinda uwalandira: 1:19
B. Yankho la Naomi: 1:20-21
C. Nthawi yobwerera: 1:22

IV. Rute mmunda mwa Boazi: 2:1-17

A. Kukunkha mmunda: 2:1-3
B. Boazi amzindikira: 2:4-13
C. Nthawi ya kudya ndi Boazi: 2:14
D. Kukunkha zabwino: 2:15-17
E. Kubwerera kuchoka kumunda: 2:18-23

V. Dongosolo lapaderadero: 3:1-18

A. Dongosolo la Naomi: 3:1-5
B. Zotsatira: 3:6-15
C. Kubwerera kwa Naomi: 3:16-18

VI. Chiombolo: 4:1-13

A. Mmene zinakhalira: 4:1-12
B. Ubale wa pakati pa Rute ndi Boazi: 4:13-17
C. Mdalitso: 4:14-16

VII. Mndandanda wa makolo a Davide: 4:17-22

**MAYESO ODZIYETSA NOKHA**

1. Kodi analemba buku la Rute ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Rute.

3. Kodi buku la Rute amalembera kwa ndani?

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Rute.

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Rute kuchokera pamtima.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli).

**KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Pofuna kudziwa zambiri mu pa zinthu zimene zinachitika mu nthawi ya Rute, onani buku la Oweruza.

2. Rute ndi mmodzi mwa akazi anayi amene akutchulidwa mu mndandanda wa makolo a Yesu kuthupi mu Mateyu 1. Ena ndi monga Tamara Mateyu 1:3, Rahabe, 1:5 ndi Betishaba, 1:6.

3. Malamulo a mbale woombola akupezeka mu Deuteronomo 25:5-10. Lamulo la katundu amene woombolayo akuyenera naye akupezeka ku Levitiko 25:23.
   Wachibale woombolayo amayenera kukhala ndi zomuyenereza monga:
   -Amayenera kukhala wachibale ndi munthu woomboledwayo
   -Amayenera kukhala wokonzekadi kuombola
   -Amayenera kukhala ndi kithekera koombola.
   -Amayenera kukhala mfulu mwa yekha.
   -Amayenera kukhala ndi dipo loombolera.
   Boazi anali ndi zoyenera zonsezi zoombolera Rute. Yesu anali ndi zonse zoombola anthu ochimwa.
4. Werengani chikhalidwe cha Rute:
   -Wokonda, wodzipereka: 1:16-17
   -Okhazikika: 1:18
   -Odzichepetsa: 2:2
   -Ofatsa: 2:14
   -Olungama: 2:18-19
   -Okhulupirika: 2:23
   -Omvera: 3:5
   -Ogonjera: 3:10
   -Okhazikika pa zamuyaya: 3:10
   -Okudzika ndi maonekedwe a choipa: 3:14
   -Oleza mtima: 3:18

## CHAPUTALA CHA 13

I NDI II SAMUELI

ZOLINGA:
Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula yemwe analemba mabuku a I ndi II Samueli.
- Kudziwa kumene amalembera mabukuwa.
- Kutchula cholinga cha mabukuwa.
- Kulemba Mavesi Otsogolera a mabuku a I ndi II Samueli kuchokera pamtima.
- Kutchula moyo ndi mfundo ya utumiki ya mabuku a I ndi II Samueli.

### I SAMUELI

MAWU OYAMBA

**WOLEMBA**: Samueli

**OMWE AMAWALEMBERA**: Israyeli

**CHOLINGA CHIMENE AMALEMBERA**: Kupitiliza za mbiri ya mmene Mulungu amachitira ndi anthu ake.

**MAVESI OTSOGOLERA:** I Samueli 15:22-23

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI**: Kumvera Mulungu kumaposa nsembe.

**ANTHU OMWE AKUTCHULIDWAMO:** Samueli, Elikana, Hana, Davide, Sauli, Jonatani, Mikali, Abigaeli.

### MAGAWO

I. Samueli: Oweruza otsiriza: 1:1-7:17
   A. Kubadwa ndi umwana wa Samueli: 1:1-2:10
   B. Kukanidwa kwa Eli ndi kuitanidwa kwa Samueli: 2:11-3:21
   C. Likasa pakati pa Afilisiti: 4:1-7:1
   D. Ntchito za Samueli ngati oweruza: 7:2-17

II. Sauli: Mfumu yoyamba mwa mafumu: 8:1-15:35

A. Israyeli afuna mfumu: 8:1-22
B. Chisankho cha Sauli: 9:1-11:15
C. Mawu a Samueli otsiriza: 12:1-25
D. Nkhondo ya Sauli ndi Afilisiti: 13:1-14:52
E. Kusamvera kwa Sauli ndi kukanidwa kwake: 15:1-35

III. Sauli ndi Davide: 16:1-31:13

A. Kudzodzedwa ndi maitanidwe a Davide: 16:1-23
B. Chigonjetso cha David kwa Goliati: 17:1-58
C. Davide athawa Sauli: 18:1-20:42
D. Davide ayendayenda: 21:1-30:31
E. Imfa ya Sauli: 31:1-13

## II SAMUELI

MAWU OYAMBA

**WOLEMBA**: Samueli

**OMWE AMAWALEMBERA**: Israyeli

**CHOLINGA**: Kupitiliza za mbiri ya mmene Mulungu amachitira ndi anthu ake.

**VESI LOTSOGOLERA**: II Samueli 7:22-23

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI**: Mulungu amakwaniritsa dongosolo lake kudzera kwa iwo amene amvera Iye posatengera zofooka za umunthu.

**ANTHU OMWE AKUTCHULIDWAMO**: Davide, Uriya, Betiseba, Natani, Abisalomu, Abina, Isiboseti, Yowabu.

### MAGAWO

I. Chigonjetso cha Davide: 1:1-10:19
- A. Davide alilira Sauli ndi Jonatani: 1:1-27
- B. Davide akhala mfumu ya Ayuda: 2:1-7
- C. Davide akhazikitsa chipembedzo komanso boma limodzi: 2:8-6:23
- D. Pangano la Davide: 7:1-29
- E. Chigonjetso cha Davide: 8:1-10:19

II. Masautso a Davide: 11:1-24:25
- A. Tchimo la Davide ndi kulapa kwake: 11:1-12:31
- B. Mlandu wa Aminoni ndi Abisalomu: 13:1-18:33
- C. Davide abwenzeretsedwa mphamvu: 19:1-20:26
- D. Njala ndi kubwenzera kwa a Gibiyoni: 21:1-14
- E. Chiwanga cha nkhondo ndi Afilisiti: 21:15-22
- F. Nyimbo ya Davide ndi mawu ake otsiriza: 22:1-23:7
- G. Chiwanga cha Davide: 23:8-39
- H. Chiwerengero ndi chilango cha Davide: 24:1-25

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Kodi analemba buku la I ndi II Samueli ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la I Samueli.

3. Kodi buku la I Samueli amalembera kwa ndani?

4. Tchulani mooyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la I Samueli.

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la I Samueli

6. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la II Samueli.

7. Kodi buku la II Samueli amalembera kwa ndani?

8. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la II Samueli.

9. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la II Samueli.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli).

**KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. I Samueli amafotokoza za kusintha kwa utsogoleri mu mbiri ya Israyeli kuchoka kolamulidwa ndi Mulungu (kudzera kwa ansembe ndi asilikali) kupita kodzilamulira okha (kudzera mmafumu osiyanasiyana).

2. I Samueli 15:22-23 ndi imodzi mwa ndime zazikulu zokhudza kumvera.

3. I Samueli 16:7 ndi imodzi mwa ndime zazikulu zokhudza kuyenera kwa umunthu.

4. I Samueli 17:4 amakamba za munthu wamkulu padziko lapansi.

5. I Samueli 18:1 amakamba mmodzi mwa bwenzi lofunika lokongola kwambiri Mbaibulo.

6. I Samueli analemba zambiri za anthu amene anakhala padziko kenako mkumwalira. Onani I Samueli 28; Luka 16:23-31; Chibvumbulutso 6:9-10 ndi 7:9-10.

7. Samueli anayamba maphunziro a Baibulo oyamba Mmalema. Izi zimapezeka ku Giligala, Yeriko, ndi Beteli. Onani I Samueil 10:10; I Mafumu 18:13; II Mafumu 2:3,5; 6:1-2.

8. II Samueli amakamba za lamulo lofunika la kufetsa ndi kututa mu uzimu mdzikoli. Atapemphera Davide pemphero lake la kulapa (Masalmo 51) Mulungu adamkhululukira chigololo ndi kupha kumene adachita (II Samueli 11). Komabe Davide anakolola chisoni mu ntchito zake. Zimene anakolola ndi monga imfa ya mwana wake, kugwiriridwa kwa mwana wake wamkazi ndi wa mamuna, kuphedwa kwa mbale wake ndi mbale wake, ndi kuukira kwa mwana wake wokondedwa amene zotsatira zake anaphedwa ndi msilikali wankhondo.

9. Mfundo ina yofunika kwambiri imene ikuphunzitsidwa mu buku la II Samueli ndi kuchita chifuniro cha Mulungu mu njira ya Mulungu. Chinali chifuniro cha Mulungu kuti Davide atengere likasa Mmalo Oyera, njira ya Mulungu inali kuti ansembe anyamule likasa. Kumayambiriro Davide sanamvere ndipo zotsatira zake zinali chisoni ndi imfa (6:1-17). Choncho ndizofunika kuyanjanitsa chifuniro cha Mulungu ndi njira ya Mulungu.

## CHAPUTALA CHA 14

I NDI II MAFUMU

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula amene analemba I ndi II Mafumu.
- Kudziwa amene amawalembera mabuku a I ndi II Mafumu.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku lililonse
- Kulemba Vesi Lotsogolera la mabuku a I ndi I Mafumu.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya mabuku a I ndi II Mafumu.

### I MAFUMU

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA**: Wosadziwika. Mwina Yeremiya

**OMWE AMAWALEMBERA**: Israyeli

**CHOLINGA**: Kupitiliza za mbiri ya mmene Mulungu amachitira ndi anthu ake.

**VESI LOTSOGOLERA**: I Mafumu 19:18

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI**: Kusamvera Mulungu kumaoneka kopanda tanthauzo koma kuli ndi mtengo wake.

**ANTHU OMWE AKUTCHULIDWAMO**: Davide, Solomoni, Mafumu a Ayuda (onani pa tchati), Nabati, Ahabu, Eliya, Elisa.

### MAGAWO

I. Ufumu wa mfumu Solomoni: 1:1-11:43
    A. Kudzodzedwa kwake ngati mfumu: 1:1-53
    B. Chitsimikizo cha Davide kwa Solomoni ndi imfa yake: 2:1-46
    C. Ukwati wa Solomoni ndi kusankha nzeru: 3:1-28
    D. Utsogoloeri wa Solomoni: 4:1-34
    E. Mamangidwe a Solomoni: 5:1-8:66
    F. Ulemerero ndi chuma cha Solomoni: 9:1-10:29

G. Tchimo la Solomoni: 11:1-43

II. Ufumu wa mafumu a Yuda ndi Israyeli: 12:1-22:53; umene ukupezekanso mu II Mafumu. (Onani pa tchati la mafumu.)

A. Kukwera kwa Rehoboamu: 12:1-33
B. Mafumu a Yuda: Rehoboamu to Yehosafati: 13:1-22:53
C. Mafumu a Israyeli: Yeroboamu mpaka Ahaziya: 13:1-22:53
D. Utumiki wa mneneri Eliya ku Israyeli: 17:1-22:53

## II MAFUMU

MAWU OYAMBA

**WOLEMBA**: Osadziwika. Mwina Yeremiya

**OMWE AMAWALEMBERA**: Israyeli

**CHOLINGA**: Kupitiliza za mbiri ya mmene Mulungu amachitira ndi anthu ake, Israyeli.

**VESI LOTSOGOLERA**: II Mafumu 2:9-10

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI**: Maufumu a dziko lapansi ndi akanthawi: Amadzuka ndi kugwa mwa ulamuliro wa Mulungu.

**ANTHU OMWE AKUTCHULIDWAMO**: Maufumu a Israyeli ndi Yuda (onani pa tchati la maufumu), Elisa, Eliya.

### MAGAWO

I. Utumiki wa Elisa ndi mbiri ya maufumu a Israyeli: 1:1-10:36

II. Mbiri ya maufumu a Israyeli ndi Juda: 11:1-17:41
Ikupitilira kuchokera mu I Mafumu. (Onani tchati la mafumu.)

III. Ufumu wa mafumu a Chiyuda: Hezekiya mpaka Zedekiya: 18:1-25:30
(Onani tchati la maufumu.)

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Kodi analemba mabuku a I ndi II Mafumu ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la I Mafumu.

3. Kodi buku la I Mafumu amalembera kwa ndani?

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la I Mafumu.

5. Lembani Vesi Lotsogolera ya buku la I Mafumu.

6. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la II Mafumu.

7. Kodi buku la II Mafumu amalembera kwa ndani?

8. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la II Mafumu.

9. Lembani Vesi Lotsogolera ya buku la II Mafumu.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli).

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. I Mafumu 12 amakamba za kusokonekera kwa mafuko 12 a Israyeli. Chibvumbulutso 7 amalongosola za kulumikiza mafukowa mtsogolo. Tchati mugawo limeneli likuomba mkota zokhuza kugawanikana kwa maufumu a Israyeli ndi Yuda. Mapuwa akuonetsa mmene maderawo anagawanikira.

2. Mfumu Solomoni, ndi mmodzi mwa anthu ofunika mu I Mafumu, analemba buku la Miyambo, Mlaliki, ndi Nyimbo ya Solomoni. Mabukuwa muwawernga kutsogoloku mu phunziroli.

3. Tchatili la mafumu a Israyeli ndi Yuda likuthandizani pamene mukuwerenga mabuku a Mafumu ndi Mbiri.

### Mafumu a Israyeli

| **Dzina la Mfumu** | **Zaka za ufumu** | **Masiku B.C.** | **Mabuku** |
|---|---|---|---|
| Yeroboamu I | 22 | 976-954 | I Mafumu 11:26-14:20 |
| Nadabu | 2 | 954-953 | I Mafumu 15:25-28 |
| Basa | 24 | 953-930 | I Mafumu 15:27-16:7 |
| Ela | 2 | 930-929 | I Mafumu 16:6-14 |
| Zimuri | (masiku 7) | 929 | I Mafumu 16:9-20 |
| Omuri | 12 | 929-918 | I Mafumu 16:15-28 |
| Ahabu | 21 | 918-898 | I Mafumu 16:28-22:40 |
| Ahaziya | 1 | 898-897 | I Mafumu 22:40-II Mafumu 1:18 |
| Yehoramu | 11 | 897-885 | II Mafumu 3:1-9:25 |
| Yehu | 28 | 885-857 | II Mafumu 9:1-10:36 |
| Yehoahazi | 16 | 857-841 | II Mafumu 13:1-9 |
| Yehowashi (Yowa) | 16 | 841-825 | II Mafumu 13:10-14:16 |
| Yeroboamu II | 40 | 825-773 | II Mafumu 14:23-29 |
| Zakariya | theka | 773-772 | II Mafumu 14:29-15:12 |
| Shalumu | (mwezi umodzi) | 772 | II Mafumu 15:10-15 |
| Menahemu | 10 | 772-762 | II Mafumu 15:14-22 |
| Pekahiya | 2 | 762-760 | II Mafumu 15:22-26 |
| Pekah | 20 | 760-730 | II Mafumu 15:27-31 |
| Hosea | 9 | 730-721 | II Mafumu 15:30-17:6 |

**Mafumu a Yuda**

| Dzina la Mfumu | Zaka za ufumu | Masiku B.C. | Mabuku |
|---|---|---|---|
| Rehoboamu | 17 | 976-959 | I Mafumu 11:42-14:31 |
| Abiya | 3 | 959-996 | I Mafumu 14:31-15:8 |
| Asa | 41 | 956-915 | I Mafumu 15:8-24 |
| Yehosafati | 25 | 915-893 | I Mafumu 22:41-50 |
| Yehoramu | 8 | 893-886 | II Mafumu 8:16-24 |
| Ahaziya | l | 886-885 | II Mafumu 8:24-9:29 |
| Atiliya | 6 | 885-879 | II Mafumu 11:1-20 |
| Yoashi | 40 | 879-840 | II Mafumu 11:1-12:21 |
| Amaziya | 29 | 840-811 | II Mafumu 14:1-20 |
| Azariya (Uziya) | 52 | 811-759 | II Mafumu 15:1-7 |
| Yotani | 18 | 759-743 | II Mafumu 15:32-38 |
| Ahaz i | 19 | 743-727 | II Mafumu 16:1-20 |
| Hezekiya | 29 | 727-698 | II Mafumu 18:1-20:21 |
| Manase | 55 | 698-643 | II Mafumu 21:1-18 |
| Amoni | 2 | 643-640 | II Mafumu 21:19-26 |
| Yosiya | 31 | 640-609 | II Mafumu 22:1-23:30 |
| Yehohazi | (miyesi itatu) | 609 | II Mafumu 23:31-33 |
| Yehoiyakumi | ll | 609-597 | II Mafumu 23:34-24:5 |
| Yehoiyakimu | (miyezi itatu) | 597 | II Mafumu 24:6-16 |
| Zedekiya | ll | 597-586 | II Mafumu 24:17-25:30 |

**Tchati loonetsa magawo a maufumu**

| ISRAYELI 933-722 B.C.<br>Mayina ena: | YUDA 933-586 B.C.<br>Mayina ena: |
|---|---|
| Mafuku khumi | Mafuko awiri |
| Ufumu wa kummawa | Ufumu wa kumwera |
| Samaliya / Efraimu | Nyumba ya Davide |
| | |
| Mabanja olamulira | Mabanja olamulira |
| Mabanja 9 olamulira | Banja limodzi |
| Mafumu 9 (oipa) | Mafumu 20 (ambiri abwino) |
| | |
| Mmodzi odzipa / 7 | 5 ophedwa |

| | |
|---|---|
| Ophedwa | |
| Kutalika kwa nthawi | kutalika kwa nthawi |
| Zaka 211 | zaka 347 |
| | |
| Ukapolo | ukapolo |
| Analangidwa ndi Asuri | kupita ku Babulo |
| Kumwazidwa kwa mitundu yonse | kubwerera patatha zaka 70 |
| | Kumanganso Yerusalemu ndi kachisi |
| Madera ake: | madera ake |
| Kupitilira Kanani kwa 2/3 | kuchepera Kanani kwa 1/3 |
| Gawo labwino | kachisi ndi yerusalemu |
| | |
| Chipembedzo | chipembedzo |
| Kukana njira yopembedza Mulungu | mafano ngati chipembedzo |
| Kulambira mwana wa ng’ombe | kusintha kopitilira |
| Kulambira Bala ndi Asera mu nthawi Ya ufumu wa Ahabu. | Mafumu oopa Mulungu |

## CHAPUTALA CHA 15

I NDI II MBIRI

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula amene analemba I ndi II Mbiri.
- Kudziwa kumene mabukuwa amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku lililonse.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la I ndi II Mbiri kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya I ndi II Mbiri.

### I MBIRI

MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Wosadziwika. Mwina Ezara

**OMWE AMAWALEMBERA**: Israyeli

**CHOLINGA:** Kulemba za mbiri ya chipembedzo ya Ayuda.

**VESI LOTSOGOLERA:** I Mbiri 29:11

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Pamene Mulungu wakwezedwa anthu ake amadalitsidwa.

**ANTHU OMWE AKUTCHULIDWAMO:** Mfumu Davide, Solomoni.

### MAGAWO

I. Makolo kuchokera kwa Adamu kufikira Davide: 1:1-9:44

A. Kuchokera kwa Adamu kufikira Yakobo: 1:1-2:2
B. Kuchokera kwa Yakobo kufikira Davide: 2:2-9:44

II. Mbiri ya Mfumu Davide: 10:1-29:30

A. Imfa ya Mfumu Sauli: 10:1-14

B. Kugonjetsedwa kwa Zione ndi ankhondo a Davide: 11:1-12:40
C. Kuchita bwino kwa ufumu wa Davide: 13:1-22:1
D. Kukwaniritsidwa kwa chipembedzo cha Davide: 22:2-29:30

## II MBIRI

MAWU OYAMBA

**WOLEMBA**: Osadziwika

**OMWE AMAWALEMBERA**: Israyeli

**CHOLINGA**: Kulemba mbiri ya chipembedzo ya Ayuda.

**VESI LOTSOGOLERA**: 2 Mbiri 7:14

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Madalitso a Mulungu amabwera pamene tazichepetsa ndi kumfuna Iye.

**ANTHU OMWE AKUTCHULIDWAMO**: Mfumu Solomoni, ndi amene anamuthandiza kuchokera kwa Rehoboamu mpaka Zedekiya (onani tchati la mafumu a Ayuda).

**MAGAWO**

I. Mbiri ya Mfumu Solomoni: 1:1-9:31

- A. Chuma ndi nzeru za Solomoni: 1:1-17
- B. Mamangidwe a Solomoni ndi kupatula kachisi: 2:1-7:22
- C. Ntchito zambiri za Solomoni: 8:1-9:28
- D. Imfa ya Solomoni: 9:29-31

II. Mbiri ya mafumu a Ayuda: 10:1-36:23

- A. Mafumu kuchokera kwa Rehoboamu kufikira Zedekiya: 10:1-36:21
  (Kuti mudziwe zambiri za mafumuwa, onani tchati la mafumu a Yuda mu chaputala chotsatirachi.)

- B. Chilamulo cha Kolesi: 36:22-23

**MAYESO ODZIYETSA NOKHA**

1. Kodi analemba mabuku a I ndi II Mbiri ndi ndani?

___

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la I Mbiri.

___

3. Kodi buku la I Mbiri amalembera kwa ndani?

___

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la I Mbiri.

___

5. Lembani vesi lotsogolera la buku la I Mbiri.

___

6. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la II Mbiri.

___

7. Kodi buku la II Mbiri amalembera kwa ndani?

___

8. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la II Mbiri.

___

9. Lembani vesi lotsogolera ya buku la II Mbiri.

___

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Ngakhale pali kufanana kwakukulu pakati pa II Samueli, Mafumu ndi Mbiri, koma buku lililonse linalembedwa kuti likwaniritse cholinga chake.

   Mwachitsanzo, II Samueli ndi I ndi II Mafumu akuonetsera mbiri ya utsogoleri wan dale za Yuda ndi Israyeli. Pamene mu I ndi Mbiri amapereka tsatanetsatane wa mbiri ya chipembedzo cha Yuda chokha.

   II Samueli ndi I ndi II Mafumu amaona nthawi ya atsogoleri ndi aneneri. I ndi II Mbiri amakamba za ansembe ndi kachisi.

   Pamene mukuwerenga mabukuwa mwatsatanetsatane, muyang'ane kusiyana kwa zinthu zina zimene zikubwerezedwa.

2. II Mbiri ndi buku la zitsitsimutso. Zitsitsimutso zazikulu zinachitika mu nthawi ya:

| | |
|---|---|
| -Asa: | II Mbiri 15 |
| -Yehosafati: | II Mbiri 20 |
| -Yoasi: | II Mbiri 23-24 |
| -Hezekiya: | II Mbiri 29-31 |
| -Yosiya: | II Mbiri 35 |

3. Mawu otsogolera mu ofunika mu buku la Mbiri ndi:
   -nyumba
   -lisasa
   -pangano
   -kulira (analira)
   -kufuna (anafuna)
   -mtima
   -kupemphera (pemphero, anapemphera)
   -aneneri

4. Maphunziro ambiri okhuza pemphero ndi kumfuna Mulungu akupezeka mmabukuwa. Onaninso zimene mwaphunzira poona mawu otsogolera. Werengani makamaka II Mbiri 6.
5. Kodi mwaphunzira chiyani pa zipambano zifooko za anthu awa monga Yehosafati, Hezekiya ndi Uziya?

## CHAPUTALA CHA 16

EZARA

ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula wolemba buku la Ezara.
- Kudziwa kumene buku la Ezara amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Ezara.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Ezara kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Ezara.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Ezara

**OMWE AMAWALEMBERA:** Israyeli

**CHOLINGA:** Kulemba za mbiri ya Israyeli yobwerera

**VESI LOTSOGOLERA:** Ezara 6:16

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Kubwerera ndi kubwenzeretsedwa ndi maziko a kulapa.

**ANTHU OMWE AKUTCHULIDWAMO:** Ezara, Yeswa, Zelubabele, Koresi, Hagai, Zakariya, Aritasasta.

### MAGAWO

I. Kubwenzeretsa pa utsogoleri wa Zelubabele: 1:1-6:22

A. Kubwerera koyamba ku ukapolo: 1:1-2:70
1. Lamulo ka Koresi: 1:1-11
(a) Chilembo cha chilamulo: 1:2-4
(b) Khumbo la anthu: 1:5-11
2. Mndandanda wa a ukapolo: 2:1-70

B. Kubwenzeretsa chipembedzo cha anthu: 3:1-6:22

1. Kumanganso kachisi: 3:1-6:15
(a) Malambiro abwenzeretsedwa ku Yerusalemu: 3:1-7

(b) Ntchito ya pa kachisi: 3:8-13
(c) Satana ayesera kulepheretsa ntchito: 4:1-24
(d) Aneneri athandiza: 5:1-2
(e) Mafunso a olamulira: 5:3-5
(f) Kalata yopita kwa Dariyo: 5:6-17
(g) Kufufuza: 6:1-12
(h) Yankho la Tatinai: 6:13-15

2. Kupatula kachisi: 6:16-22

II. Kusintha kwa zinthu mu nthawi ya Ezara: 7:1-10:44

A. Kubwerera kwachiwiri ku ukapolo 7:1-8:36

1. Mbiri ya Ezara ndi kukonzekera: 7:1-10
2. Kalata ya Aritasasta: 7:11-26
3. Yankho la Ezara: 7:27-28

B. Kukonza makhalidwe oipa: 9:1-10:44

1. Anthu a Mulungu achita zoipa: 9:1-2
2. Pembedzero la Ezara: 9:3-15
3. Kukhuzidwa kunakhazikika pa anthu: 10:1-8
4. Kuvomereza ndi kulapa: 10:9-16
5. Mndandanda wa anthu olakwa: 10:18-44

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Ezara ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene analembera buku la Ezara.

3. Kodi buku la Ezara amalembera kwa ndani?

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki la buku ya Ezara

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Ezara.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

**KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Werengani Masalmo137. Ndimeyi imafotokoza za chisoni cha anthu a Mulungu pamene anali pa ulendo wochokera ku Yerusalemu kupita ku ukapolo wa ku Babulo. Werengani Masalmo 126 pamene amafotokoza za chimwemwe pobwerera ku Yerusalemu kupita kuchoka ku ukapolo.

2. Maufumu onse a Israyeli ndi Yuda amene anagawana anatengedwa kupita ku ukapolo ndi adani awo. A I srayeli anatengedwa ndi Asuri mu zaka za 721 B.C. Pomwe Yuda anatengedwa ku Babulo mu zaka za 606 B.C. Kubwerera kwawo kupita ku Yerusalemu kunali kotere:

   536 B.C. Zelubabele ndi ayuda okwana 42,360, akapolo okwana 7,337, oyimba 200, abulu okwana 736, mule okwana 245, ngamira zokwana 435, ndalama zokwana 6,720, ndipo golidi ndi siliva okwana 5,400.

   457 B.C. Ezara ndi anthu okwana 1,754, matalente a golidi 100, matalente a siliva 750. Sakutiuza ngati akazi ndi ana anali nawo pa ulendowu wobwerera ku ukapolo.

   444 B.C. Nehemiya ndi asilikali omperekeza, kukamanganso ndi kutchinga Yerusalemu.

3. Panali maulendo awiri a ku ukapolo wa ku Babulo. Mu Ezara muli ma ulendo atatu obwera ku dziko la malonjezano.

Maulendo atatu a ku Babulo:

-Mmasiku a Danieli: 606 B.C.
-Mmasiku a Ezekieli: 597 B.C.
-Mmasiku a mfumu Zedekiya: 586 B.C.

Maulendo atatu a ku ufulu:

-Motsogozedwa ndi Zelubabele ndi Yoswa: 538 B.C.
-Motsogozedwa ndi Ezara: 456 B.C.
-Motsogozedwa ndi Nehemiya: 446 B.C.

## CHAPUTALA CHA 17

NEHEMIYA

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Nehemiya.
- Kudziwa amene amawalembera buku la Nehemiya.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Nehemiya.
- Kulemba Vesi Lotsogolera ya buku la Nehemiya kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Nehemiya.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Nehemiya

**OMWE AMAWALEMBERA**: Israyeli

**CHOLINGA**: Kupitilira ndi mbiri ya Israyeli. Mbiri ya kumanganso kwa malinga a Yerusalemu.

**VESI LOTSOGOLERA:** Nehemiya 6:3

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Palibe mwayi opanda chitsutso. Chikhulupiriro chopanda ntchito ndi chakufa.

**ANTHU OMWE AKUTCHULIDWAMO:** Nehemiya, Sanabalati, Gesemu, Semiya, Tobiya, Hananiya, Ezara, Aritasasta.

### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1-11

   A. Nkhani yosakhala bwino yak u Yerusalemu: 1:1-3
   B. Zimene anachita Nehemiya: 1:4-11

II. Kukonzekera ntchito: 2:1-20

   A. Limodzi ndi Mfumu: 2:1-8

B. Limodzi ndi olamulira: 2:9-10
C. Ku Yerusalemu: 2:11-15
D. Limodzi ndi akuluakulu a anthu: 2:15-20

III. Kubwenzeretsa malinga: 3:1-6:19
  A. Mndandanda wa omanga ndi gulu: 3:1-32
  B. Otsutsana nawo akunja ndi mkati mwa mzinda: 4-6:14
    1. Otsutsana nawo a mkati:
      (a) Kutsutsa kwa chindunji: 2:19
      (b) Kunyoza ndi kuchepsa: 4:1-3
      (c) Umboni wabodza: 6:5-7
      (d) Ziwawa mu nthawi yovuta: 4:6
      (e) Kusintha: 6:2
      (f) Kukopedwa ndi gulu: 6:2
      (g) Zipsezo, mantha: 6:5-9
      (h) Kuzisiya: 5:14-19
      (i) Nkhondo, kutchinga: 4:8
      (j) Chiwembu: 4:8; 6:2
      (k) Ziopsezo ndi mantha: 6:5-9
    2. Chitsutso cha mkati:
      (a) Chifooketso: 4:10-11
      (b) Kusagwirizana: 5:1-19
      (c) Okhulupirira ofooka: 4:12
      (d) Chitsutso cha atsogoleri a chipembedzo: 3:5
      (e) Aneneri a Mulungu onama: 6:10-13
  C. Linga limalizidwa: 6:15-19

IV. Chitetezo ndi kalembera: 7:1-73
  A. Kukhazikika chitetezo cha mzinda: 7:1-4
  B Kalembera wa obwerera ku ukapolo: 7:5-73

V. Kusintha kwa chipembedzo kwa Ezara ndi Nehemiya: 8:1-13:31
  A. Kuwerenga chilamulo: 8:1-8:18
  B. Kuvomereza ndi pemphero: 9:1-37
  C. Kukonzanso pangano: 9:38-10:39
  D. Mndandanda wa anthu: 11:1-12:26
  E. Kupatula linga: 12:27-47
  F. Kusintha kwa Nehemiya: 13:1-31

**Mawu olimbikitsa**

Mawu khumi a Nehemiya olimbikitsa:

-Dzanja labwino la Mulungu pa ine: 2:8
-Tiyeni tidzuke timange: 2:18
-Mulungu wa kumwamba adzatilemeretsa: 2:20
-Anthu anali ndi mtima wogwira ntchito: 4:6
-Kumbukirani Ambuye ndi kuchita nkhondo: 4:14
-Mulungu adztimenyera nkhondo: 4:20
-O Mulungu limbitsani manja athu: 6:9
-Ntchitoyi inagwiridwa ndi Mulungu wathu: 6:16
-Chimwemwe cha Ambuye ndiye mphamvu yathu: 8:10
-Kumbukirani, O Mulungu wanga: 13:29,31

**MAYESO ODZIYETSA NOKHA**

1. Kodi analemba buku la Nehemiya ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene analembera buku la Nehemiya.

3. Kodi buku la Nehemiya amalembera kwa ndani?

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Nehemiya.

5. Lembani vesi lotsogolera la buku la Nehemiya.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

**KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Ntchito ya Mulungu nthawi zonse idzakumana ndi anthu kapena Satana oyitsutsa mbali zonse. Pamene mukuwerenga buku la Nehemiya, lembani mndandanda wa ziopsezo za adani amene anayesera kuletsa ntchito ya Mulungu.

2. Zipata za malinga zimene zinazungulira Yerusalemu zili ngati moyo wa Mkhristu. Zimene zikutanthauza kuti ngakhale zinali zipata zenizeni, analinso zizindikiro za choonadi cha uzimu:

| | | **Mabuku ake** | |
|---|---|---|---|
| **Dzina la chipata** | **Kuimira** | **Nehemiya** | **Ena** |
| Chipata cha nkhosa | Mtanda | 3:1 | Yohane 10:11 |
| Chipata cha nsomba | Kupeza moyo | 3:3 | Mateyu 4:19 |
| Chipata chakale | Khalidwe lakale | 3:6 | Aroma 6:1-23 |
| Chipata cha chigwa | Mazunzo / mayesero | 3:13 | II Akorinto 1:3-5 |
| Chipata cha ndowe | Ntchito za thupi | 3:14 | Agalatiya 5:16-21 |
| Chipata cha kasupe | Mzimu Woyera | 3:15 | Yohane 7:37-39 |
| Chipata cha madzi | Mau a Mulungu | 3:26 | Yohane 4:10-14 |
| Chipata cha bulu | Nkhondo ya a Khristu | 3:28 | Aefeso 6:10-17 |
| Chipata cha kummawa | Kubwerea kwa Yesu | 3:29 | Ezekieli 43:1,2 |
| Chipata cha Mifikati | Mpando wa chiweruzo Wa Yesu | 3:31 | I Akorinto 3:9-15; II Akorinto 5:10 |

## CHAPUTALA CHA 18

ESTERE

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula amene analemba buku la Estere.
- Kudziwa kumene amalembera buku la Estere.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Estere.
- Kulemba vesi lotsogolera la Estere kuchokera pamtima.
- Kutchula moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Estere.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Osadziwika

**OMWE AMAWALEMBERA:** Ayuda ofalikira ku Peresiya

**CHOLINGA:** Kupitlira ndi mbiri ya Israyeli. Komanso kuona za thandizo la Mulungu kwa anthu ake.

**VESI LOTSOGOLERA:** Estere 4:14

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Mulungu amakumana ndi zosintha za moyo pogwiritsa anthu ngati zotengera.

**ANTHU OMWE AKUTCHILIDWAMO:** Estere, Vashiti, Hamani, Ahaswero.

### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1-22

   A. Phwando lalikulu: 1:1-9
   B. Vuto la mnyumba: 1:10-12
   C. Lamulo la mfumu: 1:13-22

II. Mkazi wa mfumu watsopano: 2:1-21

   A. Kufuna mkazi wa mfumu watsopano: 2:1-4
   B. Estere achita nawo mpikisano: 2:5-11

1. Mbiri ya Modekayi: 2:5-6
2. Mbiri ya Estere: 2:7

C. Estere mnyumba mwa Hegayi: 2:8-11
D. Akazi pamaso pa mfumu: 2:12-14
E. Estere asankhidwa ngati mkazi wa mfumu: 2:15-17
F. Phwando la Estere: 2:18
G. Chinsinsi cha Estere: 2:19

III. Anthu awiri, ziwembu ziwiri: 2:21-3:15

A. Modekayi aulura chiwembu: 2:22-23
   1. Modekayi pachipata cha mmfumu: 2:22-23
   2. Modekayi aulura chiwembu 2:21-22
   3. Achiwembu awiri apachikidwa: 2:23
B. Kukwezedwa ndi chiwembu cha Hamani: 3:1-15
   1. Hamani akwezedwa pamwamba pa ana a mafumu onse: 3:1
   2. Vuto pakati pa Hamani ndi Modekayi: 3:2-6
   3. Hamani abwenzera chiwembu: 3:7-15

IV. Kuthedwa nzeru ndi chipulumutso: 4:1-7:10

A. Kuthedwa nzeru kwa Ayuda: 4:1-3
B. Kuthedwa nzeru kwa Mfumukazi: 4:4-9
C. Dongosolo la chipulumutso: 4:10-5:14
   1. Dongosolo: 4:10-17
   2. Pamaso pa mfumu: 5:1-3
   3. Kuitanidwa ku phwando: 5:4-8
   4. Kudzikweza kwa Hamano: 5:9-14
D. Modekayi akwezedwa: 6:1-14
   1. Kuwerenga kwa Mfumu: 6:1-3
   2. Hamani apempha nzeru: 6:4-5
   3. Hamani achita modzikweza: 6:6-9
   4. Hamani achita manyazi pamene Modekayi akwezedwa: 6:10-12
   5. Zimene banja la Hamani ndi anzache anachita: 6:13-14
E. Phwando la Estere: 7:1-6
F. Hamani alangidwa: 7:7-10

V. Dongosolo la ufumu watsopano: 8:1-10:3

A. Dongosolo latsopano la mfumu: 8:1-14
B. Modekayi akwezedwa: 8:15-17

C. Chipulumutso cha Ayuda: 9:1-11
D. Nyumba ya Hamani iwonongedwa: 9:12-14
E. Phwando la Purimu: 9:15-32
F. Chionetsero cha Modekayi: 10:1-3

**MAYESO ODZIYETSA NOKHA**

1. Kodi analemba buku la Estere ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene analembera buku la Estere.

3. Kodi buku la Estere amalembera kwa ndani?

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Estere.

5. Lembani vesi lotsogolera la buku la Estere.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenkweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Ndime yaitali mu Baibulo ili mbuku la Estere 8:9. Ndimeyi ili ndi mawu okwana 90 a mu Chingerezi cha King James Vesrion.

2. Onani kusiyana pakati pa buku la Rute ndi Estere:
   -Rute anali wamitundu amene anakhala pakati pa Ayuda.
   -Estere anali mYuda amene anakhala pakati pa amitindu.
   -Rute anakwaiwa ndi mYuda.
   -Estere anakwaitwa ndi wamitundu.

   Zotsatira za nkhani zawo zonsezi zinaonekera mu mkumano wawo wa usiku:
   -Rute analankhula ndi Boazi: Rute 3:8-13
   -Hamani analankhula ndi mfumu: Estere 6:1-10

3. Phunzira khalidwe la Hamani ngati Satana:
   -Pamwamba pa ana a mafumu onse: 3:1
   -Wodzala ndi mkwiyo: 3:5
   -Wodzala ndi mnyozo: 3:6
   -Woononga: 3:6
   -Mdani: 3:10
   -Wozikundikira chuma: 3:8,9,11; 4:7
   -Wozunguzika: 3:15
   -Wodya ndalama za msonkho: 3:13
   -Wosathawa: 4:13
   -Munthu wonyasidwa: 5:9
   -Wonyanda: 5:11-12; 6:6-9
   -Wonyoza: 5:13; 6:12
   -Wachiwembu: 3:1-15; 5:14; 6:4
   -Woneneza ndi mdani: 7:6
   -Woipa: 7:8
   -Wanjira zoipa: 9:25
   -Wamantha pamaso pa mfumu: 7:6
   -Wokugwa pamaso pa anthu a Mulungu: 6:13

## MAWU OYAMBA A
## MABUKU A NDAKATULO

Mabuku asanu a ndakatulo amaonetsa kupita chitsogolo kwa moyo wauzimu.

**Yobu:** amakamba za imfa ku moyo wakale wa umwini.

**Masalmo**: amaonetsera moyo watsopano mwa Mulungu makamaka mmatamando, mpemphero, mchiyamiko, pembedzero, mchivomerezo, ndi mpembedzero. Masalmo ndi buku la nyimbo ndi malambiro a Mbaibulo.

**Miyambo:** Limapereka nzeru ya kumwamba yochita mmoyo wa pansi pano.

**Mlaliki:** Amakamba za uchabe wokhala ndi moyo “pansi pano” opanda Mulungu.

Nyimbo ya Solomoni: Bukuli limapereka chitsanzo cha moyo chatanthauzo pa ubale wa munthu ndi Yesu Khristu. Ndakatulo za Mbaibulo zisiyana ndi zinanzi zinalembedwa ndi maganizo a Chiheberi. Mfundo zothandiza kumvetsetsa zaperekedwa mu phunziro la Harvestime International Institute lotchedwa “*Njira zatsopano zophunzirira Baibulo”*

## CHAPUTALA CHA 19

YOBU

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula amene analemba buku la Yobu.
- Kudziwa kumene buku la Yobu amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Yobu.
- Kulemba vesi lotsogolera la buku la Yobu kuchokera pamtima.
- Kutchula moyo ndo mfundo ya utumiki ya buku la Yobu.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA: Osadziwika**

**OMWE AMAWALEMBERA:** Palibe kumene amalembera koma okhulupilira aliyense litha kumuthandiza.

**CHOLINGA:** Kulimbana ndi funso lakuti, "Chifukwa chiyani wolungama amavutika?"

**VESI LOTSOGOLERA:** Yobu 19:25-27; 23:10

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Pali tanthauzo la uzimu pamene munthu wolungama akuvutika. Kuvutika sichizindikiro chakuti Mulungu sakondwera nafe.

**AMENE AKUTCHULIDWAMO**: Mulungu, Satana, Yobu, Mkazi wa Yobu, Anzake, Elifazi, Bilidadi, Zofari, ndi Elihu.

### MAGAWO

I. Chiyambi: 1:1-2:13

A. Mawu oyamba: 1:1-5
B. Kuonekera koyamba kwa Satana ndi chonenera chake: 1:6-12
C. Yesero la Yobu: 1:13-22
D. Satana awonekera kachiwiri ndi chonenera chake: 2:1-6
E. Yesero la Yobu: 2:7-13

II. Gawo loyamba la zolankhula: 3:1-14:22

A. Zolankhula za Yobu: 3:1-26
B. Zolankhula za Elifazi: 4:1-5:27
C. Yankho la Yobu: 6:1-7:21
D. Zolankhula za Bilidadi: 8:1-22
E. Yankho la Yobu: 9:1-10:22
F. Zoyankhula za Zofari: 11:1-20
G. Yankho la Yobu: 12:1-14:22

III. Gawo lachiwiri la zoyankhula: 15:1-21:34

A. Elifazi alankhula: 15:1-35
B. Yobu ayankha: 16:1-17:16
C. Bilidadi ayankhula: 18:1-21
D. Yobu ayankha: 19:1-29
E. Zofari ayankhula: 20:1-34

IV. Gawo lachitatu la zoyankhula: 32:1-37

A. Elifazi alankhula komaliza: 22:1-30
B. Yobu ayankha: 23:1-24:25
C. Bilidadi alankhula komaliza: 25:1-6
D. Yobu ayankha: 26:1-31:40

V. Elihu ayankhula: 32:1-37:24

A. Kuyankhula koyamba: 32:1-33:33
B. Kuyankhula kachiwiri: 34:1-37
C. Kuyankhula kachitatu: 35:1-16
D. Kuyankhula kwachinayi 36:1-37:24

VI. Yankho la Mulungu: 38:1-42:6
A. Kuyankhula koyamba: 38:1-40:5
1. Mulungu amfusa Yobu kuchokera mu chilengedwe: 38:1-38
2. Mulungu amfusa Yobu kuchokera mu chilengedwe cha nyama: 38:39-39:30
3. Mulungu afuna mayankho ku mafunso ake: 40:1-2
4. Yankho loyamba la Yobu: 40:3-5
B. Kuyankhula kwachiwiri: 40:6-42:6
1. Mulungu amuuza Yobu azipulumutse yekha: 40:6-14

2. Mulungu afanizira mphamvu ya Yobu ndi ya Mvuu: 40:15-24
3. Mulungu afanizira mphamvu ya Yobu ndi ng'ona: 41:1-34
4. Yankho la Yobu lachiwiri: 42-1-6
    a. Yobu avomereza pa kusowa kumvetsetsa kwake: 42:1-3
    b. Yobu alapa pa kugalukira kwake: 42:4-6

VII. Mathero: 42:1-17

A. Chidzudzulo cha Umulungu kwa anzake a Yobu: 42:1-9
B. Kubwenzeretsedwa kwa Yobu: 42:10-17

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Yobu ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Yobu.

3. Kodi buku la Yobu amalembera kwa ndani?

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Yobu.

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Yobu kuchokera pamtima.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenkweni kwa bukuli).

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Lembani mndandanda wa mayina ndi khalidwe lawo amene analankhula m'buku la Yobu. Ombani mkoto pa maganizo awo. Mayankho pa vuto la kusautsika apezeka koma mosiyana malingana ndi anzake a Yobu. Onse anavomerezana kuti Yobu anachimwa.

   Elifazi amaona vuto molingana ndi mmene zimakhalira mwanseru.

   Bilidadi anakhazikitsa malangizo ake pa zimene anthu akhala akuyendera mu mbiri.

2. Fananitsani Yobu 1:21 ndi Afilipi 4:11-12

3. Buku la Yobu limatambasula mbiri ya dziko munthu kulibe. Onani chaputala 38-39. Mawu ena okhudza dziko akupezeka kuti akuthera mmalele (26:7) ndipo ndi maonekedwe a dziko (22:14).

4. Buku la Yobu limaululu choonadi mmagawo awiri:

   Choyamba, pali chifukwa chenicheni cha uzimu pamene olungama avutika: Yobu 1:6-12; 2:1-6.

   Chachiwiri, Satana sangakanthe okhulupirira opandapo Mulungu kulora: Yobu 1:6-12; 2:1-6. Mulungu amadziwa kuthekera kwathu ndipo sadzalora Satana kutiposa mphamvu (I Akorinto 10:13).

5. Bukuli muli zifukwa zambiri zimene Yobu anavutikira:
   -Satana akanakhoza kukhalitsidwa chete: 1:9-11; 2:4,5
   -Yobu akanakhoza kumaziona yekha malingana ndi mmene analili: 40:4; 42:6
   -Kuti Yobu akanakhoza kuona Mulungu: 42:5
   -Kuti anzake a Yobu akanatha osaweruza: 42:7
   -Kuti Yobu akanatha kupemphera anzake aja osati kuwatsutsa: 42:10
   -Malingaliro a Mulungu pa ana ake amabweretsa zotsatira zabwino kumapeto: 42:10

## CHAPUTALA CHA 20

MASALMO

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muuenera:

- Kutchula amene analemba buku la Masalmo.
- Kudziwa kumene buku la Masalmo amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Masalmo.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Masalmo kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Masalmo.

**MAWU OYAMBA**

**WOLEMBA:** Masalmo yense analembedwa ndi Mfumu Davide kuphatikizapo awa:
-Asafi: 50; 73-83
-Hemani: 88
-Etani: 89
-Solomoni: 127
-Mose: 90
-Hezekiya: 120, 121,123,125, 126, 128-130, 132, 134
-Wolemba wosadziwika: 1, 10, 33, 43, 66, 67, 71, 911-94, 96-100, 102, 104, 106, 107, 111-119, 135, 136, 137, 146-150

**OMWE AMAWALEMBERA**: Israyeli, ngakhale bukuli lakhala likugwiritsidwa ntchito pa chipembedzo, mapemphero, matamando kwa okhulupirira kwa nthawi yaitali.

**CHOLINGA**: Buku la Masalmo limadziwika ngati Nyimbo ya Israyeli. Mawu oti “Masalmo” amatanthauza “nyimbo zothandizana ndi zipangizo zoyimbira.” Choncho bukuli ndi pemphero komanso matamando a Mbaibulo.

**VESI LOTSOGOLERA**: Masalmo 95:1

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI**: Pemphero, mayamiko, mapembedzero, ndi chivomerezo ndi magawo a kulambira kolondora.

AMENE AKUTCHULIDWAMO: Anthu ambiri akutchulidwamo mbukuli, mkatikati mwa Masalmo komanso mmawu aakulu a Masalmo:

-Abimeleki (Akisi): I Samueli 21:10-15
-Absalomu: I Samueli 13
-Ahimeleki: I Samueli 22:9-19
-Aramu-naharaimu: Ameya kumpoto cha kumadzulo a Mesopotamiya
-Aramu-zobati: Ameya pakati pa m'Siya.
-Asafi: Mlevi, banja loyimba: II Mbiri 5:12
-Batiseba: II Samueli ll
-Kusi wa Benjamini (Simeli): II Samueli 16:5-14
-Doegi wa ku Edomu: I Samueli 22:9-23
-Etani wa ku Ezra (Munthu wanzeru mu nthawi ya Solomoni): I Mfumu 4:31
-Hemani wa ku Ezra (Banja la chi levi loyimba): II Mbiri 5:12
-Yudutuni (Otsogolera nyimbo mkachisi): I Mbiri 16:41-42
-Kora (Mlevi, otsogolera maimbidwe mkachisi): I Mbiri 6:22
-Natani (Mneneri wa Mulungu): II Samueli 12:1-14
-Ana a Kora (Banja la chi Levi loyimba): I Mbiri 6:22
-Zifi: I Samueli 23:19

## MAGAWO

Ndi zovuta kwa Buku la Masalmo kulika mmagawo chifukwa chaputala chilichonse chili ndi mutu wakewake. Masalmo ambiri ali ndi mitu imene imatiuza za zochitika pamene Masalmo amalembedwa komanso cholinga chake. Masalmo ena sanapatsedwe mitu choncho tikhoza kukhala ndi mafunso pachifukwa chimene amalembedwera ndi nthawi yake. Ife a Harvestime International Institute maphunziro athu tawatchula kuti "*Njira zatsopano zophunzirira Baibulo"* zimene zimapereka ndondomeko yophunzirira Masalmo machaputala onse. Choncho pali magawo asanu akulu a bukuli:

**Gawo loyamba: Masalmo 1-41**

| | |
|---|---|
| Chiwerengero cha Masalmo: | 41 |
| Chidule cha zonse: | Nkhani ya munthu, kudalitsika kwake, kugwa, ndi kubwerera. |
| Mawu otsogolera: | Munthu |
| Chiyamiko chotsiriza: | 41:13 |

**Gawo lachiwiri: Masalmo 42-72**

| | |
|---|---|
| Chiwerengero cha Masalmo: | 31 |
| Chidule cha zonse: | Israyeli, kugwa kwake, Momboli wake |
| Mawu otsogolera: | Chipulumutso |
| Chiyamiko chotsiriza: | 42:18-19 |

**Gawo lachitatu: Masalmo 73-89**

| | |
|---|---|
| Chiwerengero cha Masalmo: | 17 |
| Chidule cha nkhani: | Kachisi, kuyang'ana chitsogolo za kukhazikitsidwa kwake. |
| Mawu otsogolera: | Kachisi |
| Chiyamiko chotsiriza: | 89:52 |

**Gawo lachinayi: Masalmo 90-106**

| | |
|---|---|
| Chiwerengero cha Masalmo: | 17 |
| Chidule cha zonse: | Dziko: Madalitso ake ofunika, oyembekezeka, osangalasa |
| Mawu otsogolera: | Kusowa mpumulo, kukhala oyendayenda (zimene ndi mbali ya okhulupirira mudzikoli) |
| Chiyamiko chotsiriza: | 106:48 |

**Gawo lachisanu: Masalmo 107-150**

| | |
|---|---|
| Chiwerengero cha Masalmo: | 44 |
| Chidule cha zonse: | Mau a Mulungu |
| Mawu otsogolera: | Mau a Mulungu |
| Chiyamiko chotsiriza: | 150:6 |

**MAYESO ODZIYESA NOKHA**

1. Kodi analemba buku la Masalmondi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Masalmo.

3. Kodi buku la Masalmo amalembera kwa ndani?

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Masalmo.

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Masalmo.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli).

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

### ZIPANGIZO ZOYIMBIRA ZIMENE ZIKUPEZEKA MMASALMO

-Alamoti: Ichi chimayimba mokweza
-Gititi: Chofanana ndi Gitala zamakono
-Mahalati: Fuluti
-Mahalati Leyanoti: Fuluti yapadera yoimbidwa mu nthawi yachisoni
-Seminiti: Ichi chimakhala ndi zingwe zisanu.

### MITUNDU YA MASALMO

Masalmo wa malangizo: Mawu oti “Maskili” mu mutu akutanthauza izi ndi Masalmo amatha kugwiritsidwa ntchito pa chiphunzitso kapena malangizo. (Masalmo 32, 44, 52 ndi 78).

Masalmo olambira: Masalmo awa ukulu, chisomo, chikondi ndi mphamvu ya Mulungu ndi mutu waukulu. Onani Masalmo 8, 29.

Masalmo a Mbiri: Awa amabwereza mbiri yochitika ku mtundu wa Israyeli. Onani Masalmo 78,105 ndi 106.

Masalmo a Pembedzero: Awa amapereka mapempho kwa Mulungu. Onani Masalmo 86.

Masalmo oyamika: Chitsanzo chake ndi Masalmo 18.

Masalmo otemberera: Awa si Masalmo obwenzera munthu kapena olankhula molakwika. Monga mneneri wa Mulungu, wolemba akulankhula motsutsana ndi tchimo ndi adani a Mulungu. Onani Masalmo 35, 55, 58, 59, 69, 83, 109, 137 ndi 140.

Masalmo ovomereza: Chitsanzo ndi Masalmo 6, 32, 38, 51, 102, 130 ndi 143.

Masalmo a Mesiya: Masalmo awa kapena gawo la amenewa amanenera za kubweranso kwa Mesiya, Yesu Khristu. Ndipo akupezeka pa tsamba lotsatira kuti mutha kupitiliza kuphunzira.

### Uneneri wa Yesu mu buku la Masalmo

| **Masalmo** | **Kukwaniritsidwa kwake Mchipangano Chatsopano** |
|---|---|
| 8:3-8 | Ahebri 2:5-10; I Akorinto 15:27 |

| | |
|---|---|
| 72:6-17 | Izi zizachitika mtsogolo |
| 89:3-4,26, 28-29,34-37 | Machitidwe 2:30 |
| 109:6-19 | Machitidwe 1:16-20 |
| 132:12b | Machitidwe 2:30 |
| 45:6-7 | Ahebri 1:8-9 |
| 102:25-27 | Ahebri 1:10-12 |
| 110:1-7 | Mateyu 22:43-45; Machitidwe 2:33-35; Ahebri 1:13; 5:6-10; 6:20,7-24 |
| 2:1-12 | Machitidwe 4:25-28; 13:33; Ahebri 1:5; 5:5 |
| 16:10 | Machitidwe 2:24-31; 13:35-37 |
| 22:1-31 | Mateyu 27:35-46; Yohane 19:23-25; Ahebri 2:12 |
| 40:6-8 | Ahebri10:5-10 |
| 69:25 | Machitidwe 1:16-20 |

## CHAPUTALA CHA 21

MIYAMBO

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula amene analemba buku la Miyambo.
- Kudziwa kumene amalembera buku la Miyambo.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Miyambo.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Miyambo kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Miyambo.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Solomoni mwana wa mfumu Davide, analemba Miyambo yambiri. Izi zikupezeka mu I Mafumu 4:32 pamene akunena kuti Solomoni analankhula za Miyambo 3,000 mwa kuuzulidwa ndi Mulungu. Ina mwaa Miyamboyi yapatsidwa kwa ife mwa Mzimu Wooyera mbuku la Miyambo. Machaputala awiri a Miyambo analembedwa ndi wina amene ali ndi dzina lina: Aguri analemba chaputala cha 30 ndipo Lemueli analemba chaputala cha 31. Ina mwa Miyamboyi Solomoni ndiye amene anaika mmalo mwake. Zimene zikutanthauza kuti sanangolemba kokha komanso anaika mu mndandanda umene ulili Mbaibulo. Miyambo ina ya Solomoni inaikidwa mu ndandanda ndi anthu a mfumu Hezekiya.

AMENE AMAWALEMBARA: Israyeli, koma choonadi chake cha chikhalidwe ndi cha okhulupirira onse.

CHOLINGA: Chikupezeka pa Miyambo 1:1-6. Mutha kuwerenga mu Baibulo lanu. Mawu oyamba ku Miyambo akupezeka mu Mlaliki 12:8-14. Werengani ndimeyi Mbaibulo lanu.

VESI LOTSOGOLERA: Miyambo 3:13

MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI: Nzeru za umulungu ndi zofunikira kuti tikhale bwino ndi anzathu. Miyambo ndi mtolo wa mfundo za Mulungu kupita kwa munthu kuti zimutsogolere makhalidwe ndi anthu ena.

ANTHU OMWE AKUTCHULIDWAMO: Wolemba, Solomoni, Mfumu Lemueli, ndi Aguri, Mkazi kupatulapo Mulungu akutchedwa “mkazi wachilendo.” Chaputala chomalizira cha Miyambo chimalankhula zosiyana ndi iye pomutchula kuti “mkazi wangwiro” amene adziwa Mulungu.

## MAGAWO

Mawu oti “miyambo amatanthauza “zolankhula zachidule mmalo mwa mawu onse.” Vesi lililonse mu Miyambo ndi chidule choona cha choonadi chofunikira. Ndi zovuta kuonetsa magawo onse chifukwa chaputala komanso vesi lililonse limakamba za mutu wosiyana. Chifukwa chimene amalembera chidule kapena “miyambo” ndiko kugwiritsa ntchito luntha kuti tikumbukire choonadi cha uzimu bwino. Miyambo ndi chidule chachifupi koma chokhala ndi choonadi cha uzimu chapamwamba. Awa ndi magawo ake a bukuli:

I. Mawu oyamba: 1:1-6

II. Zomwe tingaphunzire pa luntha: 1:7-9:18

- A. Kufunika kwa kukhala ndi nzeru: 1:7-33
- B. Mphoto ya nzeru: 2:1-7:27
- C. Chiyamiko pa nzeru ya umulungu: 8:1-9:18

III. Miyambo ina ya Solomoni imene aniika mmalo mwake moyenera: 10:1-22:16

(Kuchokera chaputala ichi mpakana cha 25 pali zinthu zina zokhuza makhalidw a chikhristu amene ndi otsutsana ndi maganizo a uchimo ndi zotsatira zake.)

IV. Kubweretsa pamodzi miyambo ya anthu anzeru: 22:17-24:34

V. Miyambo ya Solomoni yosanjidwa bwino ndi alembi a Hezekiya: 25:1-29:27

- A. Zokhudza mafumu, mikangano, ndi ubale ndi anthu ena: 25:1-28
- B. Mawu okhuza chisilu, waulesi ndi wonena za ena: 26:1-28
- C. Kudzikonda wekha, chikondi chenicheni; zolakwitsa; maganizo a chisamaliro cha panyumba: 27:1-27
- D. Kusiyana pakati pa woipa ndi wolungama: 28:1-28
- E. Miyambo yokhuzana ndi dziko ndi makhalidwe ake: 29:1-27

VI. Miyambo ya Aguri: Chivomerezo ndi Malangizo: 30:1-33

VII. Miyambo ya Lemueli: Phunziro pa chilango ndi kudekha; chiyamiko pa mkazi wangwiro: 31:1-31

**MAYESO ODZIYETSA NOKHA**

1. Kodi analemba buku la Miyambo ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku l aMiyambo.

3. Kodi buku la Miyambo amalembera kwa ndani?

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Miyambo.

5. Lembani vesi lotsogolera la buku la Miyambo.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli).

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Mawu otsogolera pamene mukuwerenga Miyambo ndi awa:
   -Nzeru
   -Chidziwitso
   -Malangizo
   -Chitsiru
   -Kuopa, Kuopa Ambuye
   -Moyo
   -Lamulo/chilungamo/choipa
   -Mwana wanga

2. Werengani magulu awa amene akupezeka mbuku la Miyambo:
   -Zinthu zisanu zimene Mulungu amadana nazo: 6:16-19
   -Zinthu ziwiri zimene wolemba anampempha Mulungu: 30:7-9
   -Zinthu zinayi zimene sizikhutisidwa: 30:15-16
   -Zinthu zinzyi zimene dziko limavutika nazo: 30:21-23
   -Zinthu zinayi zapamwamba: 30:18-19
   -Zinthu zazing'ono zinayi koma zanzeru: 30:24-28
   -Atsogoleri anayi adziko: 30:29-31

3. Werengani mitundu ya anthu amene ndi zisilu mbuku la Miyambo:
   -Chisilu choonekeratu: 1:4,22; 7:7; 21:11
   -Chisilu chokanika: 1:7; 10:23; 12:23; 17:10; 20:3; 27:22
   -Chisilu cha mtudzu: 3:34; 21:24; 22:10; 29:8
   -Chisilu cha nkhanza: 17:21; 26:3; 30:22

4. Lembani zimene buku la Miyambo likuphunzitsa zokhudza mitu iyi:

| | | |
|---|---|---|
| -Dzina labwino | -Kudziletsa | -Mbuye/kapolo |
| -Unyamata ndi mwambo | -Chakumwa chaukali | -Mkwiyo/kusagwirizana |
| -Zokhuza malonda | -Ubwenzi | -Chuma/kusauka, umphawi |
| -Ukwati | -Mawu/lilime | -Mkazi |
| -Makhalidwe onyasa | -Nzeru ndi chisilu | -Kuzunzika |
| -Magulu oyipa | -Ulesi/ntchito | -Onyoza |
| -Nzeru | -Kudzikweza/kudzichepetsa | |

## CHAPUTALA CHA 22

## MLALIKI

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula amene analemba buku la Mlaliki.
- Kudziwa kumene amalembera buku la Mlaliki.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Mlaliki.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la Mlaliki kuchokera pamtima.
- Kutchula moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Mlaliki.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Solomoni

**OMWE AMAWALEMBERA:** Israyeli ndi onse okhulupirira makamaka achinyamata

**CHOLINGA:** Kutsindika pa kukhala mmoyo wopanda Mulungu.

**VESI LOTSOGOLERA:** Mlaliki 12:13

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Kukhala ndi moyo wopanda Mulungu kuli chabe.

**ANTHU OMWE AKUPEZEKAMO:** Solomoni. Palibenso wina amene atchulidwamo dzina.

### MAGAWO

I. Kufufuza kwa munthu poyesera zinthu: 1:1-2:26

A. Ndi nzeru: 1:12-18
B. Ndi zokhumba: 2:1-11
C. Kufananiza zinthu ziwiri: 2:12-23
D. Kuomba mkota koyamba pa choyeseracho: 2:24-26

II. Kufufuza pongozionerera zinthu: 3:1-5:20

A. Za mmene chilengedwe chimayendera: 3:1-22
B. Za mmene anthu amakhalira mdera: 4:1-16

C. Malangizo ake malingana ndi mmene amaonera zinthu ziwirizi: 5:1-17
    1. Pa chipembedzo: 5:1-7
    2. Pa mdera la anthu: 5:8
    3. Pa chuma: 5:9-17
D. Kuomba mkota kwachiwiri pa chiyesero: 5:18-20

III. Kufufuza pochita zabwino: 6:1-8:17

A. Pa mulingo wachuma: 6:1-12
B. Pa kutchuka: 7:1-22
C. Maphunziro: 7:23-8:1
D. Pa udindo: 8:2-14
E. Kuomba mkota pa chiyesero chachitatu 8:15-17

IV. Kufufuza kuonedwanso: 9:1-12:12

Solomoni akumaliza zokhudza moyo wopanda Mulungu (Zimene analankhula zikufanana ndi zambuyo pa mfundozi):

A. Ndi zopanda ntchito kotheratu: 2:11
B. Ndi wodzadza ndi zobwereza: 3:1-8
C. Ndi wodzadza ndi chisoni: 4:1
D. Ndi wowawa ndi wosokoneza: 2:17
E. Ndi wosakhazikika: 9:11-12
F. Ndi wopanda cholinga: 4:2,3; 8:15
G. Ndi wosachiritsika: 1:15
H. Ndi wosalungama: 7:15; 8:14; 9:11; 10:6-7
I. Umakhala pa mulingo wa mmene nyama imakhalira: 3:19

V. Kumaliza kufufuza; Kuomba mkota komaliza: 12:13-14

A. Tipange bwanji: 12:13
    1. Opa Mulungu: 12:13
    2. Sunga malamulo ake: 12:13
B. Chifukwa chiyani tipange chotero: 12:13b-14
    1. Ndi ntchito yonse yoyenera munthu: 12:13b
    2. Pakuti tsiku lina tidzaweruzidwa: 12:14

## MAYESO ODIYETSA NOKHA

1. Kodi ndi ndaani amene analemba buku la Mlaliki?

___

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Mlaliki.

___

___

___

3. Kodi buku la Mlaliki amalembera kwa ndani?

___

___

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Mlaliki.

___

___

___

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Mlaliki.

___

___

___

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenkweni kwa bukuli)

## KUPITLIZA KUPHUNZIRA

1. Werengani zinthu khumi zachabe izi:
   - -Nzeru ya munthu: 2:15-16
   - -Ntchito ya munthu: 2:19-21
   - -Cholinga cha munthu: 2:26
   - -Udani wa munthu: 4:4
   - -Chidziwitso cha munthu: 4:7
   - -Kutchuka kwa munthu: 4:16
   - -Kusakhutitsidwa kwa munthu: 5:10
   - -Kusilira kwa munthu: 6:9
   - -Kupusa kwa munthu: 7:6
   - -Njira za munthu zopezera zinthu: 8:10,14

2. Mawu oti "mtima" agwiritsidwa ntchito ka 40 mu buku la Mlaliki. Werengani bukuli ndi kudziwa chimene bukuli limakamba zokhudza mtima.

3. Lembani mndamndanda wa chuma cha Solomoni ndi zimene anakumana nazo mu chaputala 2. Onani mu vesi 10 akuti anali ndi "zonse zimene anazikhumba." Ndipo yang'anani zotsatira mu vesi 11: Zonse ndi chabe. Onani zimene anachita mkupangitsa kuti azindikira izi: Anaona, mkutembenuka, mkuyang'ana, ananena izi mumtima mwake.

4. Werengani mawu otsogolera mbuku la Mlaliki "chabe" amene agwiritsidwa ntchito ka 37.

5. Onani mawu awa, "pansi pa thambo." Uwu ndi moyo wa padziko pamene zauzimu sizikugwira ntchito. Mawuwa akupezeka ka 25. Pamene mukuwerenga Mlaliki, lembani zimene Solomoni analankhula komaliza za moyo opanda Mulungu (onani 2:11). Fananitsani moyowu ndi moyo umene umapezeka mwa Yesu Khristu.

6. Baibulo limakamba kuti Solomoni zinthu zonse ngati zili ndi tanthauzo pa moyo:

-Nzeru ya munthu: Mlaliki 1:16-18
-Mowa: Mlaliki 2:3
-Zosangalatsa: Mlaliki 2:1-3
-Kumanga zinthu: Mlaliki 2:4
-Munda wabwino ndi mosungira nyama: Mlaliki 2:4-6
-Kulakwa kwa munthu: Mlaliki 2:7
-Kugonana: I Mafumu 11:3
-Chuma: Mlaliki 2:7-8
-Kudziwika kutali: I Mafumu 10:6-7
-Nyimbo: Mlaliki 2:8
-Zolemba: I Mafumu 4:32
-Mphamvu za kunkhondo: I Mafumu 4:26 and 9:26
-Maluso a chibadwidwe: I Mafumu 4:33

## CHAPUTALA CHA 23

NYIMBO YA SOLOMONI

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula yemwe analemba Nyimbo ya Solomoni.
- Kudziwa kumene Nyimbo ya Solomoni amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera Nyimbo ya Solomoni.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la Nyimbo ya Solomoni kuchokera pamtima.
- Kutchula moyo ndi mfundo ya utumiki ya Nyimbo ya Solomoni.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Solomoni

**AMENE AMAWALEMBERA:** Israyeli ndi okhulupirira onse.

**CHOLINGA:** Kuonetsa ubale pakati pa Yesu ndi Mpingo monga mmene zimakhalira ubale wa ukwati.

**VESI LOTSOGOLERA:** Nyimbo ya Solomoni 8:7

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Chitsanzo cha chikondi cha umulungu pakati pa mamuna ndi mkazi ndi chizindikiro cha ubale wa pakati pa Khristu ndi Mpingo.

**AMENE AKUTCHULIDWAMO:** Solomoni amene akuimira mkwati (Yesu Khristu); Mkazi wa Sulemite amene ndi mkwatibwi (mpingo); ana akazi a ku Yerusalemu.

### MAGAWO

Kuti mumvetsetse bukuli mukuyenera kuzindikira kuti lili ndi muyeso wa matanthauzo okwana anayi:

1. Ndi chitsanzo cha ubale umene ukuyenera kukhala pakati pa mamuna ndi mkazi.
2. Ndi chitsanzo cha ubale wa Mulungu ndi anthu ake, Israyeli.
3. Ndi chitsanzo cha ubale wa pakati pa Khristu ndi mpingo.
4. Ndi chitsanzo cha ubale wa pakati pa munthu ndi Khristu ndi okhulupirira.

Bukuli lalembedwa ngati mchezo wa anthu awiri. Magawo abwino oti tingaphunzire ndi mchezowu. Amene amalankhula ndi dongosolo lake la mmene amalankhulira zili motere:

| **WOLANKHULA** | **VESI** |
|---|---|
| Mkwatibwi | 1:2-7 |
| Mkwati | 1:8-11 |
| Mkwatibwi | 1:12-14 |
| Mkwati | 1:15 |
| Mkwatibwi | 1:16-17; 2:1 |
| Mkwati | 2:2 |
| Mkwatibwi | 2:3-6 |
| Mkwati | 2:7 |
| Mkwatibwi | 2:8 kwa "ine" mu vesi 10 |
| Mkwati | 2:10 kuchokera ku mawu "dzuka" kufika vesi 15 |
| Mkwatibwi | 2:16-17; 3:1-4 |
| Mkwati | 3:5 |
| Mkwatibwi | 3:6-11 |
| Mkwati | 4:1-5 |
| Mkwatibwi | 4:6 |
| Mkwati | 4:7 ku mawu oti "kunja" mu vesi 16 |
| Mkwatibwi | 4:16 kuchokera ku mawu "lora" |
| Mkwati | 5:1 |
| Mkwatibwi | 5:2-8 |
| Akazi a ku Yerusalemu | 5:9 |
| Mkwatibwi | 5:10-16 |
| Akazi a ku Yerusalemu | 6:1 |
| Mkwatibwi | 6:2-3 |
| Mkwati | 6:4-9 |
| Akazi a ku Yerusalemu | 6:10 |
| Mkwati | 6:11-12 |
| Akazi a ku Yerusalemu | 6:13 |
| Mkwati | 7:1-9 |
| Mkwatibwi | 7:10-13; 8:1-3 |
| Mkwati | 8:4 |
| Akazi a ku Yerusalemu | 8:5 ku mawu oti "wokondedwa" |
| Mkwati | 8:5 kuchokera ku mawu oti "Ine" |
| Mkwatibwi | 8:6-8 |
| Mkwati | 8:9 |
| Mkwatibwi | 8:10-12 |
| Mkwati | 8:13 |

Mkwatibwi 8:14

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba Nyimbo ya Solomoni ndi ndani?

___

2. Tchulani cholinga chimene amalembera Nyimbo ya Solomoni.

___
___
___

3. Kodi Nyimbo ya Solomoni amalembera kwa ndani?

___
___

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya Nyimbo ya Solomoni.

___
___
___

5. Lembani Vesi Lotsogolera ya Nyimbo ya Solomoni.

___
___
___

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenkweni kwa bukuli).

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Werengani chikhalidwe cha mkwati molingana ndi mkwatibwi. Pali kufanana kwachionere kapena makhalidwe a uzimu a mkwati, Ambuye Yesu Khristu.

   -Wokondedwa wanga akunga mphoyo, pena mwana wa mbawala 2:9
   -Wokondedwa wanga ali woyera ndi wofiira, Womveka mwa zikwi khumi 5:10
   -Mutu wace ukunga golidi, woyengetsa 5:11
   -Ana a maso ace akunga nkhunda pambali pa mitsinje ya madzi 5:12
   -Masaya ace akunga citipula cabzyalamo ndiwo. Ngati mitumbira yoyangapo masamba onunkhira: 5:13
   -Milomo yace ikunga akakombo, pakukhapo madzi a nipa 5:13
   -Thupi lace likunga copanga ca minyanga colemberapo masafiro 5:14
   Zogwirika m'kamwa mwa golidi: Maonekedwe ace akunga Lebano, okometsetsa ngati Mikungudza; Miyendo yace ikunga zoimiritsa za mwala wonyezimira 5:15

2. Werengani makhalidwe a mkwatibwi molingana ndi mkwati. Kumbukirani kuti izi ndi zizindikiro cha choonadi cha uzimu. Kodi tingazifanizire bwanji kuuzimu monga "wokwatibwa" ndi Yesu Khristu.
   -Ngati sudziwa, mkaziwe woposa kukongola 8:1
   -Wokondedwa wanga ali kwa ine ngati cipukutu ca maluwa ofiira 1:14
   -Maso ako akunga a nkhunda 1:15
   -Ngati kakombo pakati pa minga 2:2
   -Tsitsi lako likunga gulu la mbuzi, Zooneka pa phiri la Gileadi 4:1
   -Mano ako akunga gulu la nkhosa zosengasenga 4:2
   -Milomo yako ikunga mbota yofiira 4:3
   -M'milomo yako, mkwatibwi, mukukha uci 4:11
   -Khosi lako likunga nsanja ya Davide anaimangira zida 4:4
   -Maere ako awiri akunga ana awiri a nswala obadwa limodzi 4:5
   -Mphukira zako ndi munda wamakangaza, Ndi zipatso zofunika, bonongwe ndi mphoka 4:13
   -Ndiwe kasupe wa m'minda, Citsime ca madzi amoyo, Ndi mitsinje yoyenda yocokera ku Lebano 4:15
   -Mapazi ako akongola m'zikwakwata; Nchito ya manja a mmisiri waluso 7:1
   -Pamcombo pako pakunga cikho coulungika; Pamimba pako pakunga mulu wa tirigu 7:2
   -Cosasowamo vinyo wosanganika 7:2
   -Mphuno yako ikunga nsanja ya ku Lebano; Imene iloza ku Damasiko 7:4
   -Walanda mtima wanga ndi diso lako limodzi, Ndi cinganga cimodzi ca pakhosi pako 4:9

## MAWU OYAMBA A MABUKU A UNENERI

Gulu lomalidza la mabuku a Mchipangano Chakale ndi mabuku a zolemberdwa za aneneri.

Anthu a Israyeli atakhala mtundu, anamaulidwa kuchokera ku ukapolo wa ku Aigupto ndipo Mulungu anawapatsa dziko lawo. Anapatsidwa malamulo oti adziwatsatira koma amakhala akulephera kudzipereka ku malamulowo.

Kupembedza mafano, nkhondo, kuchita zonyasa ndi kusasamala, Israyeli anayenera kukumbutsidwa mobwereza pa za cholinga cha moyo wawo. Choncho aneneri anali anthu amene anaitanidwa ndi Mulungu ndi cholinga choti abwenzeretse anthu kwa Mulungu. Ambiri mwa mabukuwa analembedwa munthawi imene mtundu wa Israyeli unagawanika kukhala maufumu awiri: Israyeli ndi Yuda.

Mabuku a uneneri ndi awa:

**Yesaya:** Bukuli limachenjedza za kubwera kwa chiweruzo pa Yuda chifukwa cha machimo awo pamaso pa Mulungu.

**Yeremiya**: Linalembedwa munthawi imene ufumu wa Yuda utangogwa. Limakamba za kubwera kwa chiweruza ndi change cha kugonjera kwa Nebukadinezara.

**Maliro**: Uku kunali kulira kwa Yeremiya pamene Yerusalemu anaonongedwa ndi Babulo.

**Ezekieli**: Chenjedzo loyamba pa kugwa kwa Yerusalemu ndi uneneri wa kutsogolo wobwenzeretsa.

**Danieli**: Mneneri Danieli anatengedwa koyambilira pamene Yuda anali wotetezedwa ndi kutengedwa kupita ku ukapolo wa ku Babulo. Bukuli lili ndi mbiri ya chiphunzitso komanso uneneri chimene ndi chofunika pofuna kumvetsa uneneri wa Mbaibulo.

**Hoseya**: Mutu waukulu wa bukuli ndi kusakhulupirika kwa Israyeli, chilango ndi kubwenzeretsedwa.

**Yoweli**: Amafotokoza za milili imene izaonekera mu chiweruzo cha mtsogolo.

**Amosi**: Pamene chuma cha kuthupi chachuluka, pamakhalanso kuonongeka kwa chikhalidwe. Amosi amawachenjeza ana Aisrayeli ndi maiko oyandikana nawo pa zachiweruzo cha Mulungu cha mtsogolo chifukwa cha machimo awo.

**Obadiya**: Chiweruza cha Mulungu pa Edomu, mtundu woipa wopezeka kumwera kwa Nyanja yakufa.

**Yona**: Iyi ndi nkhani ya mneneri Yona amene analalikira za kulapa ku Ninevi, mzinda wa ufumu wa Asuri. Bukuli limauluranso za chikondi cha Mulungu ndi dongosolo la kulapa kwa amitundu.

**Mika**: Uwu ndi uneneri wina wokhuza tchimo la Israyeli. Akuneneranso za malo amene Yesu azabadwirako koma patapita zaka zokwana 700 izi zisanachitike.
Nahumu: Amakamba za kubwera kwa chionongeka pa Ninevi chimene chinasiyidwa kwa zaka zokwana 150 kuchokera mkulalikira kwa Yona.

**Habakuku**: Limaulula za dongosolo la Mulungu lolanga mtundu wochimwa ndi wochimwitsitsa. Limaphunzitsa kuti "wolungama adzakhala ndi moyo ndi chikhuluiriro."

**Zefaniya**: Ichi ndi chiweruzo ndi kubwenzeretsedwa kwa Yuda.

**Hagai**: Bukuli limapempha Ayuda kumanganso kachisi atachedwetsedwa ndi adani kwa zaka zokwana 15.

**Zakariya**: Ili ndi pempho lopitilira la kumaliza kachisi ndi kudzikonzaso ku uzumu wawo. Limaneneranso za kubwera koyamba ndi kachiwiri kwa Khristu.

**Malaki**: Uneneri uwu ndi chenjezo pa kulowa pansi kwa moyo wa uzimu ndi kubwera kwa Yohane Mbatizi ndi Yesu.

Tchati lili pansipa likutiuza za nthawi imene aneneri anatumikira ndi kumene amatumikira.

| **Mneneri** | **Kumene ananenera** | **Masiku ake** |
|---|---|---|
| Yona | Asuri | Asanapite ku ukapolo (800-650) |
| Nahumu | Asuri | Asanapite ku ukapolo (800-650) |
| Obadiya | Edomu | Asanapite ku ukapolo (800) |
| Hoseya | Israyeli | Asanapite ku ukapolo (750) |
| Amosi | Israyeli | Asanapite ku ukapolo (750) |
| Yesaya | Yuda | Asanapite ku ukapolo (800-606) |

| | | |
|---|---|---|
| Yeremiya/Maliro | Yuda | Asanapite ku ukapolo (800-606) |
| Yoweli | Yuda | Asanapite ku ukapolo (800-606) |
| Mika | Yuda | Asanapite ku ukapolo (800-606) |
| Habakuku | Yuda | Asanapite ku ukapolo (800-606) |
| Zefaniya | Yuda | Asanapite ku ukapolo (800-606) |
| Ezekieli | Yuda | Ali ku ukapolo (606-536) |
| Danieli | Yuda | Ali ku ukapolo (606-536) |
| Hagai | Yuda | Utatha ukapolo (536-400) |
| Zakariya | Yuda | Utatha ukapolo (536-400) |
| Malaki | Yuda | Utatha ukapolo (536-400) |

## CHAPUTALA CHA 24

YESAYA

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula amene analemba buku la Yesaya.
- Kudziwa kumene wolemba buku amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Yesaya.
- Kuleba Vesi Lotsogolera la buku la Yesaya kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya utumiki ya buku la Yesaya.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Yesaya

**AMENE AMAWALEMBERA:** Yuda

**VESI LOTSOGOLERA:** Yesaya 53:6

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Kugalukira kumbweretsa chilango. Kulapa kumabwenzeretsa.

**ANTHU AMENE AKUTCHULIDWAMO:** Yesaya, Hezekiya

### MAGAWO

#### Gawo Loyamba

I. Uneneri wokhuza Yuda ndi Yerusalemu: 1:1-12:6

A. Chiyambi cha zonse: 1:1-31
B. Chaka cha chikwi cha madalitso ndi kudziyeretsa: 2:1-4:6
C. Chilango pa machimo a Israyeli: 5:1-30
D. Kuitanidwa ndi kupatsidwa ntchito kwa mneneri: 6:1-13
E. Uneneri wa Imanueli: 7:1-25
F. Uneneri wa kubwera kwa Asuri: 8:1-22
G. Kunenera ndi chenjezo la Mesiya: 9:1-21
H Chilango cha Asuri: 10:1-34

I. Kubwenzeretsedwa ndi madalitso: 11:1-16
J. Kulambira: 12:1-6

II. Uneneri wa kwa mitundu ya chilendo: 13:1-23:18
A. Babulo: 13:1-14:23
B. Asuri: 14:24-27
C. Filisitiya: 14:28-32
D. Moabu: 15:1-16:14
E. Damasiko: 17:1-14
F. Malire opitilira mtsinje wa Etiopiya: 18:1-7
G. Aigupto: 19:1-25
H. Aigupto ndi Etiopiya: 20:1-6
I. Duma: 21:11-12
J. Arabiya: 21:13-17
K. Chigwa cha masomphenya: 22:1-25
L. Turo: 23:1-18

III. Uneneri wokhazikitsa Ufumu: 24:1-27:13
A. Chitsautso: 24:1-23
B. Chikhalidwe cha Ufumu: 25:1-12
C. Umboni wa Israyeli wobwenzeretsedwa: 26:1-27:13

IV. Uneneri wa Yuda mogwirizana ndi Asuri:
A. Kugwa kwa Samariya: 28:1-13
B. Chenjezo kwa Yuda: 28:14-29
C. Chipsezo pa Zione: 29:1-4
D. Oopseza abalalika: 29:5-8
E. Chifukwa cha chiyeso: 29:9-16
F. Madalitso a chipulumutso chomaliza: 29:17-24
G. Chenjezo pa za ubale ndi Aigupto: 30:1-14
H. Chilimbikitso podalira thandizo la Mulungu: 30:15-31:9
I. Tsiku la Ambuye: 34:1-17
J. Dalitso la ufumu: 35:1-10

**Malo olumikizirapo**

Machaputala 36 mpaka 39 amakamba za kusintha kwa zochitika kuchokera ku Asuri kufika ku nthawi ya Babulo.

I. Kubwera kwa Senakalibu: 36:1-37:38
II. Kudwala ndi kuchira kwa Hezekiya: 38:1-22

III. Kufika kwa nthumwi za ku Babulo ndi ukapolo: 39:1-8

**Gawo Lachiwiri**

I. Chitonthozo pa ukapolo ndi lonjezo la kubwenzeretsa: 40:1-66:24
- A. Lonjezo la kubwenzeretsa: 40:1-11
- B. Gwero la chitonthozo: Chikhalidwe cha Mulungu: 40:12-31
- C. Chifukwa cha chitonthozochi: 41:1-29
- D. Wotonthoza: 42:1-25
- E. Zotsatira za chitonthozocho: 43:1-47:15
  - l. Mtundu ubwenzeretsedwa: 43:1-45:25
  - 2. Kugwa kwa mafano a Babulo: 46:1-13
  - 3. Kugwa kwa Babulo: 47:1-15
- F. Chilimbikitso cha chitonthozo kwa iwo amene atuluka ku ukapolo: 48:1-22

II. Chitonthozo pa a ku ukapolo ndi uneneri wa Yesu Momboli: 49:1-57:21
- A. Kuitana ndi ntchito: 49:1-26
- B. Kumvera ndi kukhulupirika: 50:1-11
- C. Chiombolo cha Israyeli: 51:1-52:12
- D. Nsembe ya uchimo ndi kukwezedwa: 52:13-53:12
- E. Kubwenzeretsedwa kwa Israyeli: 54:1-17
- F. Chipulumutso cha dziko lonse: 55:1-13
- G. Machenjezo ndi malonjezo: 56:1-57:21

III. Chitonthozo pa a ku ukapolo ndi uneneri wa ulemerero wamtsogolo wa Israyeli: 58:1-66:24
- A. Zotchinga pa kubwenzeretsa ndi machotsedwe ake: 58:1-59:21
- B. Ulemerero wa Yerusalemu munthawi ya Mesiya: 60:1-22
- C. Madalitso a Mesiya pa Israyeli ndi dziko lonse: 61:1-11
- D. Chikondi cha Mulungu pa Yerusalemu ndi zotsatira zake: 62:1-12
- E. Chigonjetso cha Khristu pa adani a Israyeli zinatsatira kuthokoza kwa chipulumutso cha a mitundu: 63:1-14
- F. Pemphero pa otsalawo: 63:15-64:12
- G. Yankho la Mulungu: 65:1-25
- H. Madalitso a ufumu wa Mesiya: 66:1-24

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Yesaya ndi ndani?

______________________________________________

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Yesaya.

______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________

3. Kodi buku la Yesaya amalembera kwa ndani?

______________________________________________
______________________________________________

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Yesaya.

______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Yesaya.

______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli).

**KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Buku la Yesaya limafanana ndi Baibulo motere:

   -Baibulo lilio ndi mabuku 66. Yesaya ali ndi machaputala 66.

   -Chipangano Chakale chili ndi mabuku 39 a mbiri yonse ya tchimo la Israyeli. Gawo loyamba la Yesaya lili ndi machaputala 39 amene amakamba za mutu womwewu.

   -Chipangano Chatsopano chili ndi mabuku 27 amene amakamba za utumiki wa Yesu Khristu. Gawo lomaliza la buku la Yesaya lili ndi machaputala 27 amene amakamba za mutu womwewu.

   -Chipangano Chatsopano chimayamba ndi utumiki wa Yohane Mbatizi. Gawo lachiwiri la Yesaya limayamba ndi ulosi wa utumiki wake.

   -Chipangano Chatsopano chimatha ndi nkhani ya kumwamba ndi dziko latsopano. Yesaya amatha ndi nkhani yomweyinso.

2. Yesaya amakambanso za ndime zofunikira izi:

   -Uneneri wokhawo wa chipangano chakale wokhudza za kubadwa kwa Yesu kwa mnamwali
   -Imodzi mwa mfundo zofunikira za Utatu wa Umulungu: 48:16
   -Chaputala chofunikira kwambiri cha chipangano chonse chakale: 53

3. Werengani mmene agwiritsira ntchito mawu oti "chipulumutso" mu buku la Yesaya. Mawuwa akupezeka ka 33 mbukuli.

4. Mitu yofunikira kuwerenga mu buku la Yesaya:

   -Mmene buku limaululira chikhalidwe cha Mulungu.
   -Mmene bukuli limaululira za utumiki wa Yesu.
   -Chitsautso.
   -Ufumu wa zaka chikwi wa Yesu.

5. Mawu otsogolera a uzimu mbuku la Yesaya:

   -Kutsutsika: 6:5 -Kupatulidwa: 6:8
   -Kuvomereza: 6:5 -Kutumidwa: 6:9 -Kuyeretsa: 6:7

# CHAPUTALA CHA 25

YEREMIYA

**ZOLINGA**:

Pakutha pa chaputalachi muyenera

- Kutchula amene analemba buku la Yeremiya.
- Kudziwa kumene buku la Yeremiya amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Yeremiya.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Yeremiya kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi mfundo ya Utumiki ya buku la Yeremiya.

## MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Yeremiya

**AMENE AMAWALEMBARA:** Yuda

**CHOLINGA:** Kuchenjedza pa zakubwera kwa chiweruzo cha ukapolo ndi kufunika kolapa.

**VESI LOTSOGOLERA:** Yeremiya 33:3 ndi 1:7-8

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI**: Kuonongeka kwa dziko ndi kubwerera mbuyo ndi zotsatira za kusamvera Mulungu.

**AMENE AKUTCHULIDWAMO:** Yeremiya

## MAGAWO

I. Mawu oyamba: Kuitanidwa kwa mneneri: 1:1-19

II. Uneneri wodzudzula Yuda ndi Yerusalemu: 2:1-45:5

A. Uneneri wa nthawi ya ufumu ua Yosiya ndi Yehoiyakimu: 1:1-20:18

l. Uneneri oyamba: Tchimo ndi kusayamika kwa mtundu: 2:1-3:5
2. Uneneri wachiwiri: Chionongeko cha kummawaw: 3:6-6:30
3. Uneneri wachitatu: Chiopsezo cha ukapolo: 7:1-10:25
4. Uneneri wachinayi: Kuphwanya pangano ndi chizindikiro cha nsempha: 11:1-13:27
5. Uneneri wachisanu: 14:1-17:27

a. Chilala: 14:1-15:21
b. Mneneri wosakwatira: 16:1-17:18
c. Chenjezo la pa Sabata: 17:19-27

6. Uneneri wachisanu mchimodzi: Chizindikro cha mwini nyumba: 18:1-20:18

B. Uneneri wa nthawi yaitali Yerusalemu asanagwe: 21:1-39:18

l. Chilango cha Zedekiya ndi anthu: 21:1-29:32
2. Ufumu wa Mesiya wamtsogolo: 30:1-33:26
3. Tchimo la Zedekiya ndi kumvera kwake kwa Rekabiti: 34:1-35:19
4. Chitsutso cha Yehoiyakimu: 36:1-32
5. Zimene Yeremiya anakumana nazo pamene anaziteteza: 37:1-39:18

C. Uneneri atagwa Yerusalemu: 40:1-45:5

l. Utumiki wa Yeremiya kwa otsalawo: 40:1-42:22
2. Utumiki wa Yeremiya ku Aigupto: 43:1-44:30
3. Uthenga wa Yeremiya kwa Baruki: 45:1-5

III. Uneneri wotsutsa amitundu: 46:1-51:64

A. Aigupto: 46:1-28
B. Filisitiya: 47:1-7
C. Moabu: 48:1-47
D. Amoni: 49:1-6
E. Edomu: 49:7-22
F. Damasiko: 49:23-27
G. Arabiya: 49:28-33
H. Elamu: 49:34-39
I. Babulo: 50:1-51:64

IV. Mawo utsiriza: Kugwa ndi kumasulidwa: 52:1-52:34

A. Kugwa ndi ukapolo wa Yuda: 52:1-30
B. Kumasulidwa: 52:31-34

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Yeremiya ndi ndani?

___

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Yeremiya.

___

___

___

3. Kodi buku la Yeremiya amalembera kwa ndani?

___

___

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Yeremiya.

___

___

___

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Yeremiya.

___

___

___

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli).

**KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Yeremiya anagwiritsa ntchito zitsanzo zooneka pofuna kuonetsera choonadi cha uzimu. Werengani zina mwa zitsanzo izi zimene anagwiritsa ntchito mmachaputala aperekedwawa:
   - Ntyole ya katungurume: l
   -Mphika wogaduka: l
   -Chingwe choonongeka: 13
   -Botolo lodazadza: 13
   -Chilala: 14
   -Chotengera cha oumba: 18
   -Botolo losweka: 19
   -Madengu awiri a mkuyu: 24
   -Bonds and bars: 27
   -Kugula munda: 32
   -Miyala yobisika: 43
   -Buku lomira mumtsinje: 51

2. Yeremiya anali mmeneli yekhayo Mbaibulo amene anakanizidwa kupempherera dziko lake: 7:16; 11:14; 14:11; 16:5

3. Mazunzo a Yeremiya amafananiranako ndi a Yesu motere:

   - Onse anazunzidwa ndi banja lakwao: Yeremiya 12:6, Yohane 7:5

   -Onse anapangidwa chipongwe ndi mzika za dera lawo: Yeremiya 11:21, Luka 4:28-30

   -Onse anadedwa ndi zipembedzo za dziko lapansi: Yeremiya 26:7-8, Yohane 11:47-53

   -Onse anakanidwa ndi atsogolera a Msunagoge: Yeremiya 20:1, Yohane18:13,24

   -Onse anathandizidwa ndi mafumu: Yeremiya 38:16, Luka 23:4

   -Onse analongosoledwa mofanana: Yeremiya 11:19, Yesaya 53:7

   -Onse anatunthuzidwa mu Yerusalemu: Yeremiya 9:1, Luka 19:41

   -Onse analosera za kuonongeka kwa Kachisi: Yeremiya 7:11-15, Mateyu 24:1-2

**CHAPUTALA CHA 26**

MALIRO

ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula amene analemba buku la Maliro.
- Kudziwa kumene buku la Maliro amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Maliro.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Maliro kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Maliro.

**MAWU OYAMBA**

**WOLEMBA:** Yeremiya

**KOMWE AMALEMBERA:** Ayuda amene anali akapolo ku Babulo

**CHOLINGA:** Kubweretsa kulapa pa kubwenzeretsedwa kwa uzimu.

**VESI LOTSOGOLERA:** Maliro 3:22-23

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Mulungu ndi wokhulupirika pa chiweruzo ndi chifundo.

**ANTHU OMWE AKUPEZEKAMO:** Yeremiya

**MAGAWO**

I. Mmene analili Yerusalemu: 1:1-22
Onani mavesiwa akuwaimba mulandu: 1:1,3,8,9,17

II. Chilango chochokera kwa Mulungu: Zitsatira zake azinena: 2:1-22

A. Mulungu adaononga khomo lililonse la Yuda: 2:1-2
B. Chipata komanso chiteteza chilichonse anaononga: 2:2
C. Chobonga chake cha chiweruza chinali pa dziko lonse: 2:4
D. Kachisi adagwa: 2:6
E. Adani a Yuda anapatsidwa ufulu woononga: 2:15-16

F. Matupi a anthu anapezeka munsewu wa Yerusalemu: 2:21-22

III. Mneneri wa Mulungu: 3:1-66

A. Chizunzo cha mneneri: 3:1-19
B. Chitsimikizo cha mneneri: 3:21-27, 31-33
C. Langizo la mneneri: 3:40-66

IV. Kupitiliza kulongosola za mmene zinalili: 4:1-22
A. Ana ali ndi ludzu: 4:4
B. Achinyamata akuzunzidwa: 5:13
C. Olemera animilira munsewu kumapempha: 4:5
D. Ana a mfumu amene anali amphamvu akhala ndi nkhope zosaonkeka bwino: 4:7,8
E. Akazi amaphika mkudya ana awo: 4:10
F. Aneneri komanso ansembe abodza anachititsidwa khungu munsewu: 4:14
G. Mfumu Zedekiya anatengedwa, mkuchititsdwa khungu mkupita naye ku ukapolo: 4:20

V. Pemphero la mneneri: 5:1-18

Linali pemphero la:

A. Chikumbukiro: 5:1
B. Kulapa: 5:16
C. Kuzindikira Mulungu: 5:19
D. Kukonzanso: 5:21

**MAFUNSO ODZIYETSA NOKHA**

1. Kodi analemba buku la Maliro ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Maliro.

3. Kodi buku la Maliro amalembera kwa ndani?

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Maliro.

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Maliro.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli).

**KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Imodzi mwa ndime zazikulu zokhuza kukhulupirirka kwa Mulungu ikupezeka mu Maliro 3:21-33. Onaninso II Timoteo 2:13.

2. Fananitsani Chibvumbulutso 18 ndi buku la Maliro. Mu Maliro, mnenei akulilira za kuonongeka kwa mzinda wa Mesiya wa Yerusalemu. Mu Chibvumbulutso 18, eni dziko akulilira za kuonongeka kwa mzinda wa wa chuma wa Babulo.

3. Werengani Maliro 5:16. Ndimeyi imakamba chidule cha chifukwa cha chiweruzo cha Mulungu. Munthawi ya 1000 Yesu asanabwere, Davide anakhazikitsa Yerusalemu ngati mzinda waukulu. Mulungu anaudalitsa mzindawu kwa zaka pafupifupi 400 ndipo anaulekerera kuti ufumu wa kummawa utengedwe ndi Asuri mu zaka za 721. Zifundo zake zonse zinali chabe, kuti anthu a Yuda chikhalire mu uchimo, chiwerizo chinawapeza.

4. A Yuda kwa zaka zambiri akhala akuwerenga Maliro chaka chilichonse mwezi wa khumi ndi chinayi wa Ab ndi cholinga chokumbukira za kuonongeka kwa kachisi woyamba mu 586 ndi kachisi wachiwiri mu zaka za 70 Yesu asanabadwe.

5. Amanena kuti Yeremiya anakhala panja pa chipata cha Yerusalemu kummawa kumalira malo otchedwa Gologota amene Yesu adafera patapita nthawi.

6. Yerusalemu amadzika ngatu mkazi. Lembani zimene zinachitika ku Yerusalemu ndi zifukwa zake. Onetsetsani kukhuzidwa kwake, ululu wake chifukwa cha ana ake, malingaliro ake ndi zikumbukiro zake zimene akuyenera kuchita nazo.

7. Lembani zimene mwaphunzira zokhuza Mulungu mu bukuli: Chikhalidwe chake, chiweruzo chake, ndi chifukwa chimene amachita zimene achita. Mwachitsanzo, Maliro 1:5 amakamba kuti Mulungu analora Yuda kuvutika chifukwa cha machimo ake ndipo anawatengera ku ukapolo chifukwa cha mphulupulu zake.

8. Mukuganiza kuti mchifukwa chiyani Mulungu amachita ndi uchimo mwa mtundu wotere? Ife timachita bwanji? Werengani chaputala cha 3 kuti "kuuseka" kwanu sikuzakhala "kulira."

## CHAPUTALA CHA 27

EZEKIELI

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Ezekieli.
- Kudziwa kumene buku la Ezekieli amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Ezekieli.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Ezekieli kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumuki ya buku la Ezekieli.

### MAWU OYAMBA

**WOLWMBA:** Ezekieli

**KUMENE AMALEMBERA:** Yuda

**CHOLINGA:** Ezekieli amachenjeza za ukapolo umene umabwera, ndipo ananenera kwa akapolo utatha ukapolowo.

**VESI LOTSOGOLERA:** Ezekieli 22:30

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Mulungu amalamulira zochitika za anthu kuti mitundu imudziwe Iye.

**ANTHU AMENE AKUPEZEKAMO:** Ezekieli.

### MAGAWO

**Gawo Loyamba: Uneneri Yerusalemu asanatchingidwe – Machaputala 1-24**

Patasala zaka zisanu mchimodzi Yerusalemu asanaonongedwe, Ezekieli anayamba uneneri wochenjeza Ayuda.

1. Kuitanidwa ndi kutumidwa: 1:1-3:27

    A. Masomphenya: 1:1-28
    B. Kuitanidwa: 2:1-3:27

II. Uneneri wotsutsa Ayuda ndi Yerusalemu: 4:1-24:27

- A. Chionongeko chiloseredwa: 4:1-7:27
    - l. Mwa zizindikiro ndi ziziwitso: 4:1-5:17
    - 2. Mwa uneneri: 6:1-7:27
- B. Machimo ndi chilango cha Yerusalemu: 8:1-11:25
    - l. Masomphenya a uchimo: 8:1-18
    - 2. Chilango: 9:1-11:25
- C. Ubwino wa chilango: 12:1-19:14
- D. Chenjezo lotsiriza asanagwe: 20:1-24:27

**Gawo Lachiwiri: Uneneri panthawi imene Yerusalemu anali wotetezedwa--Chaputala 25-32**

Mauneneriwa amapita kwa adani a Yuda.

I. Uneneri wa kwa mitundu yozungulira Yuda: 25:1-32:32

- A. Kwa Amoni: 25:1-7
- B. Kwa Moabu: 25:8-11
- C. Kwa Edomu: 25:12-14
- D. Kwa Filisitiya: 25:15-17
- E. Kwa Turo: 26:1-28:19
- F. Kwa Sidoni: 28:20-26
- G. Kwa Aigupto: 29:1-32:32

**Gawo Lachitatu: Uneneri Yerusalemu atatha kutchingidwa--Machaputala 33-48**

Uneneriwu ndi okhudza kubwenzeretsedwa kwa Yuda.

I. Zochitika zotsatira kukhazikitsidwa kwa ufumu: 33:1-39:29

- A. Woipa achotsedwa: 33:1-33
- B. Abusa achinyengo apereka mpata kwa abusa owona: 34:1-31
- C. Kubwenzeretsedwa kwa dziko: 36:1-15
- D. Kubwenzeretsedwa kwa anthu: 36:16-37:28
- E. Chiweruzo pa adani a Israyeli: 38:1-39:24
- F. Mtundu wobwenzeretsedwa: 39:25-29

II. Ufumu wa zaka chikwi: 40:1-48:35

A. Kachisi: 40:1-43:27
B. Kulambira: 44:1-46:24
C. Dziko: 47:1-48:35

**MAYESO ODZIYETSA NOKHA**

1. Kodi analemba buku la Ezekieli ndi ndani?

______________________________________________

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Ezekieli.

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

3. Kodi buku la Ezekieli amalembera kwaa ndani?

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Ezekieli.

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Ezekieli.

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

**KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Fananitsani Ezekieli 16 ndi buku la Hoseya.

2. Masomphenya odziwikiratu mu Chipangano Chakale ndi a chingwa cha mafupa owuma pa Ezekieli 37. Werengani chaputalachi.

3. Bukuli limalongosola limodzi mwa Kachisi wa Mbaibulo, kachisi zaka chikwi. Onani Ezekieli chaputala 40-48. Werengani machaputala ena a kachisi wa mbaibulo mmavesi awa:
   - Chihema cha Mose: Eksodo 40
   -Kachisi wa Solomoni: I Mafumu 6
   -Kachisi wa Zerubabele/Herodi: Ezara 6, Yohane 2
   -Kachisi wa thupi la Khristu: Yohane 2
   -Kachisi wa uzimu: Mpingo: Machitidwe 2
   -Kachisi wa chisautso: Chibvumbulutso 11

4. Ndi zofunika kuzindikira kuti Mulungu amalamulira zochitika ndi cholinga chimodzi: Kuti dziko limudziwe Iye amene ndi owona. Mawu achidule okuti, "azadziwa kuti ndine Yehova" akupezeka ka 70 mu bukuli. Lembani mzere kunsi kwa mawuwa pamene mukuwerenga Ezekieli kuti mudziwe cholinga cha Mulungu chikuchitika.

5. Ezekieli ndi mneneri wa masompheya. Analemba zoti pamene anali pakati pa akapolo, "kumwamba kunatsekuka, ndipo ndinaona masomphenya a Mulungu" (Ezekieli 1:1). Awa ndi masomphenya anaona:
   -Masomphenya a Akerubi: Ezekieli 1:1-3:13
   -Masomphenya a ulemerero ndi chisapembedzo: Ezekieli 8:1-11:25
   -Masomphenya a vinyo woyaka: Ezekiel 15:18
   -Masomphenya a mafupa owuna: Ezekiel 37:1-28

6. Mafanizo ndi zizindikiro zopezeka mbuku la Ezekieli:
   -Fanizo la ziwomba nkhanga ziwiri zimene zinaululu mfumu yak u Babulo ndi mfumu yak u Aigupto, nthambi yaikulu yofanana ndi Yehoiyakimu, mbewu ya mdziko inali Zedekiya; mphukira wosakhwima umaimira Mesiya: Ezekieli chaputala 17

   -Machaputala 20-23 alinso ndi mafanizo. Limodzi mwa ofunikira ndi la akazi awiri, Ahola ndi Aholiba. Amaimira kuonongeka kwa Israyeli ndi Yuda pakupembedza mafano.

   -Fanizo la Mphika wowila limaimira nyengo imene Yerusalemu anagonjetsedwa ndi mtundu wa ku Babulo: Ezekieli 11:1-13

-Mitengo iwiri, umodzi Yuda ndi wina Israyeli, zikuoneka zolumikizana pansi pa Mfumu ya mbusa: Ezekieli 37:1-28

## CHAPUTALA CHA 28

DANIELI

**ZOLINGA**:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Danieli.
- Kudziwa kumene wolemba amawalembera.
- Kutchula cholinga cha buku Danieli.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Danieli kuchokera pamtima.
- Kuchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Danieli.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA**: Danieli

**OMWE AMAWALEMBERA:** Ayuda a ku ukapolo

**CHOLINGA:** Kuonetsa kuti Mulungu amalamulira zochita za anthu.

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Mulungu ali wolamulira ndipo amachitira ulemu iwo amene amchitira ulemu.

**AMENE AKUTCHULIDWAMO:** Danieli

### MAGAWO

I. Mawu oyamba a mmene zinthu zinalili: Zifukwa zimene Danieli anapambanira: 1:1-21

II. Masomphenya ndi zochitika mu nthawi ya Nebukadinezara: 2:1-6:28

A. Fano ndi tanthauzo lake: 2:1-49
Maufumu anayi a dziko:
1. Babulo: 606 B.C.
2. Medo-Peresiya: 538 B.C.
3. Grecian: 330 B.C.

4. Chiroma: 63 B.C.

B. Moto woyaka: 3:1-30
   1. Lamulo la mfumu: 3:1-7
   2. Kukhazikika kwa anthu a Mulungu: 3:8-23
   3. Chiweruzo ndi chipulumutso: 3:24-30

C. Masomphenya a mtengo wa Nebukadinezala ndi tanthauzo lake: 4:1-37
   1. Maloto: 4:1-18
   2. Tanthuazo: 4:19-27
   3. Kukwaniritsidwa: 4:28-37

D. Phwando la Belisazara: 5:1-31
   1. Phwando: 5:1-4
   2. Chiweruzo: 5:5-9
   3. Kufufuza womasulira: 5:10-16
   4. Kumasulira: 5:17-29
   5. Kukwaniritsidwa: 5:30-31

E. Danieli apulumuka ku dzenje la mikango: 6:1-28
   1. Lingaliro loipa: 6:1-9
   2. Zimene Danieli anachita: 6:10-20
   3. Kupulumuka ku dzenje: 6:21-28

III. Masomphenya a Belisazara, Dariyo ndi Kupro: 7:1-12:13

A. Zorombo zinayi ndi tanthauzo lake: 7:1-28
   1. Zinatuluka mu Nyanja yaikulu: 7:1-3
      (a) Chirombo ngati nkango: Babulo: 7:4
      (b) Chirombo ngati chimbalangondo: Medo-Peresiya: 7:5
      (c) Chirombo ngati nyarugwe: Giriki: 7:6
      (d) Chirombo choopsa: Aroma: 7:7
   2. Nyanga yaing’ono (wokana Khristu): 7:8
   3. Ufumu wa Mulungu: 7:9-14
   4. Tanthauzo lake: 7:15-28

B. Tanthauzo la nkhosa yamphongo ndi tonde: 8:1-27
   1. Mawu oyamba: 8:1-2
   2. Masomphenya: 8:3-14
      (a) Nkhosa yamphongo ndi Medo-Peresiya: 8:3-4
      (b) Tonde ndi Giriki: 8:5-14
   3. Vumbulutso lokhuza Antiokasi Epifane ndi wokana Khristu: 8:15-27

C. Sabata zisanu ndi ziwiri: 9:1-27
   1. Mawu oyamba: 9:1-2

2. Pemphero: 9:3-19
3. Sabata zisanu ndi ziwiri: 9:20-27

D. Kukonzekera vumbulutso lotsiriza: 10:1-21
1. Mawu oyamba: 10:1-3
2. Munthu wovala chovala choyera: 10:4-6
3. Zimene Danieli anachita: 10:10-12
4. Mkangano wa Gabriyeli ndi karonga wa Aperesi: 10:13
5. Chifukwa chimene mngelo anabwera: 10:14-21

E. Masomphenya a zochitika kuchokera pa Dariyo mpaka kumapeto a nthawi: 11:1-12:13
1. Vumbulutso la zimene zili mkudza: 11:1-12:3
2. Lamulo la kusindikiza buku: 12:4
3. Kulankhula komaliza ndi mnthenga: 12:5-13

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Danieli ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Danieli.

3. Kodi buku Danieli amalembera kwa ndani?

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Danieli.

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Danieli.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenkweni kwa bukuli)

**KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Ezekieli amafanana ndi Danieli. Amamfaniziranso ndi Nowa komanso Yobu. Ezekieli 14:14. Amafaniziranso nzeru za Danieli: Ezekieli 28:3. Yesu adakambapo za Danieli: Mateyu 24: 15.

2. Danieli amakamba za pemphero lalikulu la kuvomereza kwa munthu: 9:3-19

3. Zinthu zofunika kwa Danieli:
   -Phwando lochititsa chidwi la Mbaibulo: 5
   -Malongosoledwe a Atate mu chipangano chakale: 7:9-14
   -Buku lokhalo limene limakamba za Gabriyeli ndi Mikayeli (Angelo awiri a kumwamba) 10:13; 12:1
   -Chifukwa chimene nthawi zina pemphero limatchingidwa: 10:10-13
   -Malongosoledwe onse a wokana Khristu: 7:7-27; 8:23-25; 9:26; 11:36-45

4. Sabata zokwana 70 zikupezeka mu Danieli 9:24-27, agwiritsa nthcito mawu oti “sabata” kutanthauza nthawi ya zaka zokwana 70. Choncho ngati pali ma 70 okwana asanu ndi awiri, ndiye kuti pali zaka 490. Magawidwe ake a zakazi ali motere:

   -Sabata 7 kapena zaka 49 zinayamba palamulo lomanga Yerusalemu munthawi ya Ezara ndi Nehamiya.

   -Sabata 62, kapena zaka 434 zinayamba pamene amamanga chiapata cha Yerusalemu mpaka mu nthawi ya kupachikidwa pamene Yesu anachotsedwa

   -Ulamuliro wa amitundu, zaka zosadziwika zinapezeka patatha sabata ya 69. Apapa ndiye kuti tili mu nthawi imeneyi, kudikira kubweranso kwa Yesu.

   -Sabata ya 70, zaka 7 zimene sizinayambe zimene Mulungu azathana ndi Israyeli. Izi zizayamba pamene wokana Khristu azakhala ndi mphamvu ndipo chisautso chidzayamba. Izi zizakhala chiyambi cha nthawi ya mavuto imene Danieli 12:1 amaitchula kuti chisautso chachikulu monga chikupezeka mu Chibvumbulutso.

5. Kudzuka komanso kugwa kwa mafumu a dziko lapansi zikupezeka mu Danieli chaputala 2, 7, ndi 8 ndipo chidule chili pa tsamba la mmusili:

## CHAPUTALA CHA 29

HOSEYA

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Hoseya.
- Kudziwa kumene buku la Hoseya amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Hoseya.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Hoseya kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Hoseya.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Hoseya

**KUMENE AMALEMBERA:** Ufumu wa kumpoto wa Israyeli.

**CHOLINGA**: Kuchenjeza Israyeli za machimo awo ndi kuwabweretsa kwa Mulungu

**VESI LOTSOGOLERA:** Hoseya 4:1

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Zimene timakumana nazo zimatithandiza kudziwa ndi kukhala ndi chifundo.

**ANTHU OPEZEKAMO:** Hoseya, Gomeri, Yezeli, Lo-Ruhama, Lo-Ami

### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1

II. Zizindikiro za chitsanzo: 1:1-2:23

A. Israyeli akanidwa: Ukwati wa Hoseya ndi kubadwa kwa ana ake.
1. Alamulidwa kutenga mkazi amene ndi hule: 1:2-3
2. Yezereli akuimira kugwa kwa ufumu wa Yehu: 1:4-5
3. Lo-ruhama: Mulungu sadzakhalanso ndi chifundo pa Israyeli: 1:6-7
4. Lo-Ami: Lankhula zokana Israyeli: 1:8-9

B. Israyeli atonthozedwa: 1:10-11
C. Israyeli alangidwa: 2:1-13
    1. Chidzudzulo cha makhalidwe ochima: 2:1-7
    2. Chilango chilongosoledwa: 2:8-13
D. Israyeli abwenzeretsedwa: 2:14-23
    1. Lonjezo la kutembenuka: 2:14-17
    2. Kukonzanso pangano: 2:18-23

III. Kuombola mkazi wa chigololo: 3:1-5
A. Zimene Hoseya anakumana zano: 3:1-3
B. Zimene Israyeli anakumana nazo mobwereza: 3:4-5

IV. Chigonjetso pa chikondi cha Umulungunpa kubwenzeretsa mtundu wolapa: 4:1-14:9
A. Uchimo wa Israyeli: 4:1-19
    l. Lamulo la onse: 4:1-5
    2. Umbuli wochita mwadala: 4:6-11
    3. Mafano: 4:12-19
B. Kunyasidwa kwa Umulungu: 5:1-15
    1. Uchimo wa ansembe, anthu ndi akaronga: 5:1-7
    2. Chiweruzo chitsatapo: 5:8-15
C. Kulapa kwa otsalawo: 6:1-3
    1. Kubwerera koma opanda kulapa kwa mumtima: 6:1-3
D. Zimene Mulungu anachita: 6:4-13:8
    1. Mulungu sanyengedwa: 6:4-11
E. Chinyengo cha boma lolamulira: 7:1-7
F. Chinyengo cha maboma achilendo: 7:8-16
G. Zotsatira za chinyengo cha maboma: 8:1-14
H. Uchimo ndi chilango chake: 9:1-9
I. Monga Mulungu anasankha Israyeli ndipo anakhala: 9:10-17
J. Mafumu awamba ndi milungu: 10:1-3
K. Chilungamo chiosanduka chokhupha: 10:4-5
L. Asuri agwiritsidwa ntchito ngati chiweruzo: 10:6-7
M. Chiopsezo cha chiweruzo: 10:8
N. Kukana pa kugalukira: 10:9-15
O. Kusayamika pa chikondi cha Mulungu: 11:1-7
P. Njira za Israyeli za kanani: 11:12-12:14
Q. Kupembedza mafano ndiye maziko a chionongeko: 13:1-8

V. Kubwenzeretsedwa kotsiriza: 13:9-14:9

A. Kusadalira Mulungu: 13:9-1.
B. Kupempha kuti alape: 14:1-3
C. Lonjezo la machiritso Mawu otsiriza—Israyeli alapa, Mulungu amva: 14:4-9

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Hoseya ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Hoseya.

3. Kodi Hoseya amalembera kwa ndani?

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Hoseya.

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Hoseya.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Werengani II Mafumu 14:23-17:41. Ndimeti imakamba za nthawi imene Hoseya ananenera.

2. Zitsanzo za machimo amene Mulungu anawagwiritsa ntchito mu buku la Hoseya:
   -Mkazi wachigololo: 3:1
   -Woledzera: 4:11
   -Ng'ombe yaikazi yokugwa: 4:16
   -Gulu la ankhondo akuba: 6:9
   -Achigololo: 7:4
   -Chophikira chofuka utsi: 7:7
   -Mkate wophikidwa theka: 7:8
   -Nkhunda yopusa: 7:11
   -Uta wachinyengo: 7:16
   -Kumezedwa: 8:8
   -Chotengera: 8:8
   -Mbizi ya kuthengo: 8:9

3. Mchifukwa chiyani Mulungu amauza munthu kuti akwatire hule? Pali zifukwa zambiri: Choyamba pakukwatira mkazi wosakhulupirira Hoseya anamvetsa ululu mu mtima mwake. Anthu a Mulungu amachita chigololo cha uzimu. Kachiwiri ukwati wa Hoseya unali chitsanzo choonetsera uthenga a Mulungu kwa Israyeli. Kachtatu, Mulungu analmulira Hoseya kuti awatchule ana ake mayina amene amaimira chilango ndi kubwenzeretsedwa kwa Israyeli mtsogolo.

4. Mndandanda wa machimo a Israyeli mbuku la Hoseya: Bodza 4:1; Umbava: 7:1, Kupha: 5:2, Kuzunza: 12:7, Kulowelera: 11

5. Hoseya anagwiritsa ntchito mawu ovuta pakupita kwawo ndi uthenga umene Mulungu anampatsa. Anagwiritsa ntchito mawu oti mkazi wosakhulupirika ka 14, wokondedwa ka 6, hule ka 4, mawu ena oimira wachigololo ka 6, uhule kawiri, mchitidwe wogonana kawiri ndi mchitidwe wa uhule kamodzi.

6. Hoseya anagwiritsa ntchito zizindikiro zitatu pofuna kutsindika ubale wa Mulungu ndi anthu ake: Chitsanzo cha atate ndi mwana (11:1); mamuna ndi mkazi wake (2:16) ndi mfumu ndi anthu ake (13:10).

## CHAPUTALA CHA 30

YOWELI

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula yemwe analeba bukui la Yoweli.
- Kudziwa kumene wolemba buku la Yoweli amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Yoweli.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Yoweli kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Yoweli.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Yoweli

**AMENE AMAWALEMBERA:** Yuda

**CHOLINGA:** Kuchenjeza Ayuda pa machimo awo ndi kuwapempha kuti alape ndi kulolera malingaliro a Mulungu pa dziko lawo. Chiweruzo choyamba (1:2-2:17) chikutsatira chiweruzo chachikulu (2:18-3:21).

**VESI LOTSOGOLERA:** Yoweli 2:28-29

### MAGAWO

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Ngakhale pakati pa kukonza chiweruzo, Mulungu amakhala ndi dongosolo la madalitso pa anthu ake.

**ANTHU OPEZEKAMO:** Yoweli

### MAGAWO

I. Mneneri awonetsedwa: 1:1

II. A type of the "tsiku la Ambuye": 1:2-20
  A. Mulili wa dzombe: 1:2-7

B. Anthu alimbikitsidwa kulapa: 1:8-20
   1. Akulu (atsogoleri): 1:2
   2. Akulu ndi ang'ono: 1:2-3
   3. Woledzera: 1:5-7
   4. Mtundu wonse: 1:8-12
   5. Ansembe (atumiki): 1:9
   6. Mwini munda: Wogwira ntchito: 1:10-12

C. Pempho kuti alape: 1:13-14

D. "Tsiku la Yehova": Pemphero la chifundo: 1:15-20 Onani kuti tikuyenera . . .
   1. Kumva: 1:1
   2. Kudzuka: 1:5
   3. Kulira: 1:8
   4. Kuchita manyazi: 1:11
   5. Kuvala ziguduli: 1:13
   6. Kupatula kusala kudya: 1:14
   7. Kufunsa msonkhano wa kulapa: 1:15
   8. Kulira kwa Ambuye: 1:14,19

III. "Tsiku la Ambuye": 2:1-32

A. Kubwera kwa asilikali a kummawa: 2:1-10

B. Atsilikali a ku Hamagedoni: 2:11

C. Otsalawo olapa: 2:12-17
   1. Ng'ambani mitima osati chovala: 2:12-14
   2. Kulapa kwenikweni ndi pemphero lowona: 2:15-17

D. Yankho la Mulungu kwa osalawo: 2:18-29
   1. Kulapa: 2:18
   2. Kubwenzeretsa: 2:19-27
   3. Kutsanulira Mzimu: 2:28-29
   4. Chiweruzo pa oyipa: 2:20,30-31
   5. Otsala athawira ku Zione: 2:32

E. Zizindikiro za "tsiku la Ambuye": 2:30-32

IV. Chiweruzo pa amitundu: 3:1-16

A. Israyeli abwenzeretsedwa: 3:1

B. Mitundi iweruzidwa: 3:2-3

C. Fonisiya ndi Afilisiti aweruzidwa: 3:4-8

D. Mitundu aibetchera nkhondo ndi chiweruzo: 3:9-16

V. Uneneri wa ufumu wa madamitso: 3:17-21

A. Kukwezedwa kwa Yerusalemu: 3:17
B. Yuda achita bwino: 3:18
C. Kuonongeka kwa Aigupto ndi Edomu: 3:19
D. Kukwezedwa kwake kwa Yerusalemu: 3:20-21

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Yoweli ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Yoweli.

3. Kodi buku la Yoweli amalembera kwa ndani?

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Yoweli.

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Yoweli.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Yoweli anali mneneri wiyamba kugwiritsa ntchito mawu "tsiku la Ambuye." Mutuwu umakamba za zaka zisanu za chisautso chimene chidzadza pa dziko lapansi mu nthawi yotsiriza ya chiweruzo cha Mulungu. Werengani za "tsiku la Ambuye" mu Yoweli 1:15; 2:1,11,31; and 3:14.

2. Ichi ndi chidule cha nyengo ya Yuda molingana ndi Yoweli:

-Anaonongedwa ndi adani: 1:4,6-7
-Vinyo watsopano achotsedwa: 1:6,10
(Yesu ndiye vinyo; anthu anachotsedwa kwa vinyo, maziko a moyo.)
-Zokolola zitayika: 1:11-12
-Adataya chikondi choyamba: 1:8
-Zopereka zichotsedwa: 1:9
-Atumiki alira: 1:9
-Chimwemwe chichoka: 1:12,16
-Njala yak u uzimi: 1:17-20

3. Izi ndi zopulumukira zimene Mulungu adampatsa Yoweli:

-Kulapa: 2:12-13
-Kuzindikira Mulungu: 2:26
-Ubale (kufika podziwa Mulungu): 2:27
-Kuopa Mulungu: 2:27 ("Ine ndine Ambuye; palibe wina oposa ine")

4. Ngati Yuda akanalapa, izi zikanachitika:

-Kubwenzeretsa: 2:25
-Chitsitsimutso ndi kukonzanso: 2:23
-Vumbulutso: 2:28-31
-Chiombolo (chipulumutso) ndi kumasulidwa (mamasulidwe): 2:32
-Kukonzekera (kukonzeka, osachita mayazi): 3:13-14

## CHAPUTALA CHA 31

AMOSI

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula amene analemba buku la Amosi
- Kudziwa kumene wolemba buku la Amosi amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Amosi.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Amosi.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Amosi.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA: Amosi**

**AMENE AMAWALEMBERA:** Israyeli

**CHOLINGA:** Kuitanira Israyeli kuti abwerere kwa Mulungu.

**VESI LOTSOGOLERA:** Amosi 4:12

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Kuitana amitundu kulipode, "Konzekerani kukumana ndi Mulungu wanu."

**AMENE AKUTCHULIDWAMO:** Amosi

### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1-2

II. Chiweruzo pa mitundu yozungulira Israyeli: 1:3-2:3

A. Damasiko 1:3-5
B. Filisitiya: 1:6-8
C. Foyinisiya: 1:9-10
D. Edomu: 1:11-12
E. Amoni: 1:13-15
F. Moabu: 2:1-3

III. Chiweruzo cha Yuda ndi Israyeli: 2:4-16

A. Pa Yuda: 2:4-5
B. Pa Israyeli: 2:6-16

IV. Lamulo la Mulungu pa banja la Yakobo: 3:1-9:10

A. Zinthu zitatu za chiweruzo: 3:1-6:15
    l. Chiweruzo ndichoyenera: 3:1-10
    Chiweruzo mchilamulo: 3:11-15
    2. Chiweruzo ndichoyenera: 4:1-11
    Chiweruzo mchilamulo: 4:12-13
    3. Chiweruzo ndichoyenera: 5:1-15
    Chiweruzo mchilamulo: 5:16-6:14
B. Zizindikiro za masomphenya a zilango: 7:1-9:10
    l. Dzomba: 7:1-3
    2. Chilala: 7:4-6
    3. Chipangizo cha umboni wa zochitika: 7:7-17
    4. Dengu la zipatso: 8:1-14
    5. Ambuye aimilira pa guwa: 9:1-10

V. Chiyembekezo cha tsogolo lowala: 9:11-15

A. Kubwera kwa Yesu ndi kukhazikitsa ulamuliro wa Mesiya: 9:11-12
B. Kuchita bwino mu zaka chikwi: 9:13
C. Israyeli abwenzeretsedwa: 9:14-15

**MAYESO OZIYETSA NOKHA**

1. Kodi analemba buku la Amosi ndi ndani?

___

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Amosi.

___
___
___

3. Kodi buku la Amosi amalembera kwa ndani?

___
___

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Amosi.

___
___
___

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Amosi.

___
___
___

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli).

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Maso atcheru a Mulungu amaona:

-Tchimo lakale: 1:3
-Zimene munthu achita: 1:6
-Malonjezo osweka: 1:9
-Udani wobisika wa muntima: 1:11
-Zokhumba ndi zolinga: 1:13
-Malingaliro ndi machimo osungidwa: 2:1

2. Yoweli akukamba za zinthu zisanu za tsiku la Ambuye:

-Mfumu: 9:11
-Mitundu: 9:12
-Dziko: 9:13
-Anthu: 9:14
-Nthaka: 9:15

3. Gawo loyamba la buku la Yoweli lili mkati mwa malemba awiri a nkango wobuma 1:2 and 3:8. Nkango koyamba ukukana machimo a dziko la amitundu (1:3-2:3), kenako dziko la Israyeli (Kumwera kwa ufumu wa Yuda 2:4-5 ndi kumpoto kwa ufumu wa Israyeli 2:6, 16), ndipo komaliza ndi kuwaika pamodzi mmawu amaliza (3:1-2).

4. Lembani mitundu yonse imene ikupezeka mu buku la Yoweli, ndi chifukwa chimene akulandira chilango ndi chiweruza cha mtsogolo:

| **Mtundu** | **Chifukwa cha chilango** | **Chiweruzo cha mtsogolo** |
|---|---|---|

## CHAPUTALA CHA 32

OBADIYA

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula amene analemba buku ala Obadiya.
- Kudziwa kumene wolemba Obadiya amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Obadiya.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Obadiya kuchoketa pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Obadiya.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Obadiya

**OMWE AMAWALEMBERA:** Mtundu wa Edomu

**CHOLINGA:** Kuchenjeza za chilango cha Mulungu pa tchimo.

**VESI LOTSOGOLERA:** Obadiya 1:4

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Mulungu amatsitsa odzikweza ku tchimo.

**ANTHU OPEZEKAMO:** Obadiya

### MAGAWO

I. Tsogolo la Edomu alilosera: 1:1-9

A. Uthenga wochokera kwa Ambuye wopita kwa Edomu kudzera kwa Obadiya: 1:1
B. Edomu osagonjetsedwa adzagonjetsedwa: 1:2-4
   1. Edomu adzachepetsedwa ndi kunyozedwa pakati pa amitundu: 1:2
   2. Afzanyengedwa ndi kudzitama: 1:3
   3. Adzatsitsidwa pansi ndi Mulungu: 1:4
C. Edomu adzatengedwa ndi kusiyidwa kotheratu: 1:5-9
   1. Akuba ndi mbava: 1:5
   2. Chuma chobisika chinafunidwa: 1:6
   3. Edomu anyengedwa ndi kukodwa: 1:7

4. Anthu anzeru awonongedwa: 1:8
5. Anthu amphamvu achita mantha pa kuchotsedwa kwa Edomu: 1:9

II. Choyambitsa chiwawa: 1:10-14

A. Chiwawa: 1:10
B. Maganizo a udani: 1:11
C. Chimwemwe ndi zowawa za ena: 1:12
D. Kudzitaandira pa zowawa za ena: 1:12
E. Kuwononga anthu a Mulungu: 1:13
F. Kupewa kuthawa kwa osakhazikika: 1:14
G. Kudzipereka: 1:14

III. "Tsiku la Ambuye" pamene chiweruzo chidzabwera pa a mitundu osadziwa Mulungu, osati kwa Edomu yekha: 1:15-21

A. Chiweruzo pa Edomu ndi mitundu ina: 1:15-16
1. Monga mmene wachitira udzalandiranso: 1:15
2. Monga mmene anachitira adzalandiranso: 1:16

B. Chipulumutso pa nyumba ya Yakobo: 1:17-20
1. Chipumulutso ndi chiyero pa phiri la Zione: 1:17
2. Nyumba ya Yakobo, Yosefe ndi Esau: 1:18
3. Katundu: 1:19-20

C. Ulamuliro wa zaka chikwi wa Yesu: 1:21

**MAYESO ODZIYETSA NOKHA**

1. Kodi analemba buku la Obadiya ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Obadiya.

3. Kodi wolemba buku la Obadiya amalembera kwa ndani?

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Obadiya.

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Obadiya.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Ma uneneri ena anayi a Edomu werengani mabuku awaw:

-Yesaya 34:5-15
-Yeremiya 49:7-22
-Ezekieli 25:12-14; 35:1-5
-Amosi 1:11-12

2. "Edomu" amatanthauza kuffira. A Edomu anachokera kwa Esau. Kuti mudziwe za mbiri yawo onani Genesis 36; Eksodo 15:15; Numeri 20:14; 20-21; ndi Deuteronomo 23:7-8.

3. Awa ndiwo machimo enieni amene akupezeka mbuku la Obadiya mu machaputala awa:

-Ziwawa: 10
-Malingaliro a udani: 11
-Chimwemwe ndi zowawa za ena: 12
-Kudzikweza pa mavuto a ena: 12
-Kuononga anthu a Mulungu: 13
-Kupewa kuthawa kwa osakhazikika:
-Kudzipereka: 14

4. Mawu otsogolera a mbuku la Obadiya:

-Atero Ambuye
-Ndi za
-Imvani mawu awa
-Ambuye anandionetsa

## CHAPUTALA CHA 33

YONA

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Yona
- Kudziwa amene wolemba buku amawalembera
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Yona.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Yona kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Yona.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Yona

**AMENE AMAWALEMBERA:** Mtundu wa ku Ninevi kuwachenjeza za zotsatira za kusamvera Mulungu.

**CHOLINGA:** Osati kulalikira Mzinda wa Ninevi koma kuphunzitsa Israyeli kuti chipulumutso si cha Ayuda okha.

**VESI LOTSOGOLERA:** Yona 3:1-2

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Chipulumutso sichitchingidwa ndi mtundu kapena zina. "Aliyense amene ayitanira pa dzina la Ambuye adzapulumuka." (Aroma 10:13).

**AMENE AKUTCHULIWAMO:** Yona

### MAGAWO

I. Kutumidwa koyamba: 1:1-2:10
  A. Maitanidwe a umulungu: dzuka, pita, lira: 1:1-2
  B. Kusamvera kwa Yona: Adadzuka mkuthawa: 1:3
  C. Zotsatira za kusamvera: 1:4-17
    l. Kutengedwa ndi mafunde: 1:4-6
    2. Kupezedwa olakwa: 1:7
    3. Thrown overboard: 1:8-16
    4. Kumezedwa ndi nsomba: 1:17
  D. Pemphero la Yona: 2:1-9
    1. Akumbukira zowawa za moyo: 2:3,5-6
    2. Azindikira chitsogozo cha dongosolo la Mulungu: 2:3

3. Azindikira kuti ndi chokhumba cha Ambuye kuyankha pemphero: 2:2,7
4. Akufunika kudziperekenso ndi kulapa: 2:9
5. Zotsatira za chipulumutso: 2:10

E. Chipulumutso cha Yona: 2:10

II. Kutumidwa kwachiwiri: Dzuka, pita, lalikira: 3:1-10

A. Kumvera: Adadzuka, anapita, analira: 3:1-4

B. Zotsatira za kumvera: 3:5-10

l. Anthu anakhulupirira: 3:5
2. Analapa: Kusala kwa munthu ndi nyama, chiguduli ndi mphulusa: 3:5-9
3. Mzinda unatetezedwa: 3:10

III. Vuto la mneneri: 4:1-11

A. Mkwiyo wa mneneri: 4:1-5

B. Chidzudzulo cha Mulungu: 4:6-11

**MAYESO ODZIYETSA NOKHA**

1. Kodi analemba buku la Yona ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene analembera buku la Yona.

3. Kodi buku la Yona amlembera kwa ndani?

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Yona.

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Yona.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Pamene Mulungu "analapa" sizitanthauza kulapa ku zoipa (3:10).
Mulungu, mwa chifundo, anaganiza zosabweretsa chiweruzo chimene anachikonza kale chifukwa anthu a ku Ninevi anakhulupirira uthenga wa Yona. Onani Amosi 7:3; Luka11:30; Mateyu 12:39.

2. Yona anali mtundu wa Israyeli:

-Wosankhidwa kuchita umboni: Deuteronomo 14:2; Ezekieli 20:5
-Wotumidwa ndi Mulungu: Yesaya 43:10-12 ndi 44:8
-Kusamvera chifuniro cha Ambuye: Eksodo 32:1-4; Oweruza 2:11-19; Ezekieli 6:1-5; Marko 7:6-9
-Pakati pa anthu a mitundu yosiyana: Deuteronomo 4:27; Ezekieli 12:15
-Chikhalire pakati pa anthu osadziwa Mulungu, anamudziwa Mulungu: Aroma 11:11
-Modabwitsa anapulumutsidwa: Hoseya 3:3; Yeremiya 30:11; 31:35-37

3. Onani zifukwa zimene Yona sanmusangalase Mulungu. Chifukwa anali wodzala ndi chisomo, chifundo, wosakwiya msanga, wazifundo zochuluka, ndipo amalapa chiweruzo.

4. Yona amatsogozedwa ndi maganizo a umunthu. Mwachitsanzo mu chaputala cha 4 anali wokwiya, kenako anakondwa, nakwiyanso. Anali wofuna zake zokha (chaputala 1) ndipo anali ndi makhalidwe onyada (4:2). Amaika chidwi pa chimwemwe ndi chitonthozo chake (chaputala 4) koposa miyoyo yotaika.

5. Pamene munthu athawa Mulungu, pamakhala . . .

-Kuchita mosiyana ndi lamulo lake: 1:2-3
-Kulephera kubisala: 1:4,17
-Kupanda chitetezo mtsogolo: 1:15
-Kulephera kuzithandiza wekha: 1:4-6

6. Yona ndi mtundu wa Khristu. Onse anali ndi uthenga wapadera, Yona wa chiweruzo ndipo Yesu wachipulumutso. Onse anakumana ndi namondwe. Yona anponyedwa mmadzi ndipo Yesu analetsa namondwe. Yona anlira mmimba mwa nsomba ndipo Yesu analira pamtanda. Onse anadzuka tsiku lachitatu (Yona kuchokera mmimba mwa nsomba Yesu kuchokera kumanda) ndipo onse analalikira atauka.

## CHAPUTALA CHA 34

MIKA

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Mika.
- Kudziwa kumene wolemba buku la Mika amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Mika.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Mika kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Mika.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Mika

**AMENE AMAWALEMBERA**: Yuda ndi Israyeli.

**VESI LOTSOGOLERA:** Mika 6:8

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Mulungu amaweruza amene amazunza anthu a Mulungu.

**AMENE AKUTCHULIDWAMO:** Mika

### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1

II. Uneneri wa chiweruzo: 1:2-2:13

- A. Chiweruzo pa Samaliya: 1:2-8
    1. Kulengeza za chiweruzo: 1:2-4
    2. Kuonongeka kwa Samaliya: 1:2-8
- B. Chiweruzo pa Yuda: 1:9-16
- C. Chiweruzo pa ozunza: 2:1-11
    1. Mwano ndi chiwawa cha akulu: 2:1-5
    2. Aneneri aboza amene akhalitsa chete aneneri owona: 2:6-11
- D. Chifundo pa osalawo: 2:12-13

III. Kukhazikitsa ufumu wa Mesiya: 3:1-5:15

- A. Chiweruzo pa atsogoleri oyipa, aneneri aboza, ndi mitundu: 3:1-12

1. Machimo a atsogoleri a boma: 3:1-4
2. Machimo a aneneri abodza: 3:5-8
3. Atsogoleri, aneneri, ndi ansembe: 3:9-11

B. Chikhalidwe cha ufumu: 4:1-5

C. Kukhazikitsa ufumu: 4:6-13
   1. Kubwenzeretsa ulamuliro woyamba: 4:6-8
   2. Ku Babulo asanabwenzeretse: 4:9-10
   3. Chipulumutso cha Zione ndi chionongeko cha adani: 4:11-5:1

D. Kubwera koyamba ndi kukanidwa kwa mfumu: 5:1-2

E. Nthawi pakati pa kukanidwa kwa mfumu ndi kubwerera: 5:3

F. Zochitika pa kubwerera kwake: 5:4-15
   1. Azapatsa nkhosa zake chakudya: 5:4
   2. Azakhala mtendere wa anthu ake: 5:5-6
   3. Azapereka mphamvu kwa anthu ake: 5:7-9
      (a) Otsalawo ngati mame: 5:7
      (b) Otsalawo ngati nkango: 5:8
      (c) Otsalawo ngati ogonjetsa: 5:9-15

IV. Vuto la Ambuye ndi anthu ake ndi chifundo chake chomaliza: 6:1-7:20

A. Kusayamika ndi zoipa za anthu: 6:1-7:6
   1. Kusayamika chifukwa cha madalitso: 6:1-5
   2. Makhalidwe a chilungamo ndi oyenera Mulungu, osati nsembe za kunja: 6:6-8
   3. Chiopsezo cha chiweuzo cha Mulungu: 6:9-14

B. Pembedzero la mneneri: 7:7-20
   1. Kuvomereza uchimo wa dziko: 7:1-6
   2. Kuvomereza chikhulupiriro: 7:7-13
   3. Pemphero la kusintha kwa chisomo: 7:14
   4. Yankho la Ambuye: 7:15-17
   5. Mawu oyamika: 7:18-20

**MAYESO ODZIYETSA NOKHA**

1. Kodi amene analemba buku la Mika ndi ndani?

_______________________________________________

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Mika.

_______________________________________________
_______________________________________________
_______________________________________________

3. Kodi wolemba buku la Mika amalembera kwa ndani?

_______________________________________________
_______________________________________________

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Mika.

_______________________________________________
_______________________________________________
_______________________________________________

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Mika kuchokera pamtima.

_______________________________________________
_______________________________________________
_______________________________________________

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli).

**KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Mawu achidule ochokera mbuku la Mika akanatha kupulumutso moyo wa Yeremiya mneneri zaka zambiri zapitazo. Werengani Yeremiya 26:16-18 ndipo fanizirani ndi Mika 3:12.

2. Mika 4:1-5 amatiuza za nkhani yabwino ya zaka chikwi cha Mbaibulo.

3. Mawu atatu awa akhoza kukuthandizani kukumbukira buku la Mika:

   -Kunja: Maulaliki ake ochokera machaputala 1-6
   -Mkati: Malingaliro ake akupezeka pa 7:1-6
   -Kumwamba: Pemphero lake la kwa Mulungu limapita kumwamba pa 7:7-20

4. Pa zokhuza Mbiri ya mmbuyo ya mafumu a Yuda ikupezeka mu Mika 1:1 werengani 2 Mafumu 15:32-20:21 ndi 2 Mbiri 27:1-33:20.

5. Uneneri wa Mika umakamba za ufumu wa kumpoto wa Samaliya ndi ufumu wa kummawa wa Yuda. Nthawi zonse pamene akutchulapo za Samaliya pamakhala malire a ufumu wa kumpoto. Nthawi zonse pamene akukamba za Yerusalemu pamakhala malire a ufumu wa kumwera.

6. Mu Mika 6:6-8 Mulungu amatiuza za mmene tingamfikilire ndi zimene amafuna. Werengani ndimeyi mosamala.

## CHAPUTALA CHA 35

NAHUMU

ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula amene analemba buku la Nahumu
- Kudziwa kumene wolemba buku la Nahumu amalembera
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Nahumu.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la Nahumu.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Nahumu.

**MAWU OYAMABA**

**WOLEMBA**: Nahumu

**AMENE AMAWALEMBERA**: Mzinda wa Ninevi

**CHOLINGA**: Kuchenjeza za chiweruzo pa Ninevi, mzinda wa ufumu wa Asuriumene unatengera anthu a Mulungu ku ukapolo.

**VESI LOTSOGOLERA**: Nahumu 1:2

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI**: Chenjerani, Mulungu amabwenzera choipa

**ANTHU OPEZEKAMO**: Nahumu.

**MAGAWO**

I. Uneneri wa chionongeko, gawo loyamba: 1:1-14

   A. Mawu oyamba: 1:1
   B. Gwero la chionongeko: Mulungu mwini: 1:2-9
      1. Kubwenzera ndi chifundo cha Mulungu: 1:2-3
      2. Mkwiyo wa wowawa pa tchimo: 1:4-6
      3. Kukula kwa chifundo chake: 1:7
      4. Wolondora adani ake: 1:8
   C. Chifukwa chimene amaonongera: Tchimo: 1:9-14
      1. Kukhulipirika kwa Mulungu mu zowawa: 1:9-11
      2. Chionongeko cha Asuri: 1:12-14
      3. Chimwemwe ku Zione: 1:15

II. Promise to Judah: They no longer need fear this cruel nation: 1:15

III. Uneneri wa chiononongeko, gawo lachiwiri: 2:1-3:19

A. Chitetezo ndi kuonongeka kwa mzinda: 2:3-13
   1. Chiononongeko pa Ninevi: Kuonongeka kwa mzinda: 2:1-7
      (a) Kukonzekera nkhondo mwa mkwiyo: 2:1-4
      (b) Kukana kosowa chiyembekezo: 2:5-6
      (c) Mzinda ngati mkazi wa mfumu ugwida: 2:7
   2. Kuthawa kwa anthu ndi kuononga mzinda: 2:8-13
      (a) Okhala mdzikomo athawa: 2:8-10
      (b) Chiononongeko chimalizika: 2:11-13

B. Chifukwa chimene Ninevi anagwera: 3:1-9
   1. Mmene inalili nkhondo: 3:1-3
   2. Choyambitsa: Machimo ake: 3:1-6,16,19
   3. Kusabisika kwa machimo ake ndi Mulungu: 3:5-7

C. Chiononongeko chosowa Amoni ndi chiononongeko cha Ninevi: 3:8-11 (Onani Yeremiya 46:25; Ezekieli 30:14)

D. Kulephera kwa Ninevi kupulumutsa mzinda: 3:12-19
   l. Kugwa kwa malinga okhazikika: 3:12-13
   2. Chitetezo ndi kuonongeka kwa mzinda: 3:14-19a
   3. Chimwemwe cha aliyense pa kugwa pa Ninevi: 3:19b

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Nahumu ndi ndani?

______________________________________________

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Nahumu.

______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________

3. Kodi wolemba buku la Nahumu amalemberakwa ndani?

______________________________________________
______________________________________________

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Nahumu.

______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Nahumu.

______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Lembani zifukwa zimene Mulungu amabweretsera chiweruzo pa mzinda wa Ninevi.

2. Kodi mukukumbukira za aneneri ena amene mwaphunzira mmbuyomu, amene ananenera ku Ninevi? Kodi mzindawu utachita bwabji pa uneneri woyambawu? (Onani buku la Yona).
3. Fananitsani mavesi awa:

| | |
|---|---|
| Yesaya 8:8; 10:23 | Nahumu 1:8-9 |
| Yesaya 24:1 | Nahumu 2:10 |
| Yesaya 21:3 | Nahumu 2:10 |
| Yesaya 52:7 | Nahumu 1:15 |

4. Izi ndi zina mwa zifukwa zimene mzinda wa Ninevi unagwera:
   -Kukhetsa mwazi: 3:1
   -Bodza: 3:1
   -Umbava: 3:1
   -Kupha anthu osalakwa: 3:3-4
   -Uhule: 3:4
   -Nyanga: 3:4
   -Zonyasa: 3:5
   -Chiwawa cha mseri: 3:6
   -Asilikari (olembedwa) owononga: 3:16
   -Bala limene ndi lalikulu losachiritsika: 3:19
   -Kupitilira kuchita choipa: 3:19

## CHAPUTALA CHA 36

HABAKUKU

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula amene analemba buku la Habukuku.
- Kudziwa kumene wolemba buku la Habakuku amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Habakuku.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Habakuku.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Habakuku.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Habakuku

**AMENE AMAWALEMBERA:** Yuda

**CHOLINGA**: Kuwauza Ayuda akhale tcheru ku zofuna za ku uzimu ndi kuwachenjeza za chilango chimene chikubwera.

**VESI LOTSOGOLERA:** Habakuku 3:2

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Olungama adzakhala ndi moyo mwachikhulupiriro.

**AMENE AKUTCHULIDWAMO:** Habakuku.

### MAGAWO

Bukuli lagawidwa magawo atatu mumachaputala. Habakuku chiphinjo cha uzimu mu chaputala choyamba, masomphenya muchaputala chachiwiri ndi pemphero mu chaputala chachitatu. Zonsezi zimakhuza za chiweruzo cha Mulungu pa Yuda kudzera mwa mtundu wa Akasidi.

I. Mawu otsogolera: 1:1

II. Dandaulo loyamba la Habakuku: 1:2-4

A. Funso la mneneri: 1:2-3a
B. Chikhalidwe ndi malamulo mmene analili kwa Ayuda: 1:3b
C. Mawu otsiriza a mneneri: 1:4

III. Yankho la Ambuye: 1:5-11

A. Ntchito zodabwitsa za Amuye: 1:5
B. Akasidi ndi mphamvu zawo: 1:6-11

IV. Kulimba mtima kwa Habakuku mwa Ambuye: 1:12

V. Dandaulo lachiwiri la Habakuku: 1:13-17

VI. Mneneri odikilira: 2:1

VII. Yankho la Ambuye: 2:2-4

A. Masopmhenya alembedwe poonekera: 2:2
B. Masomphenyawo azakwaniritsidwa: 2:3
C. Masomphenya: 2:4

VIII. Masoka asanu: 2:5-19
A. Mawu oyamba: 2:5-6a
B. Masoka asnu pa Akasidi: 2:6b-19
1. Tsoka loyamba: 2:6b-8
2. Tsoka lachiwiri: 2:9-11
3. Tsoka lachitatu: 2:12-13
(Dziko kudzadza ndi chidziwitso cha Mulungu: 2:14)
4. Tsoka lachinayi: 2:15-18
5. Tsoka lachisanu: 2:19

IX. Nyimbo ya Habakuku: 3:1-19

A. Mutu wake: 3:1
B. Pempho: 3:2
C. Yankho la Ambuye: 3:3-15
D. Yankho la Habakuku: 3:16-19a
E. Kuyimba nyimbo: 3:19b

**MAYESO ODZIYETSA NOKHA**

1. Kodi analemba buku la Habakuku ndi ndani?

______________________________________________

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Habakuku.

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

3. Kodi wolemba buku la Habakuku amalembera kwa ndani?

______________________________________________

______________________________________________

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumuki ya buku la Habakuku.

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Habakuku.

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

**KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Mawu a Habakuku, "wolungama adzakhala ndi moyo mwachikhulupiriro" akupezeka katatu mu chipangano chatsopano. Onani Aroma 1:17, Agalatiya 3:11, ndi Ahebri 10:38.

2. Onaninso Machitidwe 13:40-41 ndi Afilipi 4:4, 10-19.

3. "Mawu olankhulidwa" akhoza kutanthauzidwa ngati "chiphinjo." Kodi chiphinjo cha Habakuku chinali chani? Ndi chiyani chimene chimamuvuta?

4. Onani zimene analankhula zokhuza Mulungu, Woyerayo, Ambuye, ndi mlowammalo oimira Mulungu. Lembani mwachidule zimene mwaphunzira zokhudza Mulungu mbukuli.

5. Onani mawu oti, "munthu wodzikuza kapena wonyada." Lembani mwachidule zimene akuyerekezera ndi amene akusiyana naye. Yakobo 4 amakamba kuti Mulungu akaniza odzikudza.

6. Onani amene agwiritsa ntchito ngati "tsoka" ndipo onetsetsani kumene mawuwa akuoita, ndi chifukwa chimene akupitira, ndi chimene chidzachitika zikafika. Kodi zimenezi ndi zokukhudzani molingana ndi moyo wanu? Ngati ndi choncho lapani.

## CHAPUTALA CHA 37

ZEFANIYA

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula amene analemba buku la Zefaniya.
- Kudziwa kumene wolemba buku la Zefaniya amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Zefaniya.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Zefaniya.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Zefaniya.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Zefaniya

**AMENE AMAWALEMBERA:** Israyeli

**CHOLINGA:** Kuchenjeza Israyeli ndi mitundu ina za chiweruzo cha Mulungu.

**VESI LOTSOGOLERA:** Zefaniya 3:17

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Mulungu ndi wamphamvu populumutsa.

**AMENE AKUTCHULIDWAMO:** Zefaniya

### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1-3

   A. Mnthenga: 1:1
   B. Chidule cha uthenga: 1:2-3

II. Kuyang'ana kwa mkati: 1:4-2:3

   A. Zoona zake za chiweruzo: 1:4-14
      1. Chiweruzo pa mitundi inayi yolambira: 1:4-7
      2. Chiweruzo pa ochimwa a mitundu yonse: 1:8-13
   B. Chikhalidwe ndi zotsatira za chiweruzo: 1:14-18

1. Chili pafupi: 1:14
2. Ngakhale amphmvu atsitsidwa: 1:14
3. Tsiku la mdima lowawa, zotsala, chiwonongeko: 1:15-16
4. Mavuto, mwazi, thupi ngati ndowe: 1:17
5. Opanda chipulumutso: 1:18
6. Tsiku la mkwiyo wa Ambuye: 1:2-3

C. Dzina la chiweruzo: Tsiku la Ambuye: 2:1-3
D. Chiyembekezo cha chiweruzo: 2:3

III. Onani: Chiweruzo chibwera pa amitundu yonse: 2:4-3:7

A. Mizinda ya Afilisiti: 2:4-7
B. Moabu ndi Amoni: 2:8-11
C. Etiopiya: 2:12
D. Asuri ndi mzinda wake wa Ninevi: 2:13-15
E. Chiweruza pa Yerusalemu: 3:1-7
   1. Onani nyengo imene Yerusalemu anali:
      (a) Yonyasa, ozunzika, oonongeka: 3:1
      (b) Osamvera: 3:2
      (c) Atsogoleri oipa a kudziko: 3:3
      (d) Atsogoleri oipa a ku uzimu: 3:4
   2. Onani zifundo za Mulungu: 3:5-7

IV. Onani kutsogolo: Chitatha chiweruzo, machiritso adzafika: 3:8-20

A. Cholinga cha Mulungu chidzkwaniritsidwa: 3:8
B. Kuchokera pa osadziwa Mulungu, otsala a Mulungu adzaoneka: 3:9-10, 12-13
C. Chiweruza pa iwo amene anakhalapo adani a Mulungu: 3:9-13
D. Mesiya wa Israyeli aonekera ngati mfumu: 3:14-20

**MAYESO ODZIYETSA NOKHA**

1. Kodi analemba buku la Zefaniya ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Zefaniya.

3. Kodi buku la Zefaniya amalembera kwa ndani?

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Zefaniya.

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Zefaniya.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Mutu wa mawu oti "Mfumu ya Israyeli" agwiritsidwa ntchito ndi Mulungu kawiri Mbaibulo. Zefaniya anawagwiritsa ntchito mu chipangano chatsopano (3:15). Natanieli, wophunzira wa Yesu, anagwiritsa ntchito mu chipangano chatsopano (Yohane 1:49).

2. Molingana ndi Zefaniya, chiweruzo amachitcha "tsiku la Ambuye." Anagwiritsa ntchito mawuwa kasanu ndi kawiri. (Onani 1:7,8,14,18; 2:2-3).

   Izi ndi zimene tingaphunzire zokhudza tsiku la Ambuye:

   -Lili pafupi: 1:4,7,14
   -Ngakhale amphamvu adzagwa pansi: 1:14
   -Ndi nthawi ya mdima, mantha, mkwiyo, chiwonongeko: 1:15
   -Ndi nthawi ya lipenga: 1:16
   -Chiweruzo chidzadza pa tchimo: 1:17
   -Lidzatsatidwa ndi zizindikiro zazikulu za chilengedwe: 1:15
   -Ndi tsiku la mkwiyo wa Ambuye: 1:2-3
   -Likufika pa zolengedwa zonse: 2:1-15; 3:8

## CHAPUTALA CHA 38

HAGAI

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula amene analemba buku la Hagai.
- Kudziwa kumene wolemba Hagai amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Hagai.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Hagai kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Hagai.

**MAWU OYAMBA**

**WOLEMBA:** Hagai

**AMENE AMAWALEMBERA:** Israyeli, atachoka ku ukapolo; makamaka a Yuda amene anabwerera ku Yerusalemu.

**CHOLINGA:** Kulimbikitsa Israyeli kukhala ndi change chatsopano cha Mulungu ndi kuwapanga atsogoleri onse kudziwa udindo wawo womanga kachisi wolambiramo.

**VESI LOTSOGOLERA:** Hagai 1:5

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Kumanga ufumu wa Mulungu chikuyenera kukhala chinthu choyambirira kwa wokhulupirira weniweni.

**AMENE AKUTCHULIDWAMO:** Hagai

**MAGAWO**

I. Uthenga woyamba: Lamulo lomanganso kachisi (lopatsidwa patsiku loyamba la mwezi wa chisanu mchimodzi) 1:1-15

- A. Tsiku: 1:1
- B. Uthenga: 1:2-11
    - l. Kuchedwa kwa anthu: 1:2-4
    - 2. Zotsatira zake: 1:5-11
- C. Zimene anthu anachita: 1:12-15
    - 1. Kumvera ndi kuopa Mulungu: 1:12
    - 2. Ntchito ya chilimbikitso: 1:13
    - 3. Ntchito inayamba: 1:14
    - 4. Tsiku: 1:15

II. Uthenga wachiwiri: Uneneri wa kachisi wa zaka chikwi umene udzakhala wopambana kuposa kachisi adzamange (tsiku la 21 la mwezi wa chisanu ndi chiwiri) 2:1-9

A. Tsiku: 2:1
B. Uthenga: 2:2-9
   1. Kachisi afanizidwa: 2:2-3
   2. Yankho la chokhumudwitsa: 2:4-5
   3. Kugwedezeka kwa onse ndi ulemerero wotsiriza wa kachisi: 2:6-9

III. Uthenga wachitatu: Lonjezo la madalitso pa kumanganso kachisi (pa tsiku la 24 mwezi wa 9) 2:10-19

A. Tsiku: 2:10
B. Uthenga: Tchimo amapatsirana: 2:11-19
   1. Ansembe afunsidwa: 2:11-13
   2. Zimene angachite: 2:14-19

IV. Uthenga wachinayi: Uneneri wa chionongeko cha kutsogolo ya mphamvu ya maufumu a mitundu (tsiku la 24 mwezi wa 9) 2:20-23

A. Tsiku: 2:20
B. Uthenga: 2:21-23
   1. Kugwetsa mphamvu za dziko lapansi: 2:21-22
   2. Zerubabele wosindikizidwa ndi mphete: 2:23

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Hagai ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Hagai.

3. Kodi buku la Hagai amalembera kwa ndani?

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Hagai.

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Hagai.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenkweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Werengani Hagai 1:9 ndi kupeza zifukwa zimene Israyeli samasngalasa Mulungu.

2. Choonadi cha uzimu mu buku la Hagai:

-Ntchito ya Ambuye imakhala yoyambirira pa zonse.

-Ntchito ya Ambuye imafuna zipangizo zoyera.

-Ntchito ya Ambuye ndi yolumikizana ndi cholinga cha Mulungu kwa anthu.

-Chabwino sapatsirana, koma choipa.

3. Ndinu kachisi wa Mzimu Woyera. Gwiritsani ntchito choonadi cha Hagai kwa inu nokha. Kodi mwakangalika ndi kuika chidwi pa zinthu zanu zokha ndi kusiya zinthu za Mulungu zimene ndi zofunika pa kulalikira uthenga wabwino for spreading the Gospel ndi kupitiliza ntchito yake?

4. Onani mawu onse awa "mawu a Mulungu anadza kwa mneneri Hagai" ndi "ndipo mawu a Mulungu anadza kwa Mneneri Hagai." Mawu onsewa akuyamba ndi uthenga. Izi zikuthandizani kudziwa za mmene buku la Hagai lalembedwera.

5. Kuti mudziwe kumene buku la Hagai analembera werengani Ezara 4:24-6:22.

6. Mulungu anati kwa Israyeli, “Ndizakupanga iwe kukhala mphete” (Hagai 2:23). Mphete ndi chovala ngati chizindikiro cha chikole. Chimagwiranso ntchito ngati chizindikirocha ulemu ndi ulamuliro wa chifumu. Yesu anali “mphete” ya Mulungu imene Anaika pa onse okhulupirira chifanizo chake natipatsa ife ulamuliro.

7. Gwiritsani ntchito ziphunzitso za Hagai za ntchito imene siinathe ya mpingo yofikira dziko ndi uthenga wabwino. Lingalirani za zinthu izi:

-Ntchitoyi ikuyenera kukhala yoyambirira pa ntchito zina zonse.
-Ntchitoyi imafuna zipangizo zoyera.
-Ntchitoyi ndi yolumikizana ndi cholinga cha Mulungu kwa anthu onse.

8. Ngati Hagai amalembera kwa inu ngati munthu molingana ndi mmene mukuchitira ndi ntchito yotumidwa, mukuganiza kuti munganene chiyani?

## CHAPUTALA CHA 39

ZAKARIYA

**ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula amene analemba buku la Zakariya.
- Kudziwa kumene wolemba buku la Zakariya amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Zakariya.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Zakariya kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Zakariya.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Zakariya

**AMENE AMAWALEMBERA:** Israyeli

**CHOLINGA:** Kulimbikitsa Israyeli kuti amalize kachisi

**VESI LOTSOGOLERA:** Zakariya 13:1

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI**: Mulungu ndiye amene amatsogolera zochitika za anthu ndi maiko.

**AMENE ATCHULIDWAMO:** Zakariya

### MAGAWO

I. Mawu oyamba oyitanira ku kulapa: 1:1-6

II. Uneneri wa masomphenya: 1:7-6:8

A. Munthu woyenda pakati pa mitengo yamchisu: 1:7-17 (Israyeli wakunja, koma wosaiwalidwa ndi Mulungu.)
B. Nyanga zinayi: 1:18-21 (Kugwetsedwa kwa Israyeli ndi adani.)
C. Munthu wa chitsulo cha muyeso: 2:1-13 (Kubwera kwa chuma cha Yerusalemu.)
D. Yoswa wansembe wamkulu: 3:1-10 (Tchimo la Israyeli linachotsedwa ndi Yesu, nthambi.)

E. Choikapo nyali ndi mitengo iwiri: 4:1-14 (Israyeli ndi tsogolo lonyamula kuunika kwa mtsogolo.)
    1. Funso loyamba ndi kulongosola kwake: 4:1-10
    2. Funso lachiwiri ndi kulongosola kwake: 4:11-14
F. Mpukutu wouluka: 5:1-4 (Boma loyipa lotembereredwa ndi Mulungu)
G. Mkazi ndi efa: 5:5-11 (Choipa chichoka pa mapiko a umulungu)
H. Magareta anayi: 6:1-8 (Chiweruzo cha Mulungu.)

III. Uneneri woonekera mu zinthu: 6:9-8:23

A. Ayuda obwerera: 6:9-15
B. Zachabe za anthu: 7:1-8:23
    1. Masiku osala a Israyeli ndi kumvera mawu: 7:1-17
        (a) Mmene uneneri unachitikira: 7:1-3
        (b) Kusala sikofunika, koma kumva: 7:4-7
    2. Theka loyamba la yankho la Ambuya ku funso la kusala kudya: 7:8-14
        (a) Chimene Mulungu amafuna kwa atate: 7:8-10
        (b) Kukana kwa atate kukumvera: 7:11-14
    3. Gawo lachiwiri la yankho la Ambuye: 8:1-23
        (a) Nthawi ya chiombolo: 8:1-8
        (b) Uthenga wolimbikitsa: 8:9-17
        (c) Kusala kusintha mkukhala chimwemwe: 8:18-23

IV. Uneneri wachindunji: 9:1-14:21
A. Uneneri woyamba: Kubwera koyamba ndi kukanidwa kwa Yesu: 9:1-11:17
    1. Kugwa kwa maiko osadziwa Mulungu ndi chipulumutso cha ku Zione: 9-10
    2. Abusa abwino ndi oyipa: 11:1-17
        (a) Dziko lochepetsedwa: 11:1-3
        (b) Mbusa wabwino: 11:4-14
        (c) Mbusa wopusa: 11:15-17
B. Uneneri wachiwiri: Kubwera kwachiwiri ndi kulandiridwa kwa Yesu: 12:1-14:21
    1. Chipulumutso ndi kutembenuka kwa Israyeli mtsogolo: 12:1-13:9
        (a) Chipulumutso cha Yuda ndi Yerusalemu: 12:1-9
        (b) Mzimu wa chisomo ndi maliro: 12:10-14
        (c) Kasupe wachisomo cha chipulumutso: 13:1-6
    2. Kubwera kwa Yesu: 14:1-21
        (a) Chiweruzo ndi chipulumutso: 14:1-5
        (b) Chipulumutso chomaliza: 14:6-11
        (c) Chionongeko cha mitundu imene ndi adani: 14:12-15
        (d) Kutembenuka kwa mitundu yosadziwa Mulungu: 14:16-19

(e) Chilichonse chosayera chichotsedwa: 14:20-21

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Zakariya ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Zakariya.

3. Kodi buku la Zakariya amalembera kwa ndani?

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Zakariya.

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Zakariya.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Buku la Zakariya limapereka nkhani yambiri yokhudza utumiki wa angelo. Onani machaputala 1 ndi 2.

2. Monganso buku la Yobu, Zakariya limapereka chinthunzithunzi cha kumwamba pa mkangano wa Mulungu ndi Satana. Onani Yobu 1 ndi 2 ndi Zakariya 3:1-5.

3. Zoona zambiri zokhudza Yesu zikupezeka mu Zakariya:
   -Kutuma kwake: 2:8-11
   -Ntchito yake ya pano: 3:1-2
   -Kukhuzidwa kwake pa Yerusalemu: 1:12
   -Dzina lake: 6:12
   -Kachisi wake: 6:13
   -Kulowa kwake ku Yesusalemu mwachigonjetso: 9:9
   -Kuperekedwa kwake: 11:12
   -Kupachikidwa kake: 12:10; 13:7
   -Kuzindikiridwa kwake ndi Israyeli: 12:1
   -Kuonekera kwake ku Phiri la Zione: 14:4
   -Kulambiridwa kwake ndi mitundu yonse: 14:16
   -Chigonjetso chake pa nkhondo ya Harmagedoni: 14:3

4. Zoona zambiri zokhudza mzinda wa Mulungu zikupezeka mu Zakariya:
   -Mzinda wa choonadi: 8:3
   -Wozingidwa ndi ulemerero wa Mulungu: 2:5
   -Wozazidwa ndi ana: 8:5
   -Wochezeredwa ndi mitundu yonse: 8:20-23
   -Wozungulilidwanso ndi adani: 12:2; 14:2
   -Adani ake agonjetsedwa: 12:9; 14:12-14
   -Mzika zake zimudziwa Mesiya: 12:10
   -Wodzadza ndi chiyero cha Mulungu: 14:21

## CHAPUTALA CHA 40

## MALAKI

**ZOLINGA**:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kutchula amene analemba buku la Malaki.
- Kudziwa kumene wolemba buku la Malaki amalembera.
- Kutchula cholinga chimene amalembera buku la Malaki.
- Kulemba Vesi Lotsogolera la buku la Malaki kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Malaki.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Malaki

**AMENE AMAWALEMBERA:** Israyeli

**CHOLINGA:** Kufunsa mtundu kuti ulape ndi kutsata chilungamo.

**VESI LOTSOGOLERA:** Malaki 2:2

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Kulapa (malingaliro) + Kutembenuka (ntchito) = Kubwenzeretsa
Malingaliro (kulapa ku uchimo) ndi ntchito (kubwerera kwa Mulungu) ndi zofunika pa chikhululukiro (kubwenzeretsa ku chilungamo cha Mulungu).

**AMENE AKUTCHULIDWAMO:** Malaki

### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1-5

  A. Mnthenga: 1:1
  B. Uthenga: 1:1
  C. Wolandira uthenga:  Israyeli: 1:1
  D. Chikondi cha Mulungu pa Israyeli: 1:2-5
    1. Esau ndo Yakobo: 1:2-3
    2. Mulungu ndi Edomu: 1:4-5

II. Uthenga wa kwa ansembe: 1:6-2:9

A. Kunyalanyaza kwao pa ntchito za chpiembedzo: 1:6-2:4
   1. kupanda ntchito kwa nsembe: 1:6-14
   2. Bola kutseka kachisi kusiyana ndi kupanga chipembedzo chopanda ntchito: 1:9-10
   3. Ntchito za pamwamba za amitundu: 1:11
   4. Zoyenera polambira: 1:12-13 kusiyana ndi chipembedzo cha pamwamba 1:11.
   5. Temberero la Mulungu: 1:14-2:4
B. Kulakwa pophunzitsa chilamulo: 2:5-9
   1. Pangano ndi Levi ndi wansembe weniweni: 2:5-7
   2. Ansembe opanduka ndi manyazi awo: 2:8-9

III. Uthenga wa Ayuda a wamba: 2:10-4:3

A. Lamulo pa nkhanza: 2:10-16
B. Chenjezo pa chiweruzo: 2:17-3:6
   1. Mafunso awo: 2:17
   2. Mulungu moto woyeretsa: 3:1-3
   3. Kuyeretsa ansembe ndi anthu: 3:3-5
   4. Mulungu sasintha: 3:6
C. Kufunika kwa kulapa: 3:7-12
   1. Kusakhulupirika kwa anthu ndi temberero la Mulungu: 3:7-9
   2. Mphoto ya Mulungu pa ulemu ndi kukhulupirika kwawo: 3:10-12
D. Lamulo la umulungu pa tchimo: 3:13-4:3
   1. Dandaulo: 3:13-15
   2. Kusiyanitsa pakati pa olungama ndi oyipa: 3:16-18
   3. Kulankhula chionongeko pa oyipa: 4:1
   4. Kukwezedwa ndi ulemerero wa olungama: 4:2-3

IV. Chenjezo lotsiriza: 4:4-6

A. Kusunga lamulo la Mose: 4:4
B. Kuyembekezera kubwera kwachiwiri kwa Yesu: 4:5-6

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi amene analemba buku la Malaki ndi ndani?

2. Tchulani cholinga chimene amalembera buku la Malaki.

3. Kodi buku la Malaki amalembera kwa ndani?

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Malaki.

5. Lembani Vesi Lotsogolera la buku la Malaki.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

**KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Malaki ali ndi ndime zotsogolera zingapo:
   -Yodziwika bwino ya Mchipangano Chakale ndi yokhudza kupereka: 3:8-10
   -Yodabwitsa ya zochitika nthawi zonse ndi: 3:16
   -Ndime yokhayo imene okhulupirira amatchedwa ana ake: 3:17
   -Buku lokhalo la Mchipangano Chakale lomwe limalosera za kubwera kwa Eliya kutumikira munthawi ya chisautso chachikulu: 4:5

2. Ndizovuta kwa munthu kuvomereza choonadi kuti ndi wochimwa. Onani mmene anthu amalimbanira ndi chiweruzo cha Mulungu mu buku la Malaki. "Komai nu mukuti" ndi mawu otsogolera amene akuonetsera kulimbana kwa anthu ndi Mulungu: 1:2,6,7; 2:17; 3:7,8,13.

3. Onani magawo enieni a mayesero a mtumiki: 1:6-2:9

4. Pali mawo ot "onani" mu buku la Malaki:
   -Onani ndizaipsa ndi kukana malambiro: 2:3
   -Onani ndidzatumiza mnthenga wanga (Yohane Mbatizi): 3:1
   -Onani dziko lazapsa: 4:1
   -Onani Eliya adzachenjeza: 4:5

5. Buku la Mulungu la "Chikumbukiro": Onaninso Eksodo 32:32; Masalmo 56:8; 69:28; 139:16; Ezekieli 13:9; Danieli 7:10; 11:1; Afilipi 4:3; Chibvumbulutso 20:12

6. Ngakhale aneneri ambiri anakhala ndi kunenera kwa masiku a kusintha kwakukulu utsogoleri, Malaki anakhala mu nyengo ya chete imene Mulungu amaoneka ngati wawaiwala anthu ake amene amavutika ndi umphawi komanso ulamuliro wachilendo ku Yuda. Masiku a zozizwa amaoneka kuti anapita ndi Eliya ndi Elisa. Kachisi sanatsilizidwe ndipo palibe chachilendo chimene chinachitika choonetsa kupezeka kwa Mulungu wa ulemerero wodzala monga Ezekieli ananenera (Ezekieli 43:4). Anthu amagwirabe ntchito za chipembedzo koma opanda chidwi. Mu zoona zake, malonjezo amene anaperekedwa amayembekezera zinthu zina kwa anthu zimene anthuwo amalephera kuchita pamaso pa Mulungu kuti alandira. Uneneri wa Malaki umalora ife kuona zowawa nomanso mayesero a nthawi ya moyo wodikira. Kwambirinso, amaonetsa njira ya mbuyo ya chikhulupiriro chenicheni mwa Mulungu amene sasintha (3:6); amene amaitana anthu kubwerera kwa Iye (3:7); ndipo amene saiwala amene afika kwa Iye (3:16).

## MAYANKHO KU MAFUNSO ODZIYETSA NOKHA

### CHAPUTALA CHA 1:

1. Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitso, citsutsano, cikonzero, cilangizo ca m'cilungamo.

   kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kucita nchito iri yonse yabwino (II Timoteo 4:16-17).

2. Mawu oti "Baibulu" amatanthauza "mabuku."

3. Mawu oti "Lemba" amatanthauza "zolemba zopatulika."

4. Chipangano Chakale ndi Chipangano Chatsopano.

5. 66

6. Chilamulo, mbiri, ndakatulo ndi uneneri.

7. Mauthenga abwino, mbiri, makalata ndi uneneri.

8. Mawu oti "chipangano" amatanthauza "pangano."

9. Pa chiphunzitso, chidzudzulo, chikonzero, ndi chilangizo cha chilungamo. (II Timoteo 3:16-17)

10. Baibulo silimazitsutsa ndipo ndi logwirizana mu mitu yake ikuluikulu.

11. Baibulo lili ndi zambiri.

12. a. T; b. T; c. F; d. F; e. F

13. Yesu. Luka 24:44-48.

**CHAPUTALA CHA 2:**

1. Kupfuula kwanga kuyandikire pamaso pano, Yehova;
   Mundizindikiritse monga mwa mau anu. (Masalmo 119:169)

2. 39

3. 27

4. Mukuyenera kuliwerenga mwandongosolo kuti mumvetsetse zomwe zalembedwamo.

5. Werengani tsiku ndi tsiku, mosankha, mwapemphero ndi mwandondomeko.

**CHAPUTALA CHA 3:**

1. Ambuye anapatsa mau: Akazi akulalikira uthengawo ndiwo khamu lalikuru (Masalmo 68:11).

2. Mtundu wa kalembedwe ka Baibulo ndi chilankhulo chosiyana ndi choyamba chimene mawu a Mulungu anatanthauziridwa pachiyambi.

3. Kutanthauzira ndi mawu ndi mawu mu chi Heleni, Chiheberi ndi Chi Aramaiki. Pamene chidule sichitanthauzira mawi ndi mawu, koma ganizo pa ganizo.

4. Baibulo la King James

5. Chifukwa palibe zilankhulo ziwiri zimene ndi zofanana, choncho kusiyanaku kunabwera chifukwa cha kutanthauzira.

6. Chiheberi, Chi Aramaiki ndi Chgiriki.

**CHAPUTALA CHA 4:**

1. Taona ndakhwimitsa nkhope yako itsutsane nazo nkhope zao; ndalimbitsanso mutu wako utsutsane nayo mitu yao (Ezekieli 3:8).

2. Mnadndanda wa magawo ndi dongosolo la zowelemba zimene ukuyenera kuwerenga. Nkhani zimalembedwa mwachidule zimene utha kugwiritsa ntchito mtsogolo potumikira komanso powerenga.

3. Ngati mulu ndi vuto lomvetsetsa mndandanda wa magawowa, onaninso malangizo a mmene mungalembere dongosololi mu chaputalachi.

4. Mfundo zikuluzikulu zimaonetsaedwa ndi ma nambala a Choroma.

5. Mfundo zotsatira ku mfundo yaikulu zimaonetsedwa ndi chilembo chachikulu cha afabeti.

**CHAPUTALA CHA 5:**

1. Mose

2. Kusunga mbiri ya Israyeli ndi nkhani za chilengedwe, tchimo, chiombolo ndi mmene Mulungu amachitira ndi munthu.

3. Israyeli.

4. Dongosolo la Mulungu pa chiyambi ndi la amitundi yonse. Mulungu amayamba zinthu zatsopano ndi anthu.

5. Ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo, ndi pakati pa mbeu yako ndi mbeu yace; ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira citende cace (Genesis 3:15).

**CHAPUTALA CHA 6:**

1. Mose.

2. Kulemba mbiri ya Israyeli kuchoka ku akapolo ndi kutsindika cholinga chawo chokhala padziko.

3. Israyeli.

4. Chipulumutso chimdza mwa mwazi wa mwana wa nkhosa wa Mulungu, Yesu.

5. Ndipo mwaziwo udzakhala cizindikilo kwa inu pa nyumba zimene mukhalamo; pamene ndiona mwaziwo ndidzapitirira inu, ndipo sipadzakhala mliri wakukuonongani, pakukantha Ine dziko la Aigupto (Eksodo 12:13).

**CHAPUTALA CHA 7:**

1. Mose.

2. Kuwaonetsa Israyeli za mmene angakhalire mtundu woyera mu chiyanjano ndi Mulungu ndi kuwakonzekeretsa kutalikitsa dongosolo la Mulungu la chiombolo kwa mitundu yonse.

3. Mulungu amafuna chiyero kwa anthu ake.

4. Cifukwa cace dzipatuleni, nimukhale oyera; pakuti Ine ndine Yehova Mulungu wanu (Levitiko 20:7).

**CHAPUTALA CHA 8:**

1. Mose.

2. Kuonetsa zomwe anakumana nazo mu lendo wa mu chipululu umene ndi mtundu wa Mkhristu wogonjetsedwa.

3. Israyeli.

4. Mulungu sasangalatsidwa ndi chinachilichonse kupatula kudzipereka kwa Iye kwa mtunthu.

5. Koma mukapanda kutero, taonani, mwacimwira Yehova; ndipo zindikirani kuti cimo lanu lidzakupezani (Numeri 32:23).

**CHAPUTALA CHA 9:**

1. Mose.

2. Kubwenzeretsa chilamulo ku mbadwo watsopano wa Israyeli umene unabadwapa phiri la Sinayi.

3. Israyeli.

4. Kumvera kumabweretsa madalitso. Kusamvera kumabweretsa chiwereuzo

5. Imvani, Israyeli; Yehova Mulungu wathu, Yehova ndiye mmodzi; 5ndipo muzikonda Yehova Mulungu wanu ndi mtima wanu wonse, ndi moyo wanu wonse, ndi mphamvu yanu yonse (Deuteronomo 6:4-5).

**CHAPUTALA CHA 10:**

1. Yoswa.

2. Kulemba mbiri yogonjetsa a Kanani

3. Israyeli.

4. Palibe chipambano chabwino kapena chigonjetso cha uzimu popanda nkhondo.

5. Ndipo ngati kutumikira Yehova kukuipirani mudzisankhire lero amene mudzamtumikira, kapena milungu imene anaitumikira makolo anu okhala tsidya lija la mtsinje, kapena milungu ya Aamori amene mukhala m'dziko lao; koma ine, ndi a m'nyumba yanga, tidzatumikira Yehova (Yoswa 24:15).

**CHAPUTALA CHA 11:**

1. Samueli.

2. Mbiri ya ulamuliro wa Oweruza imene inachitika kumapeto kwa buku la Yoswa.

3. Israyeli.

4. Pamakhala chilango cha umulungu wokonzedwa ndi Mulungu ndi cholinga chowabwenza anthu kuchoka ku uchimo mkuwapulumutsa.

5. Masikuwa panalibe mfumu m'Israyeli, yense anacita comuyenera m'maso mwace (Oweruza 17:6).

**CHAPUTALA CHA 12:**

1. Wolemba wosadziwika

2. Linalembedwa ngati mbiri ya Israyeli yofuna kuonetsa chidwi cha Mulungu pa anthu onse. Komanso imaonetsa amene amayenera kuwombola ngati Yesu Christu.

3. Israyeli.

4. Mulungu akhoza kusintha zowawa kukhala mdalitso.

5. Nati Rute, Musandiumirize kuti ndikusiyeni, ndi kubwerera osakutsatani; pakuti kumene mumukako ndimuka inenso, ndi kumene mugonako ndigona inenso; anthu a kwanu ndiwo anthu a kwa inenso, ndi Mulungu wanu ndiye Mulungu wanga; 17kumene mudzafera inu ine ndidzafera komweko, ndi kuikidwa komweko; andilange Yehova naonjezeko, ciri conse cikasiyanitsa inu ndi ine, koma imfa ndiyo (Rute 1:16-17).

**CHAPUTALA CHA 13:**

1. Samueli.

2. Mbiri ya mmene Mulungu amachitira ndi anthu ake.

3. Israyeli.

4. Kumvera kuposa nsembe yopsereza.

5. Ndipo Samueli anati, Kodi Yehova akondwera ndi nsembe zopsereza ndi nsembe zophera, monga ndi kumvera mau a Yehova? Taonani, kumvera ndiko kokoma koposa nsembe, kuchera khutu koposa mafuta a nkhosa zamphongo, 23Pakuti kupanduka kuli ngati coipa ca kucita nyanga, ndi mtima waliuma uli ngati kupembedza milungu yacabe ndi maula. Popeza inu munakaniza mau a Yehova, Iyenso anakaniza inu, kuti simudzakhalanso mfumu (I Samueli 15:22-23).

6. Kupitiliza ndi mbiri imene Mulungu amkachitira ndi anthu ake.

7. Israyeli.

8. Mulungu amakwaniritsa ma dongosolo kudzera kwa iwo amene amvera Iye posatengera zofoka zawo.

9. Ndiponso mtundu uti wa pa dziko lapansi ufanana ndi anthu anu, ndiwo Israyeli, amene Mulungu anakadziombolera akhale anthu ace, ndi kuti limveke dzina lace, ndi kukucitirani zinthu zazikuru ndi kucitira dziko lanu zoopsa, pamaso pa anthu anu, amene munadziombolera kuwaturutsa ku dziko la Aigupto mwa amitundu ndi milungu yao? (II Samuel 7:22-23).

**CHAPUTALA CHA 14:**

1. Wolemba ndi wosadziwika. Mwina anali Yeremiya.

2. Kupitilira kulemba Mbiri ya mmene Mulungu amachitira ndi anthu ake, Israyeli.

3. Israyeli.

4. Kulekerera kumaoneka ngati mkosavuta koma kulinso ndi mtengo wake.

5. Ndiponso ndidasiya m'lsrayeli anthu zikwi zisanu ndi ziwiri osagwadira Baala maondo ao, osampso-mpsona ndi milomo yao (I mafumu 19:18).

6. Kupitilira ndi mbiri ya mmene Mulungu amachitira ndi anthu ake, Israyeli.

7. Israyeli.

8. Maufumu a dziko lapansi ndi akanthawi. Amadzuka ndi kugwa mwa dongosolo la Mulungu.

9. Ndipo kunali ataoloka, Eliya anati kwa Elisa, Tapempha cimene ndikucitire ndisanacotsedwe kwa iwe. Ndipo Elisa anati, Mundipatse magawo awiri a mzimu wanu akhale pa ine. Nati iye, Wapempha cinthu capatali, koma ukandipenya pamene ndicotsedwa kwa iwe, kudzatero nawe; koma ukapanda kundipenyapo, sikudzatero ai (II Mafumu 2:9-10).

**CHAPUITALA CHA 15:**

1. Wolemba ndi wosadziwika. Mwina Ezara.

2. Kulemba mbiri ya chipembedzo cha Yuda.

3. Israyeli.

4. Pamene Mulungu wakwezedwa, anthu ake amadalitsika.

5. Ukulu, ndi mphamvu, ndi ulemerero, ndi kulakika, ndi cifumu ndi zanu, Yehova; pakuti zonse zam'mwamba ndi pa dziko lap ansi ndi zanu; ufumu ndi wanu, Yehova; ndipo mwakwezeka mutu wa pa zonse (I Mbiri 29:11).

6. Kulemba mbiri ya chipembedzo cha Yuda.

7. Israyeli

8. Madalitso a Mulungu amabwera tikadzichepetsa ndi kumfuna Iye.

9. Ndipo anthu anga ochedwa dzina langa akadzicepetsa, nakapemphera, nakafuna nkhope yanga, nakatembenuka kuleka njira zao zoipa; pamenepo ndidzamvera m'Mwamba, ndi kukhululukira coipa cao, ndi kuciritsa dziko lao (II Mbiri 7:14).

**CHAPUTALA CHA 16:**

1. Ezara.

2. Ezara amawauza anthu a Mulungu ochokera ku ukapolon wa Babulo za kumanganso kwa kachisi ku Yerusalemu.

3. Israyeli.

4. Kubwerera ndi kubwenzeretsa ndi mfundo za kulapa.

5. Ndipo ana a Israyeli, ansembe ndi Alevi, ndi ana otsala a ndende, anapereka nyumba iyi ya Mulungu mokondwera (Ezara 6:16).

**CHAPUTALA CHA 17:**

1. Nehemiya

2. Kupitiliza mbiri ya Israyeli. Komanso za kumanganso kwa chipata cha Yerusalemu.

3. Israyeli.

4. Palibe mwayi opanda chitsutso. Chikhulupiriro chopanda ntchito ndi chakufa.

5. Ndipo ndinawatumizira mithenga, ndi kuti, Ndirikucita nchito yaikuru, sindikhoza kutsika; ndiidulirenji padera nchito poileka ine, ndi kukutsikirani? (Nehemiya 6:3).

**CHAPUTALA CHA 18:**

1. Wosadziwika

2. Kupitilira ndi mbiri ya Israyeli. Komanso kuonetsera za thandizo la Mulungu pa anthu ake.

3. Ayuda opezeka ku Peresiya.

4. Mulungu amakumana ndi mavuto a moyo ngati zotengera zake zimene anazikonzeratu.

5. Pakuti ukakhala cete konse tsopano lino, cithandizo ndi cipulumutso zidzafuma kwina; koma iwe ndi nyumba ya atate wako mudzaonongeka; ndipo kaya, kapena walowera ufumu cifukwa ca nyengo ngati iyi? (Estere 4:14).

**CHAPUTALA CHA 19:**

1. Wosadziwika

2. Bukuli limalimbana ndi funso lakuti," Mchifukwa chiyani wolungama amavutika?"

3. Bukuli sanalembere aliyense koma litha kupita kwa onse okhulupirira amene akukumana ndi mayesero.

4. Pali chifukwa chenicheni cha uzimu chimene munthu wolungama amavutikira. Kuvutika si umboni woti Munlungu wakutaya.

5. Koma ndidziwa kuti Mombolo wanga ali ndi moyo, Nadzauka potsiriza papfumbi. Ndipo khungu langa litaonongeka, Pamenepo wopanda thupi langa, ndidzapenya Mulungu Amene ndidzampenya ndekha, Ndi maso anga adzamuona, si wina ai.
   Imso zanga zatha m'kati mwanga (Yobu 19:25-27).

   Koma adziwa njira ndilowayi; Atandiyesa ndidzaturuka ngati golidi (Yobu 23:10).

**CHAPUTALA CHA 20:**

1. Mfumu Davide ndiye amene analemba Masalmo ambiri.

2. Buku la Masalmo limadziwika ngati buku la nyimbo kwa ana a Israyeli. Ndi pemphero ndi matamando a buku la Baibulo.

3. Israyeli, koma buku lakhala likugwiritsidwa ntchito pa mapemphero, chilimbikitso ndi matamando pakati pa okhulupirira ambiri.

4. Pemphero, chiyamiko, pembedzero ndi chivomerezo ndi magawo a kulamnira koona.

5. Tiyeni tiyimbire Yehova mokondwera; Tipfuule kwa thanthwe la cipulumutso cathu (Masalmo 95:1).

**CHAPUTALA CHA 21**

1. Solomoni.

2. Zikupezeka mu Miyambo 1:1-6.

3. Israyeli, koma zoona zake mzakuti akhoza kugwiritsa ntchito okhulupirira onse.

4. Nzeru zathu za umulungu zimatithandizira kuti tikhale ndi nzeru ndi ena. Miyambo ndi kubweretsa pamodzi nzeru zopatsidwa ndi Mulungu kwa munthu kuti akathe kukhala bwino ndi ena.

5. Wodala ndi wopeza nzeru, Ndi woona luntha (Miyambo 3:13).

**CHAPUTALA CHA 22:**

1. Solomoni.

2. Kufunafuna kukhala ndi moyo wopanda Mulungu.

3. Israyeli ndi okhulupirira onse makamaka achinyamata.

4. Moyo wopanda Mulungu uli chabe.

5. Mau atha; zonse zamveka zatha; opa Mulungu, musunge malamulo ace; pakuti coyenera anthu onse ndi ici (Mlaliki 12:13).

**CHAPUTALA CHA 23:**

1. Solomoni.

2. Kuonetsa ubale wa pakati pa Yesu ndi mpingo monga ubale wa mu ukwati.

3. Israyeli ndi okhulupirira onse.

4. Chitsanzo cha chikondi cha Umulungu pakati pa mamuna ndi mkazi wake ndi chitsanzo cha ubale wa pakati pa Khristu ndi Mpinngo.

5. Madzi ambiri sangazimitse cikondi, Ngakhale mitsinje yodzala kucikokolola: Mwamuna akapereka katundu yense wa m'nyumba yace ngati sintho la cikondi, Akanyozedwa ndithu (Nyimbo ya Solomoni 8:7).

**CHAPUTALA CHA 24:**

1. Yesaya.

2. Chikonzero ndi chidzudzulo.

3. Yuda.

4. Kugalukira kumabweretsa chilango. Kulapa kumabweretsa kubwenzeretsa.

5. Tonse tasocera ngati nkhosa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa Iye mphulupulu ya ife tonse (Yesaya 53:6).

**CHAPUTALA CHA 25:**

1. Yeremiya.

2. Kuchenjeza za chiweruzo ndi ukapolo wa kutsogolo ndi kufunika kwa kulapa.

3. Yuda.

4. Ngozi za dziko ndi kubwerera mbuyo kwa zinthu ndi zotsatira za kusamvera Mulungu.

5. Undiitane Ine, ndipo Ine ndidzakuyankha iwe, ndipo ndidzakusonyeza iwe zazikuru, ndi zolakika, zimene suzidziwa (Yeremiya 33:3).

   Koma Yehova anati kwa ine, Usati, ndine mwana pakuti udzanka kwa yense amene ndidzakutumako iwe, nudzanena conse cimene ndidzakuuza. Usaope nkhope zao; cifukwa Ine ndiri ndi iwe kuti ndikulanditse iwe, ati Yehova (Yeremiya 1:7-8).

**CHAPUTALA CHA 26:**

1. Yeremiya.

2. Kubweretsa kulapa pa kubwenzeretsa moyo wa uzimu.

3. Ayuda amene anali ku ukapolo wa ku Babulo.

4. Mulungu ali wokhulupirika mu chiweruzo ndi chifundo.

5. Cifukwa cakusathedwa ife ndico cifundo ca Yehova, pakuti cisoni cace sicileka; Cioneka catsopano m'mawa ndi m'mawa; mukhulupirika ndithu (Maliro 3:22-23).

**CHAPUTALA CHA 27:**

1. Ezekieli.

2. Ezekieli amachenjeza za ukapolo uli mkudza, ndipo ananenera kwa otengedwa ku ukapolo zitzchitika.

3. Yuda.

4. Mulungu amalamulira zochitika kuti mitundu yonse ya dziko imudziwe Iye.

5. Ndipo ndinafunafuna munthu pakati pao wakumanganso linga, ndi kuimira dziko popasukira pamaso panga, kuti ndisalionongе; koma ndinapeza palibe (Ezekieli 22:30).

**CHAPUTALA CHA 28:**

1. Danieli.

2. Kuonetsa mmene Mulungu amalamulira zochita za anthu.

3. Ayuda a ku ukapolo.

4. Mulungu ndi olamulira ndipo achitira ulemu iwo amene amchitira ulemu.

5. Ndipo aphunzitsi adzawala ngati kunyezimira kwa thambo; ndi iwo otembenuza ambiri atsate cilungamo ngati nyenyezi ku nthawi za nthawi (Danieli 13:3).

**CHAPUTALA CHA 29:**

1. Hoseya.

2. Kuchenjeza Israyeli chifukwa cha machimo awo ndi kuwafunsa kuti abwerere kwa Mulungu.

3. Ufumu wa Israyeli wa kumpoto.

4. Zimene amakumana nazo munthu zimabweretsa kuzindikira ndi chifundo.

5. Imvani mau a Yehova, inu ana a Israyeli; pakuti Yehova ali ndi mlandu ndi okhala m'dziko, popeza palibe coonadi, kapena cifundo, kapena kudziwa Mulungu m'dziko (Hosea 4:1).

**CHAPUTALA CHA 30:**

1. Yoweli.

2. Kuchenjeza Ayuda pa uchimo wawo ndi kuwafunsa kuti alape ndi kuwadziwitsa za dongosolo la Mulungu pa dziko lawo.

3. Yuda.

4. Ngakhal pakati pa kuweruza, Mulungu amakhala ndi tsogolo ndi anthu ake.

5. Ndipo kudzacitika m'tsogolo mwace, ndidzatsanulira mzimu wanga pa anthu onse, ndi ana anu amuna ndi akazi adzanenera, akulu akulu anu adzalota maloto, anyamata anu adzaona masomphenya; ndi pa akapolo ndi adzakazi omwe ndidzatsanulira mzimu wanga masiku awo (Yoweli 2:28-29).

**CHAPUTALA CHA 31:**

1. Amosi.

2. Kuchenjeza za chilango cha Mulungu pa tchimo.

3. Israyeli.

4. Pempho ku maiko onse lero ndi lakuti, “konzekani kukumana ndi Mulungu.”

5. Cifukwa cace ndidzatero nawe, Israyeli; popeza ndidzakucitira ici, dzikonzeretu kukomana ndi Mulungu wako, Israyeli (Amosi 4:12).

**CHAPUTALA CHA 32:**

1. Obadiya.

2. Kuchenjeza za chilango cha Mulungu pa tchimo.

3. Edomu.

4. Mulungu amatsitsa pansi chozikwenza chilichonse patchimo.

5. Cinkana ukwera pamwamba peni peni ngati ciombankhanga, cinkana cisanja cako cisanjika pakati pa nyenyezi, ndidzakutsitsa kumeneko, ati Yehova (Obadiya 1:4).

**CHAPUTALA CHA 33:**

1. Yona

2. Cholinga sichinali kulalukira Ninevi koma kuphunzitsa Israyeli kuti chipulumutso sichinali cha Ayuda okha.

3. Ninevi.

4. Chipulumutso sichikhala ndi malire a mtundu, chikhalidwe, ndi zotchinga zina. Onani Aroma 10:13.

5. Ndipo mau a Yehova anadza kwa Yona nthawi yaciwiri, ndi kuti, Nyamuka, pita ku Nineve mudzi waukuru uja, nuulalikire uthenga umene ndikuuza (Yona 3:1-2).

**CHAPUTALA CHA 34:**

1. Mika.

2. Kuwapempha kuti alape kuti asaweruzidwe.

3. Israyeli ndi Yuda.

4. Mulungu amaweruza iwo amene amazunza anthu ake.

5. Iye anakuuza, munthuwe, comwe ciri cokoma; ndipo Yehova afunanji nawe koma kuti ucite colungama, ndi kukonda cifundo ndi kuyenda modzicepetsa ndi Mulungu wako (Mika 6:8).

**CHAPUTALA CHA 35:**

1. Nahumu.

2. Kuchenjeza za chiweruzo pa Ninevi mzinda wa mfumu ya Asuri umene anthu a Mulungu anatengedwa kupita ku ukapolo.

3. Ninevi.

4. Samalani, Mulungu amabwenzera choipa.

5. Yehova ndiye Mulungu wansanje, nabwezera cilango; Yehova ndiye wobwezera cilango, ndi waukali ndithu; Yehova ndiye wobwezera cilango oyambana naye, nasungira mkwiyo pa adani ace (Nahumu 1:2).

**CHAPUTALA CHA 36:**

1. Habakuku.

2. Kuwadzutsa Ayuda moyo wawo wa uzimu ndi kuwachenjeza za chiweruzo cha patsogolo cha Mulungu.

3. Yuda.

4. Olungama adzakhala ndi moyo ndi chikhulupiriro.

5. Yehova, ndinamva mbiri yanu ndi mantha; Yehova, tsitsimutsani nchito yanu pakati pa zaka, Pakati pa zaka mudziwitse; Pa mkwiyo mukumbukile cifundo (Habakuku 3:2).

**CHAPUTALA CHA 37:**

1. Zeafaniya.

2. Kuwachenjeza a Israyeli ndi mitindu ina za chiweruzo cha Mulungu.

3. Israyeli.

4. Mulungu ndi wamphamvu pa chipulumutso.

5. Yehova Mulungu wako ali pakati pako, wamphamvu wakupulumutsa; adzakondwera nawe ndi cimwemwe, adzakhala wopanda thamo m'cikondi cace; adzasekerera nawe ndi kuyimbirapo (Zefaniya 3:17).

**CHAPUTALA CHA 38:**

1. Hagai.

2. Kuwalimbikitsa a Israyeli kuti akhale ndi change chatsopano pa Mulungu ndi kuwapanga atsogoleri kudziwa udindo wawo omanganso kachisi wolambiramo.

3. Israyeli.

4. Kumanga ufumu wa Mulungu chikuyenera kukhala choyamba kwa wokhulupirira woona.

5. Cifukwa cace tsono, atero Yehova wa makamu: Mtima wanu usamalire njira zanu (Hagai 1:5).

**CHAPUTALA CHA 39:**

1. Zakariya.

2. Kulimbikitsa Israyeli kuti amalize kumanga kachisi.

3. Israyeli.

4. Mulungu amalamulira zochita za anthu ndi maiko onse.

5. Tsiku lomwelo padzatsegukira nyumba ya Davide ndi okhala m'Yerusalemu kasupe wa kwa ucimo ndi cidetso (Zakariya 13:1).

**CHAPUTALA CHA 40:**

1. Malaki.

2. Kuwafunsa a Israyeli alape ndi kuchita chilunganmo.

3. Israyeli.

4. Kulapa ndi kubwerera zimabweretsa kubwenzeretsa. Malingaliro ndi ntchito ndi zofunika pa chikhulululukiro.

5. Mukapanda kumvera, mukapanda kuliika mumtima mwanu, kupatsa dzina langa ulemerero, ati Yehova wa makamu, ndidzakutumizirani temberero, ndi kutemberera madalitso anu; inde, ndawatemberera kale cifukwa simuliika mumtima (Malaki 2:2).